

**CHAUZIMU
MWA
CHILENGEDWE.**

Buku Lolembedwa ndi:

**MARK PAMODZI
NDI PATTIE VIRKLER**

Losindikizidwa mu chaka cha 1990 ndi Mark Virkler.

ISBN 1-56043-0605

Buku ili lili lotetezedwa ndi bungwe loona za kusabelana kwa luso la ku Amerika. Buku ili silili loyenera kukoperedwa popanda chilolezo. Kulemba ndime zina kuti mugwiritse ntchito pa kusanthula malembo opatulika kuli kovomerezeka. Malembo opatulika onse achokera mu baibulo lotchedwa “New King James” losindikizidwa mu chaka cha 1984 ndi bungwe lotchedwa “Thomas Nelson Publisher’s malembo onse opatulika alembedwa posindika fundo zolembedwa mu bukuli.

Losindikizidwa ndi a
Destiny Image Publisher
P.O. Box 310
Shippensburg, P.A.
17257.

“ Kulankhula zolinga za Mulungu ku m'bado uno”

Logawidwa:

Ku dziko lonse lapansi.

Losindikizidwa ku Amerika.

Ku Amerika, mukhoza kuchita telefoni kuti muitanitse bukuli pogwiritsa ntchito nambala iyi.

1-800-722-6774.

Buku ili ndi zotsatira za kugwirira ntchito pamodzi kwa akonzi awiri awa. Fundo zonse izi ndi mavumbulutso onse a kusanthula kwao malembo opatulika ndi zokhudza onse awiri pa moyo wao. Mau oti “ Ine akugwiritsidwa ntchito kuimilira umodzi wa anthu awiri awa pa maganizo awo. Buku ili ndi kutambasula kwa zolembedwa zopezeka mu buku lotchedwa “ Kukhala mwa Khristu lolembedwa ndi akonzi onse awiri awa.

ZAMKATIMU

MALONJE CHAUZIMU MWA CHILENGEDWE!

Moni okonedwa. Lero tiyamba ulendo kumene uthere mkovuta kunena chifukwa choti panopa nditangokamba pang'ono za mbiri ya moyo wanga. Ndiliba mutu weniweni wa ichi. Izi zili choncho chifukwa choti moyo wanga wakhala wopanda tchutchuchu wa zochitikazo ndipo pa chifukwa cha ichi mutu wake weniweni ndi wovuta kupereka. Ndimangokhala basi. Sindikudziwa ngati nkololeka kufotokoza nkhani yonse kapena kungokamba fundo chabe. Apa sindikudziwa. Nchifukwa chiyani sitikuyesa chabe ndi kupeza zenizeni zake?

Sindifotokoza mbiri yonse ya moyo wanga mu buku ili. M'malo mwake ndikungofuna kukuuzani za phata limodzi mwa maphunziro omwe ndaphunzira pa zaka makumi awiri ndi mphambu zitatu (23) monga mkhristu wokhala moyo wosandulika osati wa ine ndekha. Ndidakhala moyo ngati mkhristu pa zaka khumi ndi mphambu ziwiri (12) ndisadzindikire choonadi ichi. Pa nthawi imeneyo ndidali "Ine" kukhala ndi moyo. Apa musasokonezeke nkumaganiza kuti sindidali mkhristu koma kuti ndidali wa chipembedzo. Ayi, ndidapereka moyo wanga kwa Yesu ndili ndi zaka khumi ndi mphambu zisanu (15). Ndidapempha Ambuye kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wanga komanso kundiyeretsa ndi mwazi wake. Ndidali kuyesetsa kukhala moyo wa chikhristu komanso kumusangalatsa iye.

Mwa chitsanzo, malembo opatulika adali kundiuza kukonda adani anga, mwa ichi ndidayetsa kwambiri (ndi thandizo la Ambuye) kuchita motero sindidaonetsere kuti ndidali kuchita bwino poyesera kupemphera monga ndimadziwira. Sizidali kupereka kusiyana kwina kulikonse kuti ndi lamulo liti mu baibulo lomwe ndimamvera, koma kuti ndidali kuona kulephera kokhakokha sindidali kuona kuti chikhristu ndi chinthu cha uzimu chapadera. Ndidayesetsa kupempha chithandizo kwa Mulungu. Apa sindidali kutanthauza kuti ndidali kukonda adani anga koma kuti ndidali kuyesetsa.

Kenako vumbulutso lidayamba kubwera mu mtima mwanga. Ndidapeza kuti "Ine" adayamba kufa mwa ine. Ndidapachikidwa ndi Khristu ndipo Khristu adakhala wa moyo mwa ine! Zimaoneka zovuta kuvomereza chifukwa

pamene ndidali kuyang'anira pa kalilore, chithunzi chomwe ndidali kupenya chimaoneka ngati ine! Padatenga chaka kuti vumbulutso litakasike mu mtima mwanga kuti ndidali chotengera chabe chomwe chimasunga wina wake ndidali chotengera cha moyo wa Khristu Yesu komanso kuti ndidali nthambi ya mtengo wa mpesa. Apa mutha kuona kuti ndidakula moyo woganizira kuti "Ine" ndidali ndi moyo mwa ine ndekha koma awo adali maganizo chabe. Zoonza zake, zidali zoti satana – mzimu wa dziko lino lapansi adali ndi ulamuliro pa ine pa nthawiyo. Koma popeza ndidalibe chidziwitso chokwanira kuti ndikathe kuona ichi, ndidakula ndi moyo wokhulupilira zotero kuti "Ineyo" adali kulamulira. Tsopano popeza ndidali mkhristu, ndidalibe kumaganizira kuti "Ine" ali ndi moyo komabe Khristu Yesu ali pambali panga kundithandiza pa moyo umene ndimakhala.

Komabe awa adali malingaliro chabe chifukwa choti Khristu sadali kungokhala nawe pambali kundithandiza koma adayenera kukhala *MOYO WANGA*. "Ine" adayenera kuferatu. Ndidayenera kutayikiratu mwa iye. Apa ndidali kumangolankhula izi ndi izo. Zidali kuoneka ngati kulankhula kwa chipembedzo pembedzo komabe kudali ndi tanthauzo lochepa kwa ine—makamaka ku moyo wanga. Ndidapenyereza pa kalilole. Ndidaona iye amene adali pamene. Ndidali "Ine" Mariko W. Virkler sadali yesu, mwa ichi awa adangokhala chabe maganizo a chipembedzopembedzo. Sadali vumbulutso loyaka mu mtima mwanga kusanduza moyo wanga. Sizidali zinthu zochitika pa moyo wa uzimu. Adali chabe maganizo a chithupithupi osiyana ndi mayendedwe a moyo wa Chikhristu ku m'bado uno.

Kenako Mulungu adapsyereza izi. Iye adaonetsera chiwalitsiro chake pa hitsokonezo icho ndipo kenako adasanduliza moyo wanga. Ndidakhala tsopano wamphamvu za uzimu zoposa zangazanga ndipo tsopano ndidayamba kukhala mwa mzimu. Ndidalibenso malire pa moyo wanga koma kuti ndidayamba kuona mphamvu za Mulungu zopanda malire zikuyenda mu moyo wanga. Ndidakhala tsopano moyo wauzimu koma mwa chilengedwe! Chikhristu tsopano chidayamba mwa ine. Chidali tsopano chenicheni osati monga poyamba paja. Pamene ndidawerenganso chipangano chatsopano lidakhala buku latsopano kwa ine. Ndidali kulipenya ndi maso otseguka kwa nthawi yoyamba ndipo ndimalephera kukhulupilira zimene ndidali kuwerenga.

Buku ili likufotokoza nkhani yonse umo vumbulutso lidabwerera mu moyo wanga. Ndi nkhani ua munthu amene amaganiza kuti adali ndi moyo komanso umo Mulungu adamuonetsera iye kuti wapachikidwa ndi Khristu ndipo tsopano Khristu akhala wa moyo mwa iye ndi nkhani yopyola mawu a chipembedzo ndi kupeza choonadi chenicheni mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Ndi nkhani ya moyo wosandulika. Ndi nkhani ya umo ungayambire kukhala mwachilengedwe wauzimu. Ndi umboni ku fundo yoti ife monga mpingo wa Yesu Khristu talumikizidwa ku ulemelero wa Mulungu. Ndi pemphero langa kuti iwenso usandulike pamene ukuwerenga bukuli.

UMO UNGAGWIRITSIRE NTCHITO BUKULI.

Buku ili lilinso ndi malingaliro pamodzi ndi mafunso okambilana pa gulu kumapeto kwa chaputala chilichonse. Ndikuona kuti ngati nkotheke, usanthule buku ili pa gulu la anthu amene amakomana pa sabata iliyonse ndipo mugwiritse ntchito chaputala chimodzi kapena ziwiri. Magulu a anthu awa akhoza kukhala a Sande sukulu mafeloshipe, misonkhano ya azimayi, ku sukulu za mau a Mulungu. Komanso m'busa akhoza kutenga mauthenga mu buku ili ndi kulalikira tsiku la Mulungu. Mpofunikanso kusanthula ma chaputala oti awerengedwe mkati mwa sabata ndipo pa nthawi yotero mukhozanso kukambilana za choonadi chimene mwaphunzira kukhuzana ndi miyoyo yanu ya uzimu. Mafunso akhalepo pa nthawi yotere muyeneranso kuligwiritsa ntchito pamene mukusanthula malembo opatulika nkoyeneranso kulembera zonse wapeza mu kope lako lapadera.

Ndipempheso kuti mtsogoleri aliyense pa gululo ayenera kubwerezanso fundo zonse zomwe zili mu chaputala chilichonse. Akhozanso kulankhula mosindika za fundo imene iye akuona kuti ili yoyenera kuti anthu amvetse bwino. Akhoza kugawana ndi anthu za vumbulutsolo. Kenako mukhoza kukambilana mafunso monga mwa gulu.

Ndikupemphera kuti maphunziro otere atsitsimutse onse pamene mukudzama mu kuyenda ndi Mulungu. Madalitso akhale nanu pamene mukuyenda ulendo wa uzimu wotere.

CHAPUTALA CHOYAMBA.

“MUNTHU WOSAKA INE”

Nagona pa kama langa koma kulephera kupeza tulo. Ndimalingalira motere, kodi chingachitike nchiyani ngati ndingafe usiku uno? Kodi ndikhoza kupita kumwamba? Ayi, ndidadzindikira kuti sindingakhoze kupita. Ndikhala mu mpingo wanga pa nthawi yaitali ndipo ndidadzindikira kuti iwo okha amene angamulandire Yesu monga mpulumutsi wao ndi amene angapite kumwamba. Ichi ine sindinachite ayi, ndimafunabe kuchita “njira yanga” kusiya zonse kutsatira “kutsatira njira yake” kumaoneka monga chinthu chovuta kwambiri kuti ndichipemphe. Mwa ichi chaka ndi chaka ndidali kukana komabe ndimadzindikira kuti ngati ndingamwalire ndidzapita ku gehena.

USIKU UMENE MULUNGU ADANDIPEZA

Koma usiku uwo udali wanga. Mulungu adandisankhula polankhula kwa angelo ake motere, “pitani mukamutenge mnyamatayo ndikumufuna kwambiri” Ine ndidali kulephera kuti ndipeze tulo. Ganizo lina lidafika kwa ine motere.....” Kodi nanga kutakhala kuti nyumbayi yapsya usiku uno? Apa ndiye kuti ndipita ku gehena” Apa ndimalephera ngakhale kutinkhatinkha ndikudziwa kuti izi zidali chomwecho chifukwa choti mngelo adali kunong’oneza mu khutu langa.

Pomaliza pa zonse, patadutsa maora angapo ndidadzuka makolo anga adali ku msonkhano wa mpingo mwa ichi ndidakhala mu chipinda kuti ndiwafotokozere zonse makolowo akafika. Ndidali kuti ndipereke mtima wanga kwa Khristu Yesu.

Ndidali ndi zaka khumi ndi zisanu (15) pamene ndidabatizidwa ndi kulowa mpingo wanga kulapa kwanga kudali kwenikweni, kudzipereka kwanga kwa Ambuye kudali kwa mntheradi. Yesu adatenga ulamuliro wonse wa moyo wanga ndipo adali Mbuye wa moyo wanga. Ndidali ndi maganizo a za kumwamba basi. Yipeeee! Ndidaona kumasuka kwa mzimu wanga.

Ndidaona mtendere ukuyenda mu moyo wanga. Ndidamzindikira kuti ndabadwanso mwatsopano. Ndidali mwana wa Mulungu.

KUFUNAFUNA KUKULA MU UZIMU PAMODZI NDI CHIYERETSO.

Ndidali ndi chikhumbokhumbo chofuna kudzidzamisa ndekha mu mau a Mulungu ndipo ichi chidachita patadutsa chaka chimodzi, ndidaganiza kupereka moyo wanga ku utumiki wa nthawi zonse osagwira ntchito yina iliyonse. Pamene ndimafika zaka khumi ndi mphambu zisanu ndi zitatu (18) ndidapita ku koleji ya Robert Wesleyan pafupi ndi Rochester, New York kumene ndidakhala pa zaka zinayi kuphunzira za mau a Mulungu komanso za utumiki wa Ubusa. Ndidafuna kupereka kwa Mulungu moyo wanga. Ndidagwira ntchito monga m'busa wa achinyamata pa zaka zitatu ndipo kenako nditatha kudzodzedwa ndidzakhala m'busa weniweni wa mpingo wangawanga. Moyo udayamba tsopano kuphuka. Ndidali kulalikira lamulungu lililonse kulandira vumbulutso kuchokera mu mawu a Mulungu la umo ungasangalatse pamodzi ndi kutumikira Mulungu. Sabata, ndidali kugawana izi ndi mpingo wanga kuwaphunzitsa umo angakhalire a mphamvu kwa Mulungu. Tidasanthula za chiyero, pamodzi ndi chilungamo kuchitira umboni pamodzi ndi pemphero komanso kufunikira kokonda adani athu. Ndidaphunzitsa za chachikhumi chopereka, chachifundo komanso umo munthu anga khale wolemela pa chuma tidakonza gulu la anthu ochitira umboni mawu a Mulungu khomo ndi khomo. Tidakonzanso dongosolo la mapemphero ammawa komanso osala chakudya. Ndidaphunzitsa za kufunika kokhala munthu woyera mtima, komanso fundo zofunika pa kukhala munthu wofatsa koma kufunika kochita zinthu zokhazo zofunikira kwambiri pamaso pa Mulungu. Tidaphunziranso zotaya zilankhulo zoipa pogwiritsa ntchito lilime lathu, kukhala ofanana ndi Yesu, kugwetsa malinga onse a satana ndidaphunzitsa zinthu zambiri zokhudzana kukhala moyo wa chikhristu kunyumba komanso ungakhazikitsire zizolowezi za chakudya. Ndidaphunzitsa za munthu wokhulupilira molingana ndi lamulo, komanso umo angachilitsire kupsyinjika kugonjetsa kusilira pamodzi ndi chigololo. Zambiri zidaphunzitsidwa zopyola apa.

GORI LIDASANDUKA LOLEMERA.

Kenako chinthu china cha chilendo chidachitika. Mmodzi wa madikoni

anga adakhala nane tsiku lina lake pa nthawi imene ndimasanthula mau a Mulungu ndipo adalankhula motere “ Mariko, sindikufunanso kumva ulaliki wina uliwonse. Sindingachite zonse zimene tsopano ndikuzizindikira pano pakuti ndizichita ndipo ngati ndingamve uthenga wina woonjezera apa, ndidzangoona kuti ndili wolakwabe kukhudzana ndi njira zanga zonse za miyambo zomwe ndikulephera kusangalatsa nazo Mulungu. “ Ndidamvetsa vuto lake. Iinso ndidali kuliona ndekha pa moyo wanga. Zimaoneka kuti ngakhale ndidali kudzipereka kwambiri kwa Mulungu mwa mtundu wanji, ndima pezekabe wolephera komanso wotsutsika. Sindikadasiya kulalikira chifukwa choti moyo wanga udali kulephera kusunga malamulo a Mulungu omwe ndidawapeza mu malembo opatulika.

Ayi, ndiyenera kulalikira- koma kenakake kadayenera kusinthika Gori idakhala lolemera padali zinthu zambiri zoti ndichite ngati ndimafuna kukhala mkhristu wabwino. Kudali kosatheka kumakumbukira malamulo onse. Ndipo pamene ndimapeza limodzi lomwe ndidaiwala, ndimazona wolephera pamodzi ndi wotsutsika. Yesu adalankhula kuti gori lake lili lopepuka koma kwa ine silidaoneke lotero! Ndidakumbukira kuti pamene ndidangotembenuka mtima ndidali kuona kuti lidali lopepuka- koma pamene ndidayamba kusanthula zimene Mulungu amayembekezera kwa ine, zinthu zidayamba kulemera mwa changu. Nchachidziwikire, Yesu sadamvetsetse kuti pamene ukukhala moyo wa mthupi, kumakhala kolemera kumusangalatsa Iye. Kapena kodi, ndidali kutsokoneza chikhristu mu njira yina yake kupanga zimene zimaoneka kukhala zopweka ndi zopepuka kuti zikhale zolemera ndi zovuta? Apa ndinadabwa kwambiri.

MUNTHU WOSAUKA

Sikuti chikhristu chidangokhala cholemera ndi chovuta kwa ine chifukwa choti padali zinthu zambiri zoti ndikumbukire kuzichita komanso ndidapeza kuti pamene ndidayesera kuchita zinthu zambiri Mulungu amafuna kuti ndichite, thupi langa lidali kukana motere “ Tsatirani za ine poyamba” ndipo zotsatira zake idali nkhondo yauzimu yokhayokha.

Mwa chitsanzo, zokonda adani anga. Munthu wina amandiukira ine mu njira yina (osamvetsa ukulu wanga, chikondi kudzipereka pamodzi ndi chiyero ndipo amabwera ndi miseche pamodzi ndi mabodza. Thupi langa limapsya mtima ndi kulankula motere, “ Chabwino, bamboo Ngwiwo

ukuganiza kuti uli woyaka kwambiri ndilole kuti ndikuuze chinthu chimodzi kapena ziwiri” kenako nkondo imayamba. Podzikumbutsa ndekha kuti lamulo la Mulungu likukamba kuti ndidayenera kukonda adani anga, ndimakhoza kuonetsa nkhope ya msangalo ndi kutonthoza chifuniro changa polankhula motere, “Udzakonda thupi losauka ili ngakhale kuti litakupha” Chabwino, lidandipha thupi langa limachita nkondo koma popeza Mulungu adandipatsa chisomo pamodzi ndi chifuniro champhamvu, pomaliza pake zonse zidagonjetsedwa ndipo ndimatha kulankhula mau abwino a chikondi. Apa sizikutanthauza kuti mkati mwanga mudali kukonda kotere. Ine ndidatsutsana ndi nkondo yonse ya mthupi mwanga polankhula motere, “udzafa ku mkwiyo wonse ukuumva” zotsatira zake, mkwiyo udaferatu mwa ine ndipo kunja kwa maonekedwe a nkhope yanga kudali chimwemwe chokhachokha pamodzi ndi mau a chikondi oturuka pakamwa panga komanso ntchito zabwino za chikondi. Izi sizidaoneke monga umo chikhristu chidayenera kukhalira! Ndikakumbukira, ndikuona kuti ndidayenera kuona chikondi ndi chimwemwe, mtendere pamodzi ndi chipiliro mkati mwa moyo wanga mmalo mwa mkwiyo ndi ntchito za imfa.

KUKOMANA NKHOPE NDI NKHOPE NDI CHIFUNIRO CHOLAMBIRA

Kenako mkazi wanga adatsokoneza zinthu kopyola. Patti adalankhula kwa ine tsiku lina motere, “Chikhristu chimagwira ntchito kwa okhawa amene ali ndi chifuniro champhamvu. Sichigwira ntchito kwa anthu okhala ndi chifuniro chofooka....” Mukuona chifuniro cha patti chimaoneka chofooka pofanizira ndi changa ndipo adali wodzala ndi chikaikiro kapena kupsyinjika mmalo modzigwiritsa izi mkati mwake ndi kudzigonjetsa monga ine ndimachitira kulankhula kwake kudandipweteka ine. Ndimadzindikira kuti chikhristu chiyenera kugwira ntchito kwa anthu onse a chifuniro chofooka pamodzi ndi a chifuniro cholimba omwe.

KUYAMBA KUSOKONEZEKA.

Tsopano ndinatsokonezeka chomwe chili chofunikira kwambiri chifukwa ndaphunzira kuti chisokonezo ndi gawo loyamba lopita ku vumbulutso. Kodi kufikira kwanga ku chikhristu sikudali koyenera? Kodi kudali ndi mabanja? Sindikuyembekeza kuti kudali chotero chifukwa choti padanditengera zaka khumi monga khristu kukhazikitsa njira iyi. Zotsatira zanga pa moyo wanga

pa nthawi iyi zidali zofanana ndi kulira kwa Paulo pa aroma chaputala cha chisanu ndi chiwiri.

..... “ Pakuti chimene ndichita sindichidziwa pakuti sindichita chimene ndifuna koma chimene ndidana ndichita ichi.... koma ngati ndichita chimene sindichifuna sindinenso amene ndichita koma uchimo wakukhalabe mkati mwanga ndiwo. Ndipo chotero ndipeza lamulo ili kuti pamene ndifuna chabwino, choipa chiliko. Pakuti monga mwa munthu wa mkati mwanga ine ndikondwera ndi chilamulo cha Mulungu koma ndiona lamulo lina m’ziwalo zanga liri kulimbana ndi lamulo la mtima wanga ndi kundigonjetsa kapolo wa lamulo la m’ziwalo zanga. Munthu wosauka ine adzandilanditsa ndani mthupi ili (**Aroma 7:15, 20-24**).

Apa ndipo ndidafika monga “ Munthu wosauka” Ndidli pa nkondo mwa ine ndekha. Ndimayesera kukhala wabwino. Ndimayesera kuchita chabwino ndimaona nkondo ya mkati mwanga kapena imfa mkati mwanga yotsakanikirana ndi kusowa kwa chikondi, chimwemwe, mtendere. Ndimadzindikira kuti payenera kukhala chikhristu chenicheni kuposa apa. Kodi uwu ndi moyo wochuluka wa Mulungu umene amakamba – munthu kumalimbana kuchita nkondo mwa iye yekha? Ngati zili chomwecho, apa ndiye nkovuta kutsatira. Ndimazona ndekha ngati ndikulankhula kwa munthu yemwe Sali mkhristu motere, “ ukhoza kulandira Yesu ngati mpulumutsi wako ndi kukhala ngati ine munthu wodzala ndi nkondo mkati mwanga” Iye akadakhocha kuyankha motere, “ Sindithokoza konse, ndili ndi mavuto okwanira a ine ndekha” Mwa ichi ndidaima kaye osachitira umboni chifukwa choti zomwe ndidali kuziona pa moyo wanga zidali zovuta kugawana ndi anthu ena. Ndipo ndinati, “ Mulungu, chonde ndiphunzitseni chimene mukuona kuti ndikuchita molakwika....”

MDERA MDERA WAVUMBULUTSO LA CHIMENE CHIDACHITIKA PA UBATIZO.

Mulungu adayamba kubweretsa mabuku oyenerera, aphunzitsi, komanso zinthu zina zochitika mu moyo wanga- ndipo pa miyezi yotsatirayo ndidaphunzitsidwa choonadi chisanu ndi chiwiri zomwe zandimasula ku kulakwa, kutsutsika , nkondo, zowawa za mkati mwa moyo pamodzi ndi chilamulo. Izi ndi zinthu zake ndidaphunzira.

Choonadi	#	1-	Mulungu ali zonse mu zonse
Choonadi	#	2-	Ndine chotengera
Choonadi	#	3-	Sindilinso ndi moyo
Choonadi	#	4 -	Khristu ndi moyo wanga
Choonadi	#	5 -	Ndafa ku chilamulo
Choonadi	#	6-	Ndili ndi moyo mwa mzimu (rhema ndi masomphenya)
Choonadi	#	7-	Ndili ndi moyo mwa chikhulupiliro kuti Mulungu ali Emmanueli.

Mu machaputala asanu ndi awiri otsatirawa, tidzakhala tikusanthula zimene Mulungu adandiphunzitsa za choonadi chilichonse pachokha chomwe chidamasula mphamvu ya Mulungu kupyolera mu kulumikizana kwa mzimu wanga.

KUONANSO MAFUNGULO ENIENI KUCHOKERA PA CHAPUTALA CHOYAMBA.

- Zinthu zochitika pa chipulumutso chathu zimabweretsa mtendere, chimwemwe pamodzi ndi kumasuka.
- Nthawi zonse munthu amayamba kusanthula malembo opatulika ndi kuona malamulo a Mulungu ku moyo wake, kuonanso kulemera komwe kumabwerera pamene munthu waona kuvuta kumvera malamulo onse omwe akuwapeza.
- Ntahwi zonse pamakhala nkhondo ya mkati mwa moyo pamene munthu akuona mu thupi lake nkhondo yomenyana ndi mzimu mu kuyesetsa kwake kuti akhale woyera.
- Zotsatira zake ndi zimene Mulungu adazitcha “Munthu wosauka”
- Uonjezere maganizo ako ena amene adali mafungulo kwa iwe. Izi ulebere padera.

GANIZANI NDIPO KAMBIRANANI.

- Kumbukira zomwe zidachitika pa chipulumutso chako. Ukhale ndi mphindi zochepe kugawana izi ndi anmzako pa gulu. Ngati wina pakati panu sadalandirepo chipulumutso ngati angafune kuti aka akomane ndi yesu monga monga mpulumutsi wake. Ngati

- ndi choncho, mtsogolere kuchipulumutso
- Kodi udaonapo nkhondo yauzimu yomwe yafotokozeredwa pa aroma chaputalacha chisanu ndi chiwiri? Ngati ndichomwecho gawana ndi amnzako umboni.
 - Kodi udayamba wa pempherapo mwa mphamvu zako kuti ukwanilitse zinthu? Kambilanani pa gulu. Ngati sitiyenera kukhazikitsa chifuniro chathu kutsutsana ndi tchimo, Kodi tsopano tikhoza kugwiritsa ntchito chifuniro chathu mu njira yotani.
 - Kodi ukutha kuona kutsutsika kapena kodi kuti wafika pa kutsutsika kumene alemba pa aroma 8:1? Ngati ndi chomwecho, kodi nchiyani chimachititsa? Kodi chingagonjetsedwe bwanji? Kodipokhala moyo wangwiro? Kodi nanga njira zake ndi ziti?
 - Kodi wapeza njira imene “Munthu wosauka ine” yemwe Paulo akulankhula pa Aroma 7 kapena kuti wakoledwa mu vuto? Ngati wapeza njirayo, fotokoza njirayo pa gulu lako.

KULEMBERA – Ulembere kufuna ili padera: “Ambuye kodi mu kufuna kulakhula chiyani kwa ine kukhuzana ndi choonadi ichi cha pa Aroma 7? Ngati siukutha kudzikira bwino za kulemba kotere, Werengani buku lotchedwa “**CHIYANJANO NDI MULUNGU**” lolembedwa ndi Mariko Virkler kapena lotchedwa “**KULANKHULANA NDI MULUNGU**” lomwe likuphunzitsa izi mozama. Buku la “**CHIYANJANO NDI MULUNGU**” lili ndi zambiri zokhudza anthu ogwiritsa ntchito mbali ya manja ya bongo. Kulemba kutanthauza kulemba mapemphero pamodzi ndi mayankho a Mulungu monga Davide adachitira ndi Masalimo. Lembera zimene Mulungu akulankhula kwa iwe mu njira ya kulemba mu buku lapadera. Ngati sizili za iwe wekha, ukhoza kuziwerenga pa gulu. Izi zikhoza kulimbikitsa pamodzi ndi kumangirira kwa onse akumvera komanso kwa iwe kuti ndi Mulungu akulankhula kwa iwe. Onetsesa kuyamba kulemba kulikonse ndi funso. Izi ndi zothandiza kwambiri. Onani kumapeto kwa bukuli kuti mukathe kuona mafungulo anayi a kumvetsera kulankhula kwa Mulungu.

CHAPUTALA CHACHIWIRI CHOONADI # 1
MULUNGU ALIYENSE MU ZONSE.

Inde, pali zambiri ku Chikristu koposa “Munthu wosauka”

wofotokozedwa ndi Paulo pa Aroma 7. Paulo mwini akufotokoza za ichi pa Aroma 8. Tiyesetse kulondola mapazi ake mu machaputala otsatirawo.

KODI MULUNGU TIMAMUONA BWANJI?

Vumbulutso loyambirira lomwe liyenera kuyaka mu mitima yathu ndi la chimene Mulungu ali. Kodi iye ali ngati chinthu chachikuru cha padera chokhala mlengalenga? Kodi ali munthu wopezeka paliponse? Kapena kodi ali wokhuzidwa ndi zinthu zochitika mu moyo wathu? Kodi Iye amakhuzidwa ndi zinthu zochitika pa dziko lapansi?

Mu kusokonezeka kwanga ndidali kuganiza kuti Mulungu ali wonga iye amene adali ndi mphamvu pamodzi ndi ulamuliro, chikondi pamodzi ndi mtendere. Ndimamuona iye monga wokhala ndi zionetsero za chikhalidwe chake zambiri zomwe ndimazisowa. Ndimakonda kumufunsa pa zinthu zotere motere, “ Mulungu chonde, mungandipatseko.....” ndimaona Mulungu monga ngati wokhala patali ndipo ndimamufunafuna pamodzi ndi kumuyitana kuti akomane nane. Ndimamaona nthawi zonse wolekana naye. Iye adali ngati uko ndipo ine ndidali ngati kuno. Ndinali wosayera. Ndimasowa kulimbikitsidwa ndi iye.

CHIKHRISTU CHA MTHUPI NDIDAKHALA NACHO.

Nthawi zambiri ndimakhoza kumuyiwala osamufunafuna. Ndimakhoza kugwiritsa ntchito mphamvu zanga kuti ndikwaniritse zimene ndimafuna kuchita ndidaganiza, “ Nchifukwa chiyani ndikumuvuta Mulungu ndi zinthu zoterezi? Ngakhale kuti ndidafunafuna pamodzi ndi kukumbukira kumufunsa ite, nthawi zina sindidali kutero chifukwa choti adali ndi zinthu zofunikira kwambiri kuchita koposa zochepa zotere. Kupatula apa, iye wandipatsa mphamvu za thupi kuchita izi mwa ine ndekha. Tsono ndimangopitilira patsogolo ndi kukhala ndi moyo. Mulungu adayamba kupasula zoterezi ndi kundipatsa vumbulutso lake mu niira zimene sindidazionepo ndi kale lonse.

ALI WA MULUNGU WAMPHAMVU ZONSE

Vumbulutso loyambilira lomwe adandionetsera ndi lakuti iye ali Mulungu wamphamvu zonse. Ichi ndi chimene ndidalankhula pa zaka zambiri. Kodi

zikutanthauza chiyani ponena kuti Mulungu ali wamphamvu yonse? Kodi ndi mphamvu zambiri bwanji zoperekedwa kwa iye? Ndi zambiri bwanji zimene zatsalira kwa ine, kwa satana, kwa ena? Ukuganizira chabe! Ndinaganiza kuti pokhala wamphamvu yonse zitanthauza kuti ali ndi mphamvu zonse za kumwamba. Apa zikutanthauza kuti ngati pali mphamvu yina yake, iyenera kukhala chionetsero cha Mulungu amene ali ndi mphamvu zonse. Apa sikuti Mulungu ali woyambitsa wa choipa.

Ilo ndi vuto lapadera lomwe tikambe posachedwa. Ayi, zimene ndikutanthauza ndi zoti mpehya uliwonse umene ngakhale anthu a chikunja amapuma amene amatemberela Mulungu, umaperekedwa kwa iwo ndi Mulungu. Ngati Mulungu angachotse mphamvu yake, munthuyo akhoza kufa. Mulungu aliyense mu zonse.

Ngati unganene kuti uli ndi mphamvu zonse apa ndiye kuti uli wabodza. Chinthu chimodzi ndi kudzikira ndi choti Mulungu Sali wabodza. Mwa ichi ngati akutero kuti ali ndi mphamvu zonse za kumwamba ndi dziko lapansi apa ndimakhulupilira. Koma kodi Mulungu anatero kuti adali ndi mphamvu zonse? Bwererani ndipo werengani pa Genesis 17:1.

..... “Pamene Abrahamu anali wa zaka makumi asanu ndi anayi, kudza zisanu ndi zinayi, Yehova anamuonekera Abrahamu nati kwa iye, “ Ine ndine Mulungu wamphamvu yonse, yenda iwe pamaso panga nukhale wangwiro.....” Kodi apa akutero kuti ali ndi mphamvu zonse? Sindikuganiza chomwecho. Kodi apa akuti bwanji? Apa akuti ali mphamvu yonse. Kodi pali kusiyana pakati pa kukhala ndi mphamvu zonse za kumwamba ndi dziko lapansi ndi kukhala wamphamvu yonse ya kumwamba ndi dziko lapansi? Ngati ndili ndi kanthu kenakake, ndikhoza kukupatsani. Koma ngati ndili kanthu kenakake ukusowa apa ndiye kuti ndiyenera kudzipereka ndekha kwa iwe.

OSATI “ALI NDI” KOMA “ALI”

Mulungu Sali ndi mphamvu zone za kumwamba ndi dziko lapansi. Iye ali “ mphamvu zonse” za kumwamba ndi dziko lapansi. Choncho ngati ndi kufotokoza za mphamvu, kodi ndikukamba za ndani? Ukhoza kuganizira apa – za Mulungu! Ngati ukuonetsera mphamvu kapena ulamuliro mu moyo wako, kodi ukuonetsera ndani? Apa ukuonetsera Mulungu wamphamvu yonse chifukwa zionetsero zonse za mphamvu ndi ulamuliro ndi za Mulungu amene

ali wamphamvu yonse. Pamene ndakweza dzanja langa la manja, ndi mphamvu ya ndani ikuonetseredwa – yanga kapena ya Mulungu? Kodi ndili ndi mphamvu yina yake mwa ine ndekha? Osati kuti ndi Mulungu ali nayo? Mwa ichi ndi mphamvu ya Mulungu kuonetseredwa.

Ngati Mulungu ali ndi mphamvu, apa ndikhoza kumupempha kuti andipatse yina mwa mphamvu yake monga ngati kanthu kenakake kapadera koma ngati Mulungu ali wamphamvu zonse ndipo ndikufuna mphamvu, apa ndiyenera kumupempha iye kuti akhale pomwepo kudzionetsera iye yekha. Ndidzalankhula motere “ *Mulungu, ndikukudzindikirani monga Emmanueli*- Mulungu ali nane. Ndikukuthokozani kuti moyo wanu pamodzi ndi mphamvu zanu zili pano ndipo zikuyendayenda. Ndikulankhula pamodzi ndi kumasula mphamvu za Mulungu wamphamvu yonse pamalo pano.....” Ukhoza kudabwa chifukwa chimene tiyenera kuyitana mphamvu yake kuti imasulidwe. Yankho ndi loti Mulungu samangoyankha zopempha zathu zilizonse (Ezeieli 22: 30,31) chifukwa choti iye amafuna kutisula, komanso kutiphunzitsa kagonjetsedwe ka adani ndikuti tilamulire monga mafumu ndi ansembe pamodzi ndi iye mu ulemelero.

Ngakhale kuti anthu ena akhala akugwiritsa ntchito mphamvu ya Mulungu kuchitira zinthu zoipa, apa sikuti sukhala mphamvu ya Mulungu? Kodi anthu otere ali atumiki ake? Iye aliyense mu zonse. Mwa chitsanzo, taganizirani za Nebukadineza- munthu woipa wa ku chipangano chakale yemwe amaononga maiko pamodzi ndi kuwayesa anthu akapolo. Kodi iye adali mtumiki wa Mulungu?

KODI NANGA ZA ANTHU AMPHAMVU OIPA?

Pa Yeremiya 25:9 Mulungu akulankhula motere..... “ Taonani ine ndidzatuma ndi kutenga mabanja onse a ku mpoto ati Yehova ndipo ndidzatuma kwa Nebukadineza mfumu ya ku Babulo, mtumiki wanga ndipo ndidzatengera iwo pa dziko lino ndi pa okhalamo ake onse ndi pa mitundu iyi yozungulira ndipo ndidzathetsa iwo ndithu ndi kuwayesa iwo chidziwitso ndi chitsonyezo” Nebukadineza – mfumu yoipa, adali mtumiki wa Mulungu kuchita kuchita chifuniro cha Mulungu.

Kodi Nebukadineza amadzindikira yekha kuti ali mtumiki wa Mulungu kuchita chifuniro cha Mulungu? Iye amaganiza kuti ali kuchita zinthu mwa

mphamvu ya iye mwini. Pa Yesaya 10: 13-14 akufotokoza motere,
“ popeza anati, mwa mphamvu ya dzanja langa ndachita icho ndi mwa
nzeru yanga pakuti ine ndiri wochenjera, ndachotsa malekezero a anthu,
ndalanda chuma chao, ndagwetsa monga munthu wolimba mtima iwo okhala
pa mipando ya chifumu, dzanja langa lapeza monga chisa, chuma cha mitundu
ya anthu ndipo monga munthu asonkhanitsa mazira osiyidwa, ine
ndasonkhanitsa dziko lonse lapansi ndipo panalibe chogwedeza phiri kapena
chotsegula pakamwa”

KODI MAGANIZO A MULUNGU ALI OTANI PA NKHANIYI

Mulungu amalankhula zoonza zake zokhazokha ndipo akufotokoza motere
pokamba za mwano wa Nebukadineza pomufunsa motere: “ Kodi nkhwangwa
idzadzikweza yokha pa iye amene adula nayo? Kodi chochokera
chidzadzikweza chokha pa iye amene ainyamula ngati ndodo inganyamule
kanthu popeza iri mtengo. Chifukwa chake Ambuye Yehova wa makamu
kuonda mwa onenepa ake.....” (Yesaya 10: 15-16)

Maganizo a Mulungu pa zoonza zake zenizeni ali osiyana ndi
Nebukadineza. Mulungu akukhulupilira kuti Nebukadineza ali monga nkono
wamanzere wa Mulungu ndipo akuona kuti sikoyenera kuti Nebukadineza
kunyada chifukwa cha mphamvu zake zomwe ali nazo pa zinthu izi. Mwa
ichi pomuthandiza Nebukadineza za kuti aone, Mulungu adatumiza kenakake.
Kusiyana kotani kwa izi ndi zoonza zake zenizeni?

Tsopano ndi nthawi yosanthula choonadi chimne ndapeza. Kodi ndikuona
kuti mphamvu zonse ndi Mulungu mu chionetsero kapena kodi ndi kuona
ndekha pamodzi ndi satana kulamulira dziko lapansi? Kodi ndikukhulupiliradi
kuti ali mfumu ya mafumu ndi mbuye wa Ambuye, Alefa ndi Omega woyamba
ndi wotsiliza kapena ndikuganiza kuti “ Ndili ndi mphamvu zangazanga
ndipo satana ali ndi mphamvu zake? Kodi ukuona chiyani?

VUTO LA “ MPHAMVU” KUGWIRITSIDWA NTCHITO PA CHOIPA.

Tibwereranso ku funso loti “ Kodi Mulungu akohza bwanji kukhala
wolamulira pa zoipa? Ndikuganiza kuti tilingalire pa udindo wake monga
mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa Ambuye. Ngati Mulungu ali mfumu pa
mafumu onse a dziko lapansi komanso Mbuye wa Ambuye onse apa kodi
Sali iye wolamulira pa choipa? Kodi ena mwa mafumu awa Sali oipa?

Kodi ena mwa Ambuye awa Sali oipa? Ngati munthu asankha kugwiritsa ntchito mphamvu ya Mulungu mwa iye kosayenera mmalo mwa koyenera, kodi apa ndiye kuti mphamvuyo siikhalabe ya Mulungu? Popeza kuti munthu akugwiritsa ntchito mosiyana ndi cholinga cha Mulungu kodi apa zikutanthauza kuti Mulungu Sali kumulamulirabe iye?

Ndikuganiza za abale ake a Yosefe amene adali ndi njiru, pamodzi ndi mkwiyo kugulitsa Yosefe ku Aigupto. Kodi Mulungu sadali mu ulamuliro wa ntchito zawo popeza tsopano adali kufuna kugwiritsa ntchito mphamvu za Mulungu mosayenera kuti akaphe mmalo moti akachilitse? Kodi iwe ukuganiza chiyani?

Yosefe adali mneneri. Adali munthu amene amaona zolinga za Mulungu ndipo pamene adapenyera adaona kuti Mulungu adali kulamulirabe ngakhale kuti abale ake a Yosefe adasankha kugwiritsa ntchito mphamvu ya Mulungu mkati mwawo mu njira yosayenera. Iye adalankhula motere “ Koma inu munandipandira ine choipa koma Mulungu anachipangira chabwino kuti kuchitike monga lero kupulumutsa amoyo anthu ambiri....” (**Genesis 50:20**).

Kodi umatha kuona ichi pamene ukuyenda mozama mu moyo wako? Kodi ngakhale mphamvu za munthu woipa zili mphamvu ya Mulungu koma yogwiritsidwa ntchito mosayenera ngakhale kuti Mulungu ali mkati molamulira? Kodi ukuona kuti munthu akhoza bwanji kuona mozama za ichi? Kodi timatha kulingalira mu njira yotere? Sindikukhulupilira chomwecho. Maganizo anga Sali oyambasuka motere ndipo kumvetsa kwanga sikuli kozama motere. Ndikhoza kukomoka ngati ndingathe kuganizira kuti ndidayenera kukhala wa nzeru motere ndipo mmalo mwake ndimangopemphera. Ndimalankhula motere..... “ Mulungu, chonde ndilankhuleni ndi kundionetsera chomwe chikuchitika? Kenako iye amayamba kulankhula mu zolemba zanga kundipatsa vumbulutso pamodzi ndi chidziwitso kuposa kenekalikonse ndimaganzira kapena ndimalota. Mwa ichi sindikhala wa nzeru komanso wozama mu maganizo pamodzi ndi mtima kupyolera mu kuyesetsa kwanga ndimakhala wanzeru pamodzi ndi wozama pomvetsera kulankhula kwa wanzeru ndi wankuru mwa ine. Kodi ukuganiza kuti ukhoza kuzichita mwa mphamvu zako ndi Umulungu wakowako? Ungolola kuti Mulungu akhale Mulungu mkati mwako. Zimasule ndi kukhala mmanja mwake. Leka ntchito zako za thupi ndi kulowa mu mpumulo wake (**Aheberi 3ndi 4**).

Pofuna kuti upitilire kumvetsa bwino, talingalira za umo anthu a mkwiyo adafuulira motere, “ Mpachikeni, mpachikeni? Ndipo Pilato amene adalephera kusunga chilungamo adasamba mmanja. Kenako tsopano ona zonse zimene Mulungu adachita zomwe zalembedwa pa Machitidwe 4:27-28.

MULUNGU ALI CHIKONDI

Pano tsopano tikuona limodzi mwa mkhalidwe la Mulungu. Kodi Mulungu amene tikumupembedza ali ndi chikondi chondipatsa kapena kuti iye ali chikondi? Ngati ndikusowa chikondi, ndipo ndifika kumupempha iye kuti andipatseko kodi apa ndikupempha zenizeni kapena zachabechabe? Kodi ukuganiza bwanji?

Ndikukhulupilira kuti ndikukupempha mosayenera. Ndikukhulupilira kuti kupemphera kotere ndi zotsatira za kusamvetsa za chimene Mulungu ali komanso chimene ife tiri popeza sitikulankhula za chimene ife tili, mu chaputala ichi, apa sitikamba kena kalikonse koma patsogolopo tikamba. Koma apa tikukamba za chimene Mulungu ali tsono tiyeni tione zimene Yohane adakamba za iye..... “Ndipo ife tadzindikira ndipo takhulupilira chikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi ndipo iye amene akhala m’chikondi akhala mwa Mulungu ndipo Mulungu akhala mwa iye.....”

(1 Yohane 4:16)

Ngati ndikusowa chikondi kodi ndikusowa chimene Mulungu ali nacho. Kapena ndikusowa chimene Mulungu ali? Ngati ndikusowa kenakake, komwe iye ali nako, ndikhoza kumupempha za ichi. Ngati ndikusowa chimene iye ali apa ndiye kuti ndikusowa kumupempha iye kuti adzitsanule yekha mu mtima mwanga kupyolera mwa Mzimu Woyera.

OSATI DONGOSOLO LOKONZEKANSO MWA IWE WEKHA KOMA DONGOSOLO LOLOWA MMALO MWA LOYAMBA.

Ukhoza kumazilankhulira mwa iwe wekha motere, “ Ndi mau chabe amene ukuwadzindikira umonso umalankhulira....” *AYI, AYI, AYI!* Si mau chabe sindikadatsutsana ndi mau. Nkhondo yanga ndi kuona kuti uli ndi

Mzimu Woyera amene Mulungu akufuna. Kusiyana pakati pa mapemphero awiri ali pamwamba apa ndi chimodzimidzi kusiyana pakati usiku ndi masana pakati pa chikhristu ndi chipembedzo, pakati pa Mulungu ndi Satana.

Ngati ungatehe kukumbuka bwino, adali satana amene adalankhula motere, “Udzakhala ngati Mulungu” Ali yemweyo amene nthawi zonse kukhazikitsa mwa ine ndekha makhalidwe a uMulungu. “Udzakhala ngati Mulungu” (**Genesis 3:5**) satana akutero. Pemphera kwambiri ndipo yesetsa yesetsa! Yankho labwino ku maganizo a ziwanda zotere ndi lotere, “Bwerera kumene udachokera!” chifukwa choti zidachokera ku Gehena.

Ngati Mulungu safuna dongosolo lolikonzanso mwa mphamvu ya umunthu mmene ndikhoza kugwira ntchito kwambiri kuti ndikhale wolungama ndi lachikondi komanso lodzindikira chilichonse, apa ndiye kuti ndi dongosolo la mtundu wotani lomwe Mulungu akuyendetsa? Ili ndi dongosolo la kulowa mmalo mmene iye akudzilowetsa mmalo ndi iye yekha ndi kukhala wobisala mwa Khristu Yesu amene tsopano wakhala moyo wanga. Iye sagwirizana ndi chilungamo chochilenga ndipo mmalo mwake amalowetsa chilungamo cha Mulungu. Nthambi mu mpesa siikhala ya moyo pa yokha. Ndi moyo mwa nthambi umene uli wochokera ku mpesa. Tifotokoza za ichi patsogolopo. Ndiloreni kuti ndilankhule kuti sitikusewera chabe ndi mawu awa. Tikukamba za njira ziwiri zosiyanasiyana za chikhalidwe.

Mulungu ali chikondi ndipo pamene ndikusowa chikondi chomwe ndikusowa apa ndi kuyenda kwa Mulungu mwa ine. Ichi ndi chinthu chophweka kwambiri mwa ichi ndimamupempha iye kuti ayende mwa ine, nditakweza maso anga pa iye ndi kutchera ku kuyenda kwa Mzimu mkati mwa mtima wanga. Ntheradi, Mulungu amayenda mu moyo wanga ichi ndi chosiyana ndi kukweza maso anga pa ine mwini ndi kulankhula motere, “Mulungu ndithandizeni”

MTENDERE WA MULUNGU KAPENA MULUNGU WA MTENDER.

Mkhalidwe wina wa Mulungu. Mulungu ali ndi mtendere kapena kodi iye

ali mtendere? (Afilipo 4:7,9). Ndikudzindikira kuti pali nthawi zambiri ndimasowa mtendere ndipo pamene ndafika kwa iye mu pemphero, nditatsokonezeka, iye amalankhula mu zolembe zanga motere, “ Mariko, khala mu mtendere, ine ndiri pompano.....” Mariko, wakhala akundilankhula motere aikwi zingapo kuti ndikhale mu mtendere chifukwa choti iye adali pomwepo ndipo pomaliza pake ndidakhala mu mtendere chifukwa choti iye adali pomwepo. Mwa maphunziro chabe, ndidali kudzikindikira kuti Mulungu ali Emmanueli – Mulungu ali nane. Koma kudzikindikira mwa maphunziro kusiyana ndi kumuona iye akuyenda yenda mmoyo mwako. Ndi kupyolera kumuona Mulungu mmoyo mwanga pamene ndidachotsedwa ku kudzikindikira Mulungu mwa maphunziro ndi kukhala tsopano mu chiyanjano cha Mzimu Woyera (II Akorinto 13: 14)

Apanso adali satana amene adatiyesa ife kuti tichoke ku mtengo wa chidziwitso kuti tikhale ngati Mulungu mwa ife tokha odzikindikira chabwino ndi choipa. Tidayesetsa kukhala mu njira ya satana ndipo tsopano tili ndi zipembedzo zikwi ziwiri ndi mazana atatu (2300) Ndipo chilichonse pachokha chakhazikitsa fundo zao pamodzi ndi zikhulupiliro zawo. Izi zikuonetseratu poyera kuti penapake zinthu sizili bwino chifukwa Yesu adalankhula kuti tiyenera kukhala AMODZI. Njira yokhayo imene ndikudzindikira kuti tikhale AMODZI ndi kusiya kudya mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa (kusiya kuyendera maganizo athu) ndi kuyamba tsopano kudya mtengo wa moyo umene ali Yesu- mpesa ndipo ife monga nthambi zake. Ndaphunzira kukhala mwa Mzimu Woyera wokhala mkati mwanga amene amandilembetsa osati maganizo anga chabe.

Tidzalankhula za ichi patsogolo pa nthawi ino, tiyeni tingodzindikira kuti sitikufuna kumudzindikira Mulungu mwa maphunziro mokha chabe. Tikufuna iye kuti ayende mu mitima yathu ndi mu mizimu yathu. Kwa ine kwandichera mu mtima mwanga kuti Mulungu aliyense mu zonse komanso kuti Khristu ali moyo wanga.

FUNDO ZOYENERA PA CHAPUTALA CHACHIWIRI

- Mulungu ali wankuru kuposa maganizo anga
- Mulungu ali wamphamvu yonse
- Mulungu ali chikondi
- Mulungu ali mtendere

- Chimene ndikusowa ndi Mulungu
- Sindikusowa kuti Mulungu andipatse china mwa chikhalidwe chake koma ndikusowa iye kukhala moyo wanga.
- Ulembere mu zolemba zako fundo zina zomwe waphunzira.

KUGANIZA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi Mulungu umamuona bwanji? Kodi chaputala ichi chakuthandiza kuti umuone iye? Ngati ndichomwecho, motani? Fotokoza kusintha kulokonse kumene ukuona
- Kodi waphunzitsidwa kudya ku mtengo wa moyo kapena ku mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa? Kodi munthu amadya bwanji ku mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa? Kodi munthu amadya bwanji ku mtengo wa moyo?
- Kodi kulemba ntchito imene umachita tsiku ndi tsiku? Kodi uli ngati Davide ndi ena onse mu malembo opatulika odziwa kulemba zinthu za Mulungu zolankhulidwa kwa iwe? Kodi zikuoneka zopindula kwa iwe kuchita motero? Kodi zikhoza kukwaniritsa chosowa china chilichonse ukuona mu moyo wako?
- Kodi umakhala mwa maphunziro pa za Mulungu kapena umamuona mu mtima mwako? Kodi Afansi adakhala motani? Kodi kuli koyenera kukhala mwa uzimu kapena mwa maphunziro chabe? (Omwe akufuna kukhala ndi kumvetsa bwino za izi akhoza kuwerenga buku lotchedwa “Kumuona Mulungu moyo wako” lolembedwa ndi Mariko Virkler.
- Lingalira mozama ma chaputala otsatirawa pogwirizana ndi choonadi ichi ukhoza kufuna kulemba mwa pemphero mu buku la padera. **Aheberi 11: 3, Akolose 1:11, 17, Machitidwe 17:28 1 Akorinto 1:30, Akorilose 3:4**
- Kukhudzana ndi Mulungu monga wamphamvu yonse werenga **Yesaya 45:5-7 Masalmo 75:6- 7 Miyambo21:1 Aroma 8:28, 13:1-5, Aefeso 5: 20, 1 Atesalonika 5:18.**
- Kulemba – Uemphe Mulungu chimene akufuna kulankhula kwa iwe kukhudzana ndi choonadi ichi mu chaputala ichi. Lembera zonse akulankhula mu buku lapadera. Onetsetsa kulemba funso kumapeto kwa tsamba lililonse monga njira yotsegula kuyenda kwa Mzimu ngati sizili za chinsinsi, khala wokonzekera

kuwerenga zolemba zako pa gulu lako. Zikomo kwambiri polola kuti ugawane ndi amzako. Adalitsa a Mulungu akhale pa iwe.

CHAPUTALA CHA CHITATU CHOONADI # 2-

Kodi umazona wekha bwanji? Kodi uli wamphamvu, wanzeru waluntha, wachikondi wosamalira, wochereza alendo, wolimba mtima? Kodi ukhoza kuganiza mwa iwe wekha? Kodi ukhoza kulingalira zinthu mwa tchutchuchu? Kodi ukhoza kugwira ntchito mwa mphamvu mu moyo wako? Kodi umatha kukonza mavuto okomana, nawo ndi njira yozama? Kodi waphunzirapo kuwayangata bwino? Kodi umatha kudzionana wekha? Kudanditengera nthawi yayikuru kuti ndikathe kuzimvetsa ndekha chimene ndili. Pa nthawi yaitali, ndimagana kuti ndidali kanthu kenakake kanzeru, kaluntha, kamphamvu kokhona kuganiza mwa ine ndekha ndi zina zotero.

Ndidadzindikira kuti pamene ndidali ndisadadzipeke kwa Ambuye, ndidali munthu wotayika amene ndidali kuyenda njira za ine ndekha. (Yesaya 53:6). Tsopano ndimafuna kutsatira njira ya Mulungu. Ndi dafuna kukhala moyo wotsatira iye. Tsopano ndimafuna kutumikira iye, kumukonda, komanso kumulambira iye. Ndidapita khomo ndi khomo kuchitira umboni chifukwandimafuna kufotokozera anthu onse za Yesu. Ndidakhazikitsa chifuniro changa kungoyesa tchimo mu moyo wanga komanso kukhala woyera pamaso pake.

Apa utha kuona kuti “Ine” ali phata la ndime yonse. Sikuti “ine” ndi amene akugwira ntchito Ali ndi zina zotero.

Zonse izi zili zotsatira za kusamvetsa chimene “ine” ali ine sindili mwa ine ndekha. Sindili wamphamvu mwa ine ndekha ine ndili CHOTENGERA.

CHOTENGERA?

..... “Chotengera?” ukutero.

..... “Koma tiri nacho chuma ichi m’zotengera zadothi kuti ukuru woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu wosachokera kwa ife.....”

(II Akorinto 4:7)

Inde chotengera! Tsopano ndikufuna kulingalira za ichi mu kamphindi

kochepe. Ntchito ya chotengera nchiyani? Ntchito yake ndi kunyamuliramo kanthu kenakake. Ukutanthauza kuti chifukwa chimene ndikukhalira ndi kunyamulira kanthu kenakake? Kodi ndingokhala pansi ndi kudzilola ndekha kudzadzidwa ndi kanthu kekakake? Ayi sindili mu zotero. Sindili kuyang'anira mphamvu yina yake ya uzimu kuyenda kupyolera mwa ine. Ndikufuna kuonetsera poyera kuti ndikhoza kuima pa ndekha ndi kuchita zimene ndikhoza kuchita ndi mphamvu yanga yanga ndikhoza kupemphera ndi kukamwa kwanga ndikhoza kukonda, kumuda munthu, komanso kuchita china chilichonse ndikufuna.

Ayi ukungoganiza kuti ukhoza kutero chifukwa choti wanyengedwa Adamu ndi Heva ku munda wa Edeni mmalo moti adye mtengo wa moyo, anadya wodziwitsa zabwino ndi zoipa satana adawauza motere, “mudzakhala ngati Mulungu.” Ndipo Adamu ndi Heva adakhulupilira chinyengo ichi ndipo adagwa mmalo moti azione okha monga anthu okhala pamaso pa Mulungu nthawi zonse kuchita naye chiyanjano, adayamba tsopano kukhala mwa iwo okha. Tsono pamene Mulungu adawaitana iwo, adabisala. Chiyanjano cha uzimu chidapasuka ndipo adakhala tsopano otsutsika.

Apa ndi pamene sitepe ya chipulumutso imayamba kuchokera ku chidziwitso chokhala opanda Mulungu kubwera ku chidziwitso choona kufurukira kokhala ndi Mulungu. Nkoyenera kwa munthu kudzindikira kuti “wina” wake (Mulungu) ayenera kukhala mwa iye monga iye ali chotengera.

KUKHALA CHOTENGERA OSATI CHA CHINTHU CHINA KOMA CHA MUNTHU WINA

Sikuti ndalengedwa kukhala chotengera cha “chinthu china chake” koma cha “munthu wina wake” sikuti ndangokhala chotengera komanso ndi “kachisi wa Mulungu”

..... “Kapena simudziwa kuti thupi lanu lili kachisi wa Mzimu Woyera amene ali mwa inu amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha.....” **(1 Akorinto 6: 19)**

Kodi ntchito ya kachisi nchiyani? Ndikuganiza kuti ntchito yake ndi kusungiramo Mulungu: Apa tikhoza kuona kuti talengedwa kukhala chosungiramo Mulungu wamphamvu yonse!

WINA WAKE AMAYENDA MWA IFE

Sikuti ife tangokhala kachisi motengeramo Mulungu wamphamvu yonse komanso kuti Khristu wasanduka kukhala mpesa ndipo ife ngati nthambi zake.

..... “Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake. Wakukhala mwa ine ndi ine mwa iye ameneyo abala chipatso chambiri pakutoi kopanda ine simungathe kuchita kanthu.....” **(Yohane 15:5)**

Kachisi akhoza kusunga Mulungu koma nthambi imapeza moyo wake kuchokera ku mpesa wake. Ndipo moyo uwu umakhala pomwepo nthawi zonse. Mwa ichi, pali kuyenda kwa Mzimu wa Mulungu kosalekeza kupyolera mwa ine kumene kumaonekera mwa thupi ndipo mwa thupi ndipo mwa kudziyenga kwanga ndimaganiza kuti ndi ine amene ndikukhala ndi moyo koma sikuti ndi ine koma ndi moyo kuchokera ku mpesa.

Ine ndili woposa chotengera chosunga madzi popeza ndili kachisi wa Mulungu wosunga mntsinje wa Mzimu Woyera. Mulungu amayenda mwa ine monga ngati mntsinje.....” Koma tsiku lomaliza lalikuru la phwando, Yesu anaimilira nafaula ndi kunena ngati ndi munthu akumva ludzu adze kwa ine namwe. Iye wokhulupilira ine chilembo chimati mntsinje ya madzi amoyo idzayenda kuturuka mkati mwake koma ichi anati za Mzimu amene iwo akhulupilira iye anati adzalandire pakuti Mzimu panalibe pamenepo chifukwa Yesu sanalemekezedwa pa nthawi pomwepo.....” **(Yohane 7:37-39)**

Pamene ndikuyenda, ndisamaganize kuti ndikukhala ndi moyo kwa ine ndekha mwa mphamvu zanga. Ayi, ndine amene ndimayenda wotchera khutu ku mntsinje wa madzi amoyo mkati mwa mtima wanga. Mphamvu zanga zimachokera apa. Ndaombedwa ku moyo wodzidalira mwa ine ndekha ndipo tsopano ndimadalira pa Mulungu. Sindikhala womvetsera ku maganizo kapena mphamvu zanga. Ndimamvetsera ku kuyenda Mzimu mu moyo wanga. Ilo ndi phata la mphamvu yanga pamene ndikusowa mphamvu, ndimayang’ana kwa iye amene amakhala mwa ine ndi kukweza maso anga pa iye ndipo ndimadzalankhula motere, “Yesu, khalani mphamvu

yanga pa nthawi iyi” sindikweza maso anga pa iye kuti andikonzenso koma kuti akhale ine. Tikhoza kufotokoza kuposa apa.

UMODZI WENIWENI

..... “Ndipo Iye mutu wa thupi- Eklesiayo ndiye chiyambi, wobadwa woyamba wotuluka mwa akufa kuti akakhale Iye mwa zonse woyambayamba.....” (**Akolose 1:18**)

Monga kulili kuti mutu ndi umene umalamulira thupi lonse, chomwecho Yesu amalamulira ine. Nthawi zonse maso anga ndimakweza pa Iye (**Aheberi 12:1**) Kumvetsera ku kuyenda kwa Mzimu, kuonerela masomphenya ake kumva kulankhula kwake, komanso kuchita zonse andilamulira. Ndimakhala monga iye amakhallira pa dziko lino lapansi.....

Ndipo Yesu anayankha nati kwa iwo,..... “ Indetu, Indetu ndinena kwa inu sakhoza mwana kuchita kanthu pa yekha koma chimene aona Atate a chichita ndicho. Pakuti zimene Iye azichita zomwezo mwananso azichita momwemo.....” (**Yohane 5:19**)

..... “ Sindikhoza kuchita kanthu kwa ine ndekha koma chomwe ndimva ndiweruza ndipo maweruzidwe anga ali olungama chifukwa choti sinditsata chifuniro changa (**Yohane 5:30**).....” Umu ndimo ndimakhalira. Moyo si monga ine ndichitira kalikonse mwa mphamvu zanga. Si ine kuyesera kukonda, kapena ine kuyesera kukhala kapena ine kuyesera kupemphera Ayi, Ine ndalumikizidwa kwa wina wake (**1 Akorinto 6:17**)

Iye ali moyo wanga. Iye ali mphamvu yanga. Iye amatsogolera maganizo anga sindichita kanthu kwa ine ndekha. Pamene ndikusowa kudzindikira umo ndingalingalire za chinthu china chake, ndimatchera khutu ku Mzimu Woyera wokhala mkati mwanga pamodzi ndi kukweza maso anga pa Yesu ndi kulankhula motere..... “ Ambuye chonde, ndidziwitseni zoti ndichite pa vuto ili ndipo kenako ndimadzindikira choti ndichite” Ndimona kuyenda kwa Mzimu mkati mwanga kuonekera.

SINDINACHIONE ICHI PAMENE NDIDANGOTEMBENUKA MTIMA KUMENE.

Pamene ndinapereka moyo wanga kwa Yesu Khristu, sindidli kudzindikira kuti ndili “ chotengera cha wina wake”. Ayi ndidaganiza kuti “ Ine ndakhala ndi moyo zaka zonse izi. Sindidali kudzindikira kuti moyo wanga usadapulumutsidwe, ndidali ndili chotengera- koma apa ndidali kukhala

mu mzimu wa dziko lapansi osati Mzimu Woyera. Ndidali ndisadatsegule mtima wanga kwa iye amene ali zonse mu zonse. Tsono ngakhale adali nane, komanso amandipatsa moyo pamodzi ndi mpweya, ndidali kugwiritsa ntchito izi kutemberera dzina lake popeza sindidali kumudzindikira iye. Ndimaona ngati kuti ali kutali- kumwamba –kusalikana ndi moyo wanga. Sindidamudzindikire iye monga Mbuye. Ndimaganiza kuti ndidli kutsogolera moyo wanga mwa ine ndekha.

Kupusa kotani pamodzi ndi kusapenyetsetsa! Ndidali kulamulidwa chabe ndi mzimu wina wa dziko lino lapansi ndipo ndidali mwana wa mkwiyo mwa chilengedwe..... “Ndipo inu anakupatsani moyo pokhala munali akufa ndi zolakwa ndi zochimwa zanu zimene munayendamo kale monga mwa mayendedwe a dziko lapansi lino monga mwa mkuru wa ulamuliro wa mlengalenga, wa mzimu wakuchita tsopano mwa ana a kusamvera amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale, mzilakolako za thupi ndi za maganizo..... (Aefeso 2:1-3)

Sindidali ndekha kuchita zotero koma kuti ndidali kulamulidwa ndi mzimu umene padakali pano ukugwira ntchito mwa ana akusamvera. Ndidali pansa pa ulamuliro wa satana ndipo ndidali kuchita zofuna zake.

..... “Koma ayamikidwe Mulungu kuti ngakhale mudakhala a kapolo a uchimo tsopano mwamvera ndi mtima makhaliwe aja a chiphunzitso chimene munaperekeracho ndipo pamene munamasulidwa ku uchimo munakhala akapolo a chilungamo” (Aroma 6:17-18)

Ndakhala kapolo wa wina wake pa nthawi yaitali ndidali kulamulidwa ndi mzimu wa dziko lapansi kapena Mzimu Woyera ndipo ndidakhala kapolo wa mphamvu yake. Ine ndili munthu amene ndikulamulidwa ndi wina wake kapena kusungidwa ndi wina wake..... “

..... “Mwa izi adatipitsa malonjezano a mtengo wake ndi aakuru ndithu kuti mwa izi mukakhale oyanjana nao umulungu wake mutapuluma ku chivundi chiri pa dziko lapansi mchilakolako..... “ (II Petrol 1:4)

Apa tsopano mukhoza kumvetsa bwino. Tiri olamulidwa ndi mzimu wa dziko lapansi kapena tiri zotengera za Mzimu Woyera. Zotsatira zake ndi kukhala kapolo ku uchimo kapena kapolo wa chilingamo.

KUSANTHULANSO FUNDO ZA PA CHAPUTALA CHACHITATU

- Ndife zotengera
- Ndife akachisi
- Ndife nthawi zomezetsedwa ku mpesa
- Ndife thupi la Yesu ndipo Iye ali mutu
- Ndimakhala mwa Mzimu Woyera.
- Mu nthawi imene tidali tisadapulumutsidwe tidali zotengera
- Tisadapulumutsidwe, tidali akapolo ku mzimu wa dziko lapansi.
- Tsopano tiri odzala ndi Mzimu Woyera.
- Tchula fundo zina zomwe zili zothandiza kwa iwe kuchokera mu chaputala ichi.

KUGANIZA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi satana ali chotengera (**Yesaya 14:12 –15**), **Ezekiel 28:11-17**)? (Dzina loti Lusifara litanthauza (Chotengera cha kuwala)
- Kodi umadzindikira kuti udali chotengera usadabwere kwa Yesu? Kodi ukuganiza bwanji za iwe wekha?
- Kodi tsopano ukutha kudzikindikira kuti uli chotengera pamene tsopano wakwera kw a Yesu? Kodi umayenda mwa chitsogozo cha Mzimu Woyera? Fotokozani zimene umazona mu moyo wako tsiku lili lonse. Kodi umachita zinthu wekha kapena umapempha Mulungu kuti akuchitire? Kodi umapenyererera luntha lako kapena umatchera khutu ku kuyenda kwa mzimu Woyera wolumikizana ndi mzimu wako? Kodi umapenyererera ku mphamvu zako kapena umadalira pa Mulungu?
- Kodi njira yoyenerera kutipangitsa kukhalabe odzindikira kuti ndife zotengera kapena kuti tiri akachisi kapena thupi la Yesu? Zikuonetsa kuti kuli kosavuta kuyiwala ichi ndi kuyamba kuziganizira mwa ife tokha. Nchifukwa chiyani timayiwala ichi mosavuta? Nchifukwa chiyani timayamba kudzidalira ndi kumayima pa tokha? Kodi pali njira yolewa ichi. Njira yake ndi iti?
- Kodi ukhulupilira kuti tchimo la ku munda wa Edeni lidali zotsatira za kuchoka kwa Mulungu ndi kuchita zofuna za okha?
- **KULEMBERA** – Utenge nthawi ukulemba choonadi waphunzira mu chaputala ichi. Pamwamba pa tsamba ufunse

Ambuye zimene akufuna kulankhula kwa iwe kukhudzana ndi kukhala chotengera. Lembera yankho lake. Konzekera kuwerenga zolemba zako pa gulu lako. Limbikitsa ena pamene akumvetsera mau amene Ambuye akulankhula mu zolemba zako

CHAPUTALA CHACHINAYI CHOONADI # 3- SINDILINSO NDI MOYO.

Ndimasowa vumbulutso la choonadi chafotokozedwa mu chaputala chomaliza, chonena kuti ndili chotengera. Ndidakhala moyo monga mkunja mu chinyengo choti ndidali ndi mphamvu zomazilamulira ndekha basi wopanda wina kukhala mwa ine monga wolamulira moyo wanga. Ndidalibe kudzindikira kulikonse, kuti satana adali kulamulira moyo wanga. Ndinalankhula motere, “ Palibe angalamulire moyo wanga kapena kundiuza zoti ndichite! “ chinyengo chotani! Mzimu wa satana umayenda mwa anthu mwa mphamvu koma osazindikira ndipo amaganiza kuti ali iwo kuchita zotero koma ali satana kuonetsera moyo wake kupyolera mwa iwo. Amaganiza kuti ali ozilamulira okha koma zoonza zake ndi zoti ali panso pa ulamuliro wa satana. Amaganiza kuti ali kapolo wa wina wake koma choti ali kapolo wa tchimo (Aroma 6:17). Vuto lidayamba pamene ndidakhala mkhristu. Ndidalowetsa chinyengo changa mu moyo wanga wa chikhristu. Popeza ndidakhulupilira kuti moyo wanga wakale pa chikhristu ndidali “ Ine” kukhala ndi moyo mwa ine ndekha, ndidaganiza kuti moyo wanga wa kutsogoloko ndiye kuti ndikhala wa chikhristu chenicheni. Koma kodi mukutha kuona chinyengocho? Sindidali ine ndekha masiku akalelo kapena kodi ndili “ Ine” kukhala mwa ine ndekha pa nthawi ino. Ndi Yesu kukhala ndi moyo mwa ine.

..... “ Ndinapachikidwa ndi Khristu koma ndiri ndi moyo wosatinso ine ayi koma Khristu ali ndi moyo mwa Ine.....”
(Agalatiya 2:20)

Kodi ukuganiza kuti ndikadakhosha kumvetsa bwino Vesi ili pamwamba apa? Osati pa moyo wako! Oh! Inde, ndikadakhosha kuilemba. Ndidali ndi kumvetsa kochepekera pa tanthauzo lake mwa maphunziro a mau a Mulungu koma kuti ndikhale moyo wogwirizana ndi vesilo chidali chinthu chovuta kwambiri. Ndimaganiza kuti idali kutanthauza kuti sindiyenera kukhala ndi moyo mwa ine ndekha koma kuti Yesu ayenera kukhala ndi moyo mwa ine.

Koma mutha kuona kuti kupachikidwa kwa maganizo anga kudali koti ndikukhala ndi moyo mwa ine ndekha kusiyana kotani ndi choonadi chake chenicheni! Koma umo ndimo ndidali kuonera. Kunyengedwa kotere kudali kwakukuru zedi kotero kuti pa nthawi yaitali ndidakhala moyo wotero. Pa zaka khumi ndi zisanu (15) ndimaganiza kuti ndidali kukhala moyo mwa ine ndekha. Sindidali kudzindikira kuti ndidali chotengera kapena kapolo kwa wina wake. Ndidakhulupilira kuti ndidali wolamulira kupusa kotani ndikakumbuka ichi koma pa nthawiyi sikudali kuoneka ngati kupusa. Icho chidali chokha chokha choonadi kwa ine. Palibe aliyense amandiuza zosiyana ndi zimenezo.

KUSAKANIKIRA KWA CHIKHRISTU NDI CHIPEMBEDZO.

Mpingo wanga udali kundiuza kuti “ tsopano ndiyenera kukhala moyo wa Yesu” mmalo mondiuza kuti “ Khristu Yesu akhale moyo wanga” Tsono ndidayamba kutsatira mokhulupilika chinyengocho ndi kuyamba kukhala moyo wa Yesu mwa ine ndekha. Ndidali kuchitira umboni mwa ine ndekha mmalo mokhala ndi Khristu Yesu mwa ine kumachitira umboni. Umboni wanga udali mu chidziwitso changa cha mau osati mu chionetsero cha mphamvu ya Mulungu. Yesu sadali kuloweza pa mtima zoti aphunzitse koma kuti iye adali chotengera ndipo mkati mwa iye mudali mphamvu ya mzimu yomwe imayenderera monga mbali imodzi ya moyo wake ndipo adali kuchita zokhazo zimene amapenyenera Atate akuchita komanso kulankhula mau okhawa amene iye adali kumva Atate akulankhula. Iye adali kuchilitsa odwala kuukitsa akufa, kukonza akhate, kulalikira mau a Mulungu. Kusiyana kotani ndi umo ndimalalikilira mau a Mulungu! Ndimangolalikira zimene ndaloweza pa mtima panga kutsutsa nazo ochimwa basi. Anthu ochimwa sadali kubewera kwa ine kuzaona mphamvu ya Mulungu koma anali kundithawa kuopa ziphunzitso zanga za mmutu.

Ndimayesera kumakonda anthu chifukwa akhristu ayenera kukonda adani awo koma ndidali “ Ine” kuchita zonse izi Baibulo likufotokoza momveka bwino kuti ndiyenera kufa ku ntchito zanga za thupi ndi kulowa mu mpumulo wake (Aheberi 3:4). Tsopano popeza ndadzindikira kuti sindilinso ndi moyo mwa ine ndekha, ndimangofika kwa Yesu ndi kulankhula motere, “ Inu muli moyo wanga ndipo muli chikondi cha zonse, tsono masulani mphamvu yanu ndi chikondi chanu kupyolera mu chotengera chanu pa nthawi ino ndipo ili

ndi pemphero langa” Apa mutha kuona kuti sindili kulankhula za ine ndekha. Sindikukweza maso pa ine ndekha kapena pa china chilichonse pakuti sindilinso ndi moyo mwa ine ndekha koma kuti Yesu ali wamoyo mwa ine. Mwa ichi ndimakweza maso anga pa Yesu amene ali moyo wanga ndipo kenako ndimayamba kuyitana pa iye kuti amasule mphamvu yake ndi kuionetsera kupyolera mu chotengera ichi limene lili thupi lake. Ichi ndi chimene chili choonadi chenicheni. Ichi ndi chimene uyenera kuchita. Ichi ndi chimene chimagwira ntchito mu moyo wanga.

CHOFUNIKIRA – KUMVETSA KOZAMA KWA ZIMENE CHIPANGANO CHIKUFUNA.

Ndimasowa kumvetsa kozama pa zimene chipangano chatsopano chikufuna. Mwa chitsanzo, Paulo adalankhula motere..... “ Koma dama ndi chidetso chonse kapena chitsiliro zisatchulidwe ndi kutchulidwa komwe mwa inu monga kuyenera oyera mtima.....” (Aefeso 5:3)

Apa ndidaona ngati zikutanthauza kuti ndiyenera kutaya zonse pamodzi ndi zodetsa zonse. Chomwe akutanthauza apa ndi ntchito iliyonse yochitika mwa iwe wekha osati mwa Mzimu Woyera wodzadza mwa ine. Padali malamulo ambiri mu Baibulo ku chipangano chatsopano. Ena amatero kuti ndiyenera kusenza onsewo. Chomwe ndimalephera kudzindikira ndi tanthauzo la “ Ine”

TANTHAUZO LA “INE”

..... “ Ndinapachikidwa ndi Khristu koma ndiri ndi moyo wasatinso ine ayi koma Khristu ali ndi moyo mwa ine koma moyo umene ndiri nao tsopano mthupi ndiri nawo mchikhulupiliro.....” (**Agalatiya 2:20**). Kodi ndi yani ku chipangano chatsopano amene atchedwa kuti “Ine”? Iye ali “Khristu”. Tsono pamene kuchipangano chatsopano akutero kuti “Ine” kuchita kanthu kenakake zikutanthauza Yesu kuchita kupyolera mwa ine. Ndiyenera kumvetsa bwino apa. Ndi Yesu kugwira ntchito mwa ine komanso kukhala wa moyo mwa ine osati ndekha kutero.

Pa Afilipo 4:13 akufotokoza motere posindika za ichi..... “ Ndikhoza zonse mwa iye wondipatsa mphamvuyo..... “

Ndikhoza kuzipanda ndekha ndi kulankhula motere..... “Iwe, undekha, tsopano usayiwale kulingalira za iwe wekha mu njira yotere kuyambira tsopano mpaka mtsogolomo” komabe likhoza kubwererabe ku chipembedzo chifukwa choti ndi chipembedzo chimene chimalankhula motere, “Iwe chita ichi komanso ukatha uchite icho”. Ayi koma tsopano ndikulankhula motere, “Khristu Yesu chonde ndikumbutseni za choonadi ichi nthawi zonse ndikufuna kugwa mu msampha wozidalira ndekha ndi kumaganiza kuti ndi ine chabe kuchita zoterezo”. Tsopano udindo wonse umakhala wa mphamvu ya Mzimu Woyera yokupangitsa kukhala chimene uli osati kuziyerekeza wekha ayi.

CHIPEMBEDZO-, “NDIYETSETSA KUCHITA ICHI”

Mchitidwe wonse wa uchipembedzo umakhala mkati mwa moyo wa munthu ndipo umakhala mbali iliyonse ya moyo wa munthu. Ndi Yesu yekha amene angachilitse ichi. Chinyengo chokhala munthu wa chipembedzo pembedzo mu kutsatira njira ya Mulungu ndi choti imaoneka yabwino komanso yooneka mokongola kunja chabe ndipo nkovuta kukhulupilira kuti ndi zinthu zolakwika komanso za ziwanda. Koma tamvetserani zimene chipangano chatsopano chikukamba kukhudzana ndi kuphonya Yesu amene ali mutu komanso ali mphamvu ya moyo wathu ndipo mmalo mwake kumatsatira malamulo amene ukufuna kuwamvera.

..... “Munthu aliyense asakunyengeni ndi kulanda mphoto yanu ndi kudzichepetsa mwini wake ndi kugwadira kwa angelo ndi kukhalira mu izi adazona wodzitukumula chabe ndi zolingalira za thupi lake wosagwiritsa mutuwo, kuchokera kwa iye amene thupi lonse lothandizidwa ndi kulumikizidwa pamodzi mwa fundo ndi mitsempha, likula ndi makulidwe z Mulungu ngati munafa pamodzi ndi Khristu kusiyana nazo zoyamba za dziko..... “ **(Akolose 2:18-23)**

Fundo ndi yoti sindingathe kuchita kenakalikonse ngati poyamba sindidathe kwa ine ndekha ku moyo wanga wa thupi sindingathe kukonda chifukwa ndi chikondi cha Mulungu kutsanulidwa mu mtima wanga sindingathe kupempherera chifukwa sindidziwa umo ndingapempherere koma mzimu atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka. Sindingathe kuchita

kanthu mwa ine ndekha koma chokhacho chimene ndikutha kuchipenya komanso chimene ndikutha kumv kwa Ambuye (**Yohane 5: 19, 20, 30**). Mwa ichi ndi ine amene ndimakhala wotchera khutu chabe kukuyenda kwa mzimu pamene kukuyenda kwa ine. Ndimapenyenera masomphenya a Mulungu oyenda mkati mwa ine. Ndimapenyenera pamodzi ndi kulembera zimene iye akulankhula pamodzi ndi kuvumbulutsa ndipo ndimamulola Iye kuchita ntchito yaikulu imene yomwe yavumbulutsidwa kupyolera mwa ine Iye wakhala Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiliza. Iye ali zonse mu zonse mu moyo wanga.

KUSANTHULANSO FUNDO KUCHOKERA PA CHAPUTALACHA CHINAYI.

- Sindilinso wa moyo sindifuna kukhala ndi moyo mwa ine ndekha
- Chipembedzo sichidzindikira kuti sitikhala ndi moyo
- Chipembedzo chimatiphunzitsa kuti tiyenera kuyesetsa
- Chikhristu chimatiphunzitsa kuti tisiye kuyesetsa koma kuti tilowe mu mpumulo wake.
- Ulembe fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe.

LINGALIRANI PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi umadziganizira mwa iwe wekha kapena za Khristu Yesu? Fotokoza tchutchuchu yense kukhudzana ndi funso ili
- Kodi waphunzitsidwa ndi chipembedzo ku kuyesetsa kapena waphunzitsidwa ndi chikhristu kusiya kuyesetsa koma kulowa kulowa mu mpumulo wake fotokoza kuphunzitsidwa ku kuyesetsa, lapa povomereza bodza lotere ndipo tsopano ukhale moyo watsopano mwa Khristu Yesu. Pa gulu lanu lochepa mukhoza nonse kupemphera pamodzi
- **KULEMBERA-** “ Ambuye, kodi mukufuna kulankhula nane chiyani kukhudzana ndi fundo yoti sindilinso ndi moyo? Kodi ndakondwa mu msampha wa chipembedzo? Kodi ndikhoza kumasulidwa motani? Lembera ndi mayankho a Ambuye mu bukhu lapadera. Fikani okonzekeratu kugawana mtima wako ndi gulu lochepa la anthu limene uli nalo. Ndibwino kuwerenga chigawo kapena zolembera zako kwa anthuwo.

CHAPUTALA CHA CHISANU
CHOONADI # 4 KHRISTU ALI MOYO WANGA

Tsopano pomaliza pa zonse tathana nawo Sali wa moyo ku choipa kapena ku chabwino. Iye ali wakufa. Tsopano takonzekera kulowetsa dongosolo la Mulungu mwa ife mmalo mwa dongosolo lathu lathu. Tagonjetsa ganizo loti izi ndi zinthu zochitika mwa mphamvu zathu. Izi sizili chomwecho ayi. Iye achotsa zonse mwa ine ndipo abwezeretsa moyo wa ku Edeni ndipo tsopano ndidzikhala mu chiyanjano chenicheni ndi Mulungu- kudya chipatso cha mtengo wa moyo. Sindidzatsata chidziwitso changa popeza chili mtengo woletsedwa wodziwitsa zabwino ndi zoipa. Tsopano ndidzatchera khutu ku mtima wanga kumvetsera ku kuyenda kwa madzi amoyo oturuka mwa ine pamene ndikukweza maso anga pa yesu yemwe ali woyamba ndi wotsiliza wa chikhulupiliro changa. Tsopano sindichita kanthu kena kalikonse mwa ine ndekha. Ndaphunzira kukhala monga Yesu, yemwe ali chitsanzo changa amene sadali kuchita kanthu mwa iye yekha koma chokhacho chimene amaona Atate akuchita (Yohane 5:19,20,30) Koma payenera kutenga kanthawi kuphunzira kukhala mu njira yotere chifukwa choti ndakhala wophunzitsidwa mu njira yolakwika. Ndili ndi zizolowezi zambiri zomwe ndakhala nazo pa nthawi yaitali zomwe ndiyenera kudzipasula. Kodi ndidatero kuti ndidzadzipasula? Oh, chabwino apa mukutha kuona chimene ndikutanthauza. Pa matenga nthawi kugonjetsa chinyengo ichi ndiloleni ndiyetsere kawiri. “Ndili ndi zizolowezi zambiri zimene Yesu angathe kupasula”

Ichi ndi chinthu chabwino ndi chofunikira ndikudzindikira kuti chimene ndikusowa ndi gulu londithandiza kuti tikathe kufika ku cholinga chokhala “mwa Khristu Yesu” amene ali moyo wathu ukhoza kumadabwa motere, “Ngati sindili kutenga mbali kugwira ntchito zotere tsopano ndizichita chiyani?” Funso lalikuru kwambiri! Ndimayembekezera kuti ukhoza kufunsa motere.

NTCHITO YA CHOTENGERA CHA THUPI NDI
KUZIPENYETSETSA CHOKHA PA YESU”

Ndikupenyenera pa Yesu amene ali woyamba ndi womaliza wa chikhulupiro changa. Kodi izi zikutanthauza chiyani? Mu chigiriki, mawu oti “ Kupenyenera pa Yesu” pa Aheberi 12:1 zitanthauza “ kuzipereka kwanthunthu” Izi zitanthauza kuyamba kuona Yesu penapaliponse ndi penyerera. Baibulo likufotokoza kuti ukadyetsa wosauka, apa ndiye kuti wapereka kwa Yesu ndipo pamene ndapereka madzi kwa munthu wa ludzu apa ndiye kuti ndapereka kwa Yesu. Izi ndi zoonza chifukwa choti Yesu ali zonse mu zonse. Mwa iye zinthu zonse zikhala limodzi (Akolose 1-17). Izi zinamupangitsa iye yekha kudzionetsera kupyolera m,u chinthu china chilichonse pa dziko lapansi komanso ngakhale kuthambo.

Ndimatchera khutu ku masomphenya pamene ndikuyenda ndipo ndimalankhula motere,..... “ Ambuye, mungandionetsereko inu nokha pa nthawi ino?” Nthawi zonse ndimakhala wopenyerera za uzimu. Monga aneneri a chipangano chakale timakhoza kumuona Mulungu mu kavuluvulu mu mkuntho wa mphepo, mu zitunda mmitengo, mu chilengedwe. Davide adalankhula motere,..... “ Ngakhale ndibisala ku gehena inu muli komweko..... “ tsono palibe malo ndingapite osatha kumuona Emmanueli – Mulungu ali nafe. Pamene ndikupenyenera masomphenya amene amaika pamaso panga ndimamupempha kuti alankhule nane ndipo kenako ndimatchera ku kuyenda kwa maganizo mwa mzimu oturuka mu mtima mwanga. Tsopano ndapeza kuti tanthauzo la Mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu “ umene Paulo adali kutanthauza pa Aroma 8.

Tsono ndimakhala ndi moyo bwanji? Ndimakhala ndi moyo monga wolandira. Ndimalandira mphamvu ya uzimu ndi kukhala mogwirizana nayo, Inde zochitika zimafika monga mwa zotsatira chabe. Mulungu adawauza ana a Israeli motere, “ Ine ndine Yehova Mulungu wako.... “ Yasamitsa pakamwa pako ndipo ndidzalidzaza.....”

(Masalmo 81:10)

Kodi ukatha kuona ubalewo? Mulungu ali wombolo wamphamvu. Iye lai mphamvu ndi ulamuliro. Ine ndoi amene ndimatsegula kukamwa kwanga ndipo iye amadzadzako. Kodi udayamba waonapo mwana wa mbalame mu chisa pamene may ake afika ndi mphusi kapena kuti nyongolosi? Chomwe umaona ndi kukamwa kwake kotseguka. Icho ndi chakudya chathu. Timakhala

pansi ndi kukamwa kwathu kotseguka kulandira kekakalikonse kuchokera kwa Mulungu ndi kumulola iye kukhala wa moyo mwa ife ndi kugwira ntchito iliyonse mwa ife. Ntchito iliyonse imachitika kupyolera mu mphamvu yake. Ngati ndingaichite kupyolera mu mphamvu yanga, imasanduka ntchito yakyfa (**Ahebri 6:1-2**).

“TISALENGA MA ISHMAELI”

Mukukumbukira pamene Mulungu adamuza Abrahamu zinthu zadzikuru zimene adzachite kupyolera mwa iye (**Genesis 12:15**)? Atadikira pa nthawi yochepa (zaka khumi ndi chimodzi) (11) pa Mulungu kuti a kwanilitse icho ndipo Poono kuti sadakwanilitse mwa changu, Abrahamu pamodzi mkazi wake adaonza ganizo labwino umo angathe kumuthandiza Mulungu kuti akwanilitse zolinga zake mwachangu. Zonse adachita zidapherezera ku kubadwa kwa Ishimaeli amene Mulungu adamukana polankhula motere, “Ayi, ndidzakupatsa mwana kupyolera mwa Sara,…” Mu njira yomweyo, ndimalenga kapena kubereka a Ishimaeli pamene ndachita chanu kuyesa kukwaniritsa mau a Mulungu mwa ine ndekha ndi mphamvu zanga komanso ndi nzeru zanga. Chikhaliidwe cha moyo wanga pachiyambi chidali chodzadzidwa ndi a Ishimaeli- ine kuyetsetsa kusangalatsa Mulungu mwa mphamvu zangazanga.

NTCHITO ZA KUFUFA

Mulungu amazitcha izi kuti zili “ntchito zakufa”
..... “Mwa ichi polekana nao mau a chiyambidwe cha Khristu tipitilire kutsata ukuru msikhu osaikanso maziko a kutembenuka mtima kusiyana nazo ntchito zakufa ndi a chikhulupiliro cha pa Mulungu “ (Ahebri 6:1)

Ntchito yakufa ndi iliyonse ndimachita mwa ine ndekha mmalo molola kuyenda kwa Mzimu kuti kuchite ntchitoyo. Pfupifupi moyo wanga wonse wa pa chiyambi wa chikhristu changa udali wodzadza ndi ntchito zakufa. Ndidali ine kuchita ntchitoyo osati Mzimu Woyera mwa ine. Ndidadyedwa ndi ndi chipemebedzo pamodzi ndi chifansi koma osadzindikira konse chinthu choopsy ndi choti zinthu zambiri zikuchitika mu dzina la chikhristu masiku ano zakola mu msampha womweo chifukwa choti tadya ku mtengo

wodziwitsa zabwino ndi zoipa osati kukhulupilira mtengo wa moyo.
“..... Ufumu wa Mulungu ukwatulidwa ndi mphamvu ndipo outenga akutero ndi mphamvu.....” Ndatsimikiza mtima kuti okhawo amene ali a mphamvu polimbana ndi mdani wa Mzimu wa zhipembedzo ndi amene angathe kulowa mu chidzalo cha chimene Mulungu akufuna. Kodi ukhoza kukhala mmodzi wa iwo? Kodi ukhoza kufika kwa khristu wa moyo mkati mwa moyo wako kapena kodi ukhoza kungokhala womudzindikira iye mwa maphunziro chabe a za mau a Mulungu? Chisankho ndi chako.

NJIRA YA TSOPANO YA MOYO.

Tsopano mapemphero anga akufanana potsatira motere: “Mulungu kodi ndi fundo yanji imene mumafuna kuti ndichite? Kodi ndi dzina liti lemene ndidaiwala? Phwanyani mphamvu ya mdani youkira ine. Tumuzani mngelo wanu ndi uthenga wanu kupyolera mwa ine pa nthawi ino. Ambuye ndikumasula chikondi chanu kupyolera mwa ine pa nthawi ino. Lolani chikondi chanu chidzame mwa ine. Dulani khungu la mtima wanga ndipo muchotse mkwiyo pamodzi ndi mantha. Ndikutsutsana ndi Mzimu wamantha mu dzina la Yesu. Ndikudzudzula ganizo lililonse lotsutsa mu dzina la Yesu. Ambuye, vomerezani kuona mtima kwanga pamodzi ndi maganizo znga. Ambuye sinthani zokhumba za moyo wanga. Khazikitsani zokhumba zanu mwa ine. Ambuye ndikukuthokozani chifukwa choti mwazilumikizitsa nokha kwa ine komanso kuti muli moyo wanga. Ndikukuthokozani kuti muli wamphamvu pa dziko lonse lapansi. Ambuye, chonde, masulani mphamvu kupyolera mwa ine tsopano lino.....”

Timadzindikira za moyo wathu komanso kuti wina amakhala mwa ife. Timalingalira za kumwamba osati za dziko lapansi popeza tafa ndipo moyo wathu wabisika mwa khristu Yesu.

FUNDO ZOCHOKERA PA CHAPUTALA CHACHISANU.

- Sindikhala ndi moyo pa choipa
- Sindikhala ndi moyo pa chabwino
- Sindilinso ndi moyo
- Khristu ali moyo wanga
- Sindiyenera kulimbana nako pochita zinthu
- Ndiyenera kudzipenyererera ndekha pa Yesu yekha nthawi zonse
- Ntchito iliyonse ndimachita mwa mphamvu zanga ndi yokufa

imene ndiyenera kulapa.

- Machitachita ena alionse ndingachite pofuna kukwaniritsa masomphenya a Mulungu pa moyo wanga zotsatira zake kumakhala kubadwa kwa ma Ishimaeli omwe ndi mavuto chabe ndipo zimakanidwa ndi Mulungu. Ndiyenera kulapa ma Ishimaeli onse.
- Tsopano mapemphero anga onse ndi kuyitana pa Ambuye.
- Lembera fundo zina zimene waona kuti zili za tanthauzo kwa iwe.

LINGALIRANI PAMODZI NDI KUKAMBILANA.

- Kodi zimapangitsa moyo kukhala wopheka pokungozipenyera wekha pa Yesu Khristu? Kodi palibe zinthu zina pamene tikhoza kuzipenyereraponso? Kodi nanga kudzipenyera tokha pa ntchito iliyonse pamaso pathu? Kodi tingathe bwanji kudzipenyera tokha pa Yesu ndi pa ntchito imene ili pamaso pathu nthawi yomeweyo? Kodi izi ndi zotheke? Ngati ndi chomwecho zingachitike bwanji? Fotokoza umo ungachitire. Kodi ichi ndi chimene Mulungu akufuna kuchita?
- Kodi nkotheke kukhala moyo wa Umulungu nthawi zonse? Ngati ndi choncho, fotokozani umo ungachitire- ngakhale tsiku limodzi lokha kodi kukhala pamaso pa Mulungu kukhoza kukhala chizolowezi chimene tingaphunzire? Kodi chizolowezi chotere chikhoza kulowetsedwa mmalo mwa chizolowezi chokhala mwawekha? Kodi ndi nthawi yaitali bwanji chikhoza kutenga kuphunzira chizolowezi chotere ngati ngati tingakhoze kupempha Yesu kuchikhazikitsa mu mitima yathu? Kodi chikhoza kutenga nthawi yaitali? Kodi ukhoza kudzipereka wekha kuphunzira chikhalidwe cha moyo watsopano wotere? Kodi ukhoza kukhala ndi gulu limene likhoza kukulimbikitsa kukhazikitsa moyo watsopano wotere? Kodi ukhoza kulimbikitsa anthu ena mu gulu lotere? Ngati ndi chomwecho, penyerera pamodzi ndi kukhala wodabwitsidwa pa zimene Mulungu akuchita mu moyo wako komanso pa gulu lako.
- Lembera njira zina zabwino zomwe ukulingalira zimene ukhoza

kuzigwiritsa ntchito kukuzilimbikitsa wekha pamodzi ndi ena kuti asunthe kuchokera ku kukhala moyo mwa okha ndi kubwera kwa Yesu pamene ukuziwona wekha kapena iwo akuyenda mu chitsokeretso cha iwo okha (kutanthauza kuti tiyenera kutenga nthawi ndi kuzitonholetsa tokha pamaso pa Khristu ndipo tione zimene iye atilankhule pa ichi) kapena tiyeni titenge nthawi tsopano ndi kupemphera mphamvu ya Mulungu kuti itsanulidwe. Pa ichi)

- **KULEMBERA** – tenga mabuku ako ndipo ulembere pamwamba pa tsamba motere, “ Ambuye kodi mukufuna kulankhula chiyani kwa ine kukhudzana ndi moyo wanga? Kodi izi zikutanthauza chiyani ku thupi pamodzi ndi kuuzimu? Lankhulani nane Ambuye- ndikukupemphani. Zikomo, Ambuye” Kenako tchera khutu ku kuyenda kwa mzimu ndipo upenyere maso ako pa Yesu ndipo ulembe zimene zikulankhulidwa mkati mwa moyo wako. Konzekera kugawana ndi anmzako pa gulu lako.

CHAPUTALA CHACHISANU NDI CHIMODZI- CHOONADI # 5- NDAFA KU CHILAMULO.

Tisadapitilire tiyeni tidzindikire kuti kugonjetsa “ *MUNTHU WOSAUKA INE*” njira yake ndi kudzindikira kuti Mulungu aliyense mu zonse komanso kuti ife tili zotengera chabe zimene iye ayenera kuzidzadza. Sitikhala ndi moyo mwa ife tokha koma Khristu akhala wa moyo mwa ife. Kodi ukhoza kukhulupilira izi talankhulazi? Zanditengera matsamba ambiri kulankhula izi! Tsopano tiyeni tipitilire kufukulabe fungulo lina lomwe litimasule ku “ munthu wosauka ine”

1. KUKHALA MOYO NDI MASO ANGA OPENYERERA PA MALAMULO A MULUNGU.

Ichi ndafotokoza kale pa chaputala choyamba ndikuona lamulo mu chipangano chatsopano kuti ndiyenera kuchita kanthu kenakake ndipo ndimayesetsa kuchita zimenezo. Kenako ndimadzaona lamulo lina ndipo ndimazayetsa kuchita limenelonso. Pomaliza pa zonse ndidadaona kuti ndidali ndi malamulo ambiri ndipo adali katundu wolemera. Ndimaona

kulephera pamodzi ndi kutsutsika komanso kutsautsika ndipo ndidalira motere, “Uwu siuli moyo wochuluka!” Apa Ambuye adavomerezana nane. Umo siudali moyo wochuluka! Koma kodi ndi chinthu cholakwika chanji ndidali kuhita? Kodi sindidali woyenera kuti ndidzipenyere maso anga pa malamulo a Mulungu ndi kuyesetsa kuwamvera? Ukudziwa kale mbali imodzi ya yankho. Ukudziwa kale kuti suyenera kuyesera kuchita kanthu. Ukudziwanso kuti siuli ndi moyo koma Khristu ali moyo wako. Tsopano tikhala tikuphunzira malo amene lamulo liyenera kugwira ntchito mu moyo wa munthu wokhulupilira.

KULALIKIRA PHIRI LA SINAI KAPENA PHIRI LA KALIVARE.

Adali Paulo Yonggi cho amene adalankhula motere, “Ukhoza kulalikira kuchokera pa phiri la Sinai. Kapena kuchokera pa phiri la Kalivare” Ngati ukulalikira phiri la Sinai, apa umalalikira malamulo a Mulungu. Ngati ukulalikira phiri la Kalivare umalalikira za mphamvu ya Yesu wouka mkati mwa mtima wa munthu wokhulupilira. Ulaliki wina wa ku imfa ndipo wina wa ku moyo. “amenenso anati kwanilitsa ife tikhale atumiki a pangano latsopano si la chilembo koma la mzimu pakuti chilembo chipha koma mzimu uchititsa moyo. Koma ngati utumiki wa imfa wolembedwa ndi woleledwa m’miyala unakhala m’ulemerelo kotero kuti ana a Israeli sanathe kuyang’anitsa pa nkhope ya Mose chifukwa cha ulemerelo wa nkhope yake umene unali kuchotsedwa..... “

(II Akorinto 3:6-9)

UTUMIKI WA CHITSUTSO NDI IMFA KAPENA UTUMIKI WA CHILUNGAMO NDI MOYO.

Kodi ukhoza kulingalira chabe kukhala ndi “Utumiki wa chitsutso?” Nanga za “Utumiki wa Imfa?” Mwina ukhoza kukhala mlaliki woyendayenda kufalitsa chitsutso pamodzi ndi imfa kulikonse udapita. Mwina udakhoza kulemba mu buku lako motere:

..... “Munthu wapadera mu utumiki wa chitsutso ndi imfa! Ndikukuvomereza kubweretsa kutsutsika konse pamodzi ndi kulakwa mu moyo wako. Chifukwa uli woyenera kulandira ichi. Wachimwa ndipo Mulungu amadana ndi ochimwa. Ndikuyandikitsa ku malamulo a Mulungu amene wawapasula kuti ulape ndi kufika pamaso pake ndi kulira pamodzi ndi kubuula. Pakutha pa uthenga wanga udzudzika koopsya!.....”

Ukuoneka ngati ulaliki wabwino, kodi sichomwecho? Makamaka ngati ndikufungatira kutsutsika pamodzi ndi kulakwa ndi kumaganiza motere, “Mulungu wandipatsa uthengawu monga wanga” “Bwerani, alaliki ndipo ndidzudzuleni. Ahh zili bwino ndithu. Mubwerenso nthawi yina.”

Mwatsoka, chipembedzo chimavomereza zoterezi ndipo ichi ndi chifukwa chake chimakhala chopepuka uku dziko lapansi. Mtumiki wa chitsutso akulalikira kuchokera pa phiri la Sinai.

Mtundu wina wa utumiki umene ukutchulidwa ndi wa chilungamo – utumiki wa moyo. Uthenga wa mtumiki wotere umakhala wotere “Ndiloleni ndikufotokozereni chimene muli mwa Khristu Yesu. Khristu wakumasulani ku lamulo pamodzi ndi chitsutso chake ndipo wakuvekani ndi chilungamo chake chomwe sichili chanu koma chobwera mwa chikhulupiliro. Ndikuonetserani umo mungathe kutembenukira kwa iye kumulora Mulungu kuyenda mwa inu. Bwerani ndipo phunzirani kuti mulibe malire alionse kwa Mulungu.....”
Ndikukhulupilira kuti mudayanjanitsidwa ndi Mulungu ndi uthenga wa mtundu wotere komanso kupyolera mwa mtundu wotere. Uyu akulalikira kuchokera pa phiri la Kalivare. Iye akuonetsera choonadi chenicheni cha pangano latsopano.

TAFA KU CHILAMULO.

..... “Chotsatira abale anga, inunso munayesedwa akufa ku chilamulo ndi thupi la Khristu, kuti mukakhale ake a wina ndiye amene anaukitsidwa kwa akufa kuti ife tim’balire Mulungu zipatso pakuti pamene tinali mthupi zilakolako za machimo zimene zinali mwa chilamulo ... Zinali kuchita m’ziwalo zathu kuti zibalire imfa zipatso koma tsopano tinamasulidwa ku chilamulo.....” (**Aroma 7:4-6**)

Nthawi zina pa moyo wanga ndiyenera kudzindikira kuti sindilinso ndi moyo ndi chilamulo kutanthauza kuti sindikhala ndi moyo popenyererera pa chilamulo. Anthu adachita zoterozo mu nthawi ya pangano lakale koma osati panopa. Ndafa ndipo moyo wanga wabisika mwa Khristu Yesu. Yesu wakwaniritsa zosoweka zonse za chilamulo zimene sindikadatha kuchita

monga ndili munthu wochimwa.

Tsopano Khristu ali ndi moyo mwa ine kundipatsa mphamvu yokhala moyo wa chiyero koposa zimene chilamulo chimafuna. Ngati sindingathe kukureza maso anga pa Yesu pamodzi ndi mphamvu yake apa ndikhoza kugwa mu uchimo. Ichi ndi chifukwa chake ndikufunitsitsa kusungabe chilamulo monga ukonde wonditeteza kuti ngati ndikulephera kutsatira uzimu mkati mwa ine ndikhoza kutsungika ndi lamulo kuti ndisagwe mu uchimo.

ZOLINGA ZA CHILAMULO

Kodi cholinga cha chilamulo chidali chiyani? Padali zolinga zambiri. Chilamulo siidali mbali ya cholinga cha Mulungu. Chidayikidwa chifukwa cha kulakwa kwa anthu. Pamene ndidachotsa maso anga kwa Mulungu ndi kudula chiyanjano changa ndi Mulungu ku munda wa Edeni, Mulungu adayenera kuonjezera chilamulo chonditetezera kuti ndisadziononge ndekha kotheratu. Chidandiika mu nyumba ya ndende kuti ndisadziononge ndekha, apa mkuti chisomo chisadafike pa moyo wanga. Ndikadakhala kuti sindidasunge chilamulocho, ndikadakhala kuononga moyo wanga komanso osakhoza kupeza chisomo cha chipulumutso cha Mulungu pa mapeto ake.

..... “ Koma chisanadze chikhulupiliro tinasungidwa pomvera lamulo, otsekedwa kufikira chikhulupiliro chimene chikavumbulutsidwa.....” (Agalatiya 3:23) Mwa ichi, Mulungu adaonjezera chilamulo kundisunga ine kuti ndisadziononge ndekha chilamulo chidayeneranso kundiphunzitsa kanthu kenakake. Chidali namkungwi ndi phunziro la padera kuphunzitsa: sitikadakhala mwa mphamvu za ife tokha kukhala angwiro. Palibe wolungama ngakhale mmodzi. Tsono ndidayenera kuphunzira ichi ngakhale kuti ndidasunga chilamulo chonse komabe sindikadafika ku ungwiro umene uli mwa Yesu Khristu.

..... “ Momwemo chilamulo chidakhala na mkungwi wathu wa kutifikitsa kwa Khristu kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiliro.....”
(Agalatiya 3:24-25)

Kodi ndidaphunzira phunziro langa pamene ndidafika kwa Yesu? Kutanthauza kuti, kodi ndidaphunzira kuti ndiyenera kupenyenera kuchokera ku chilamulo kupita kwa Khristu? Ayi. Ndidangoyesera kwambiri kupeza malamulo mu Baibulo ndipo ndidapenyenera kuti ndiwasunge onse kuti ndisalatse Ambuye.

Zotsatira zake zidali kutsutsika kuweruzika pamodzi ndi imfa chifukwa choti mapeto a chilamulo ni imfa.

Ndidapeza Khristu ndi mau anga (Iye ali Mbuye wanga pamodzi ndi Mpulumutsi) koma ndidali ndisadapeze njira ya chikhulupiliro.....”

Pakuti inu nonse muli ana a Mulungu mwa chikhulupiliro mwa Yesu Khristu pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khristu, mudavala Khristu.
(Agalatiya 3:26-27)

Ndidalibe kumvetsa kovala Khristu kapena kukhala mwa Khristu kapena kukweza maso anga pa Khristu Yesu pa moyo wanga. Mmallo mwake, ndimakweza maso anga pa chilamulo pamodzi ndi zinthu zimene ndimayenera kumachita ndipo ndidapeza kuti zoonadi, chilamulo chimabereka imfa mu moyo wanga mu njira ya kutsutsika, kuweruzika pamodzi ndi kupyinjika osati moyo wochuluka umene ndimayembekezera kapena ndidauzidwa.!

MULUNGU NTHAWI ZONSE AMAPEREKA CHIYANJANO- MUNTHU WASANKHA CHILAMULO.

Mulungu sadafune kuti pakhala chilamulo kuyambira pa chiyambi. Iye adayika chilamulo chifukwa cha kuswa chiyanjano komwe kudachitika ndipo zotsatira zake zidali tchimo (**Agalatiya 3:17,19**) Ngakhale adayika chilamulo ichi, sadachikhumbe. Mose akufotokoza pa Deteronomo 5 kuti Mulungu adali kulankhula chabe mau ake kuchokera kumwamba! Chiyanjano chobwezeretsedwa, ku munda wa Edeni! Koma ana a Israeli sadamumvere chifukwa sadakonde moto pamodzi ndi kulankhula kwa mau ake. Zotsatira zake Mulungu adakakamizika kuwapatsa chilamulo.

Tsopano Mulungu akupereka ku mpingo wake kulankhula kwake (mau) kawirinso pamene akukhala mu mitima yathu ndi kutibweretsa ife ku phiri za Zioni. Phiri lomaliza lidali la Sinai malo a chilamulo. Tsopano ndi phiri la Zioni pamene munthu amakhala mu chiyanjano ndi Mzimu Woyera ndipo ali ndi chenjezo limodzi lokha lotere..... “Penyani mu sakane wolankhulayo pakuti ngati iwowa sanapululumuka..... “ (Aheberi 12:25). Chinthu choipitsitsa kwa ine ndi kubwereranso ku chilamulo kusiya kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu. Iye nthawi zonse amafuna chiyanjano kuyambira

ku munda wa Edeni ku Genesis mpaka ku ukwati wa mkwatibwi ku buku la chivumbulutso. Iye wakhala akufuna chiyanjano ndi chilengedwe chake. Ife takhala tikumukana ndi kumakadya mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa uku tikupenyenera ku ntchito zathu kuti zitipulumutse kapena kusunga chilamulo.

YANKHO LAKO

Kodi udzachita chiyani? Kodi udzakhala mwa chilamulo kuyetsetsa kuchitsata ndi kuchimvera kuti upulumuke? Kapena kodi udzakhala mu kulankhula kwa mau ake, pamodzi ndi masomphenya a mlengi kapena udzapenyenera maso ako pa malamulo a mau a Mulungu kapena kuti udzapeza yesu mu tsamba lilonse la m’Baibulo ukuwerenga? Kodi udzakhala ukuyesetsa mwa iwe wekha kapena udzalansira iye amene ali mwa iwe yemwe akupatsa mphamvu yokachita za uzimu zonse? Uyenera kusankha. Kuyenda mu chiyanjano ndi Mzimu woyera kumva kulankhula kwake, masomphenya pamodzi ndi katundu wa Mulungu kutsogozedwa ndi Mzimu kapena kuti udzakhala mwa iwe wekha ndi kusunga malamulo. Njira ina ndi ya ku imfa ndipo yina ndi ya ku moyo. “ Dzisankhireni lero amene mudzamtumikira” Ngati Mulungu mtumikireni. Ngati ndi chipembedzo chitumikireni koma dzindikirani kuti chidali chipembedzo chimene chidapha mwana wa Mulungu pakati pa ana a Israeli.

Ndikusankha kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu. Ndikusankha kupenyenera masomphenya pafupifupi, kumvetsera ku kulankhula kwa mau ake, ndi kukhulupilira zonse. Kutu ndichite chisankho ichi, ndidayenera kutaya zonse ndidaphunzira ndili mwana komanso miyambo yonse. Ichi sichidakhale chinthu chophweka koma chanditengera kupita ku madera amene sindidaganizire komanso chamasula madalitso a Mulungu pa moyo wanga mu njira zimene sindidaganizire. Mulungu wandilora kuyenda pa dziko lapansi kugawana ndi thupi la Yesu Khristu pomwe ine ndidali kukonzekera kudzakhala mlimi wa za ng’ombe za mkaka ku Lowville New York. Kodi iyi si njira chabe imene Mulungu ali?

Kodi unditsatira mu chisankho changa. Chokhala mu chiyanjano ndi Mzimu Woyera mmalo mokhala mu chilamulo ndi mu miyambo? Ndipemhera kuti utero.

KUSANTHULANSO FUNDO ZA MU CHAPUTALA CHA CHISANU

NDI CHIMODZI.

- Tafa ku chilamulo
- Chilamulo sichidali cholinga cha Mulungu.
- Chidaonjezeredwa chifukwa choti chiyanjano chidasweka monga zotsatira za tchimo.
- Chiyanjano chobwezeretsedwa chimachotsa kufunikira kwa chilamulo. Chilamulo chimatha kugwira ntchito izi modikilira chabe.
 - a. Kundisunga kuti ndisadziononge ndekha ndisadafike ku chisomo cha Mulungu chogwira ntchito mu moyo wanga
 - b. Kundiphunzitsa kuti ndilibe mphamvu ya kukhala wangwiro kupyolera mu kusunga icho. Ndikusowa mphamvu ya Yesu yondilimbikitsa pa moyo wa tsiku ndi tsiku pamene ndi kukhala.
 - c. Mulungu nthawi zonse amapereka chiyanjano
 - d. Munthu nthawi zonse amakana ubale ndi Mulungu ndipo amasankha chilamulo mmalo mwake kuswa mtima wa Mulungu pokhala tsopano munthu wa chilamulo womnzunza iwo amene apeza Mzimu Woyera.
- Kodi uyambapo kukhala mu chiyanjano ndi Mzimu wa Mulungu pa moyo wako nthawi zina kugwiritsa ntchito chilamulo kukuteteza pamene ukufuna kugwa mu chisomo cha Mulungu?
- Lembera fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe.

KULINGALIRA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi ukuona chiyani pa cholinga ndi phindu la chilamulo? Ndi zolinga zotani zimene chilamulo chadzadza moyo wako? Mu njira zotani chakuthandiza?
- Kodi ukuona chiyani monga malira a chilamulo? Mu njira zotani chakupweteka pa moyo wako?
- Kodi tsopano ukufuna kupenyereka pa chilamulo pa moyo wako kapena pa mphamvu ya Yesu yokhala mwa iwe? Ngati kupenyereka kwako sikuli pa Yesu pamodzi ndi Mzimu wake pa moyo wako, nchifukwa chiyani sizili chomwecho? Nchiyani

chimene chikukuletsa kupenyera? Nchiyani chikadasinthika mwa iwe kuti kupenyera uku kudzikulike? Kodi ukhoza kusintha pa nthawi ino?

- Kodi uli kuvomereza kuti Baibulo pamodzi ndi mbiri yakale zonse zikuchitira umboni kuti anthu osunga chilamulo adakana aneneri (iwo amene amakhala mwa chilamulo osati mwa Mzimu)? Kodi ndi mbali iti imene iwe uli? Ngati siudakhale mbali ya Mulungu kodi ukufuna kusintha? Ngati ndi choncho khala mu pemphero, kumpempha Mulungu kuti akusinthe mkati mwako.
- **KULEMBERA** – “Ambuye kodi mukufuna kulankhula kwa ine chiyani kukhudzana ndi chilamulo mu moyo wanga?”

CHAPUTALA CHA CHISANU NDI CHIWIRI CHOONADI # 6-
NDIMAKHALA MWA MZIMU (RHEMA – MAU OLANKHULIDWA A
MULUNGU NDI MASOMPHENYA)

Zoonadi, sindiyenera kukhala wotsogoleledwa ndi chilamulo. Uwo ndi mpumulo tsopano popeza ndidali kulephera kuchitsatira mu njira iliyonse. Tsopano ndili ndi mantha. Kodi chitandisunge kuti ndisalalikire komanso ndisaononge moyo wanga pamodzi ndi iwo amene ali ndi ine? Poyamba nkofunika kuti tisangotayiratu chilamulo ichi ndi chofunika kutiteteza ife. Ngati tingalephere kuyenda mu uzimu, apa ndiye kuti chilamulo chitithandiza pamene tikuyesetsa kuti tibwerere ku uzimu popeza tikudzindikira kuti iwo amene atsogoleledwa ndi Mzimu Sali omvera chilamulo. Gawo lina la yankho likupezeka pa Aroma 8:1-2 pamene akulankhula motere;

“ Chifukwa chake tsopano iwo akukhala mwa Khristu yesu alibe kutsutsidwa. Pakuti chilamulo cha mzimu wa Moyo mwa Khristu Yesu chandimasula ine ku lamulo la uchimo ndi la imfa,.....”

Panalibedi kutsutsidwa! Ichi ndi chinthu chachikuru popeza ndadzindikira kuti ndikukhala ndi moyo mwa Yesu Khristu, apa sindilinso ndi moyo mwa ine ndekha. Iye ali moyo wanga. Takambapo pa nthawi yaitali zoti “Mkhristu ali mwa ine” Apa pali pomveka bwino kwambiri. Koma lamulo ili akukamba

pa vesi 2 ndilo liti lomwe likutchedwa kuti “ Chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu? “ Kodi tingathe kusanthulapo za chilamulo ichi pang’ono pokha ndi kuona kuti chili chiyani ndipo chimagwira ntchito bwanji?

CHILAMULO CHA MZIMU WA MOYO MWA KHRISTU YESU

Ili liyenera kukhala limodzi la kumva malamulo onse opezeka mu Baibulo chifukwa choti landimasula ku lamulo la uchimo ndi la imfa- koma ku munthu wosauka” amene takamba za choyamba ndi chilamulo chimene chimachilitsa nkhondo (kulimbana) kochitika mu mtima ndi kubweretsa mtendere pamodzi ndi mphamvu komanso chikondi osati chitsutso. Izi ndi zodabwitsa zedi, Paulo! Kodi chilamulo ichi ndi chiti.

Paulo akuyamba ndi kufokoza za tanthauzo la chilamulo ichi ichi pa mavesi khumi ndi awiri oyambilira pa Aroma 8. Malingana ndi vesi yachitatu, apa vuto la kufooka kwa thupi la munthu lomwe limalephera kusunga chilamulo. Pa vesi ya chinayi Mulungu akulankhula kuti iye adzatipangitsa ife kutha kukwanilitsa zosoweka za chilamulo osati polimbana mwa mphamvu za thupi koma mwa mphamvu ya Mzimu Woyera yokhala mwa ife!

Ngati ndikweza maganizo anga pa mphamvu zanga za thupi kuti ndikagonjetse zilakolako za thupi langa, apa sindikwaniritsa chifukwa choti thupi langa lilibe mphamvu zogonjetsera ndipo pomaliza pa zonse ndidzakhala wodabwa.

..... “ Pakuti iwo amene ali mwa thupi asamalira zinthu za thupi koma iwo amene ali monga mwa Mzimu asamalira zinthu za Mzimu. Pakuti chisamaliro cha thupi chiri imfa koma chisamaliro cha Mzimu chiri moyo ndi mtendere” (Aroma 8:5-6)

Chomwe ndingachite ndi kukweza maso anga pa mphamvu ya Mzimu Woyera yokhala mwa ine ndipo ndiitane. Zotsatira zake zidzakhala, moyo pamodzi ndi mtendere chifukwa Mzimu wa Mulungu uli ndi mphamvu zogonjetsera zilakolako za thupi langa. Ponjezerapo, siilinso nkhondo pakati pa ziwalo za ine ndekha. Ichi ndi chigonjetso chochitika ndi Mzimu wa Mulungu.

..... “ Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Khristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa mwa Mzimu wake wakukhala mwa inu. Chifukwa chake ife tiri amangawa si ake a thupi pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi mudzafa koma ngati ndi Mzimu mufetsa zochita zake za thupi mudzakhala ndi moyo.....” (Aroma 8:11-14)

Njira yokhayo yobweretsera moyo ku matupo athu ndi kupyolera mu ntchito kwa mphamvu Mzimu Woyera. Mwa ichi, ndiyenera kuphunzira umo ndingagonjetsere thupi langa kupyolera mu mphamvu ya Mzimu Woyera sindikudzindikira ngati ndidayambapo kumva uthenga wa umo ichi chingachitikire? Uwu ndi uthenga wake koma umo tingakhalire ku chipangano chatsopano.

Kunena zoon, mpingo umene ndimapempheramo siudali kukhulupilira za Mzimu Woyera. Pomaliza pake pamene ndinapeza mpingo umene umalalikira za moyo wopezeka mu Mzimu, adangondiuzza kuti ndidayenera kukhala ndi mzimu woyera. Sadandifotokozere kuti ndichita bwanji. Mwa ichi sindidadzindikire umo ndingapatsire mphamvu thupi langa mwa Mzimu Woyera yemwe adalumikizana ndi Mzimu Wanga. Ndidakhala moyo wakufa wotere pa zaka zambiri. Ndidali kusowa kumvetsa umo ndingathe kugwiritsa ntchito Mzimu Woyera ku moyo wanga wa Chikhristu mogwirizana ndi chipangano chatsopano. Nchosadabwitsa kuti ndidakola mu msampha wa chipembedzopembedzo.

UMO UNGAPEREKELE MPHAMVU KU THUPI LAKO KUPYOLERA MWA MZIMU WOYERA.

Pali moyo – mphamvu komanso machitachita mu mzimu wa Mulungu. Pamene mayi wina wake adakhudza yesu kuti apeze machilitso, Yesu adalankhula kuti adaona mphamvu itaturuka mwa iye. Mau oti “ Energis” ndi amodzi mwa mawu atatu ku chipangano chatsopano otanthauza “ Mphamvu” ndipo amatanthauzanso kuti “ machitachita” pali mphamvu ya padera imene imakhoza kuchokera mu thupi la munthu wina kupita kwa wina makamaka pamene wakhuzidwa. Anthu ena otona zithunzi akhala akuona

kuwala kwa padera kuturuka mmanja mwa mlaliki pamene akupempherera machilitso.

..... “ Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi mudzafa koma ngati ndi mzimu mufetsa zochita za thupi mudzakhala ndi moyo (Aroma 8:13).....”

Pali njira ziwiri zogonjetsera thupi kuti life ku ntchito zake. Yoyambira ndi kugwiritsa ntchito mphamvu za Mzimu Woyera. Yachiwiri ndi kugwiritsa ntchito chifuniro chako ndi mphamvu zako imene nthawi zambiri siikhoza kugwira ntchito. Zotsatira za njira yachiwiri iyi kumakhala “ kupemphera kwa imfa” kosakhala mwa Mzimu Woyera. Tsopano tisanthula umo tingagonjetsere ntchito za thupi kupyolera mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

LAMULO LIMODZI – KUKHALA MWA MZIMU.

Uyenera kudzindikira muyeso wa mzimu wako pophunzira kudzindikira umo mzimu wako umakhalira. Pali njira zambiri zochitira izi. Ndidafufuza mu malembo opatulika pa za mtima ndi mzimu ndipo ndidadzifunsa ndekha motere, “ Kodi ndaonapo fungo la mzimu la kufotokozedwa mu vesi? “ Ngati ndi chomwecho, uwu ndi uzimuwo. Njira iyi idali thandizo labwino ku kumvetsa umo fungo la uzimu limakhalira. Chitsanzo cha zimene baibulo likufotokoza za kuona fungo la Mzimu Woyera ndi zipatso zisanu ndi zinayi za mzimu woyera zomwe ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, (Agalatiya 5:22). Izi zimalengedwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera yokhala mkati mwathu.

LAMULO LACHIWIRI – KUPENYERERA PA MZIMU WOYERA WOLUMIKIZANA KU MZIMU WAKO.

Ndimamuona Mulungu kupyolera mwa masomphenya (mau olankhulidwa (rhema) pamodzi ndi katundu (kumene kuli kukhudzikwa kwa moyo pamene ndikudzindikira pamaso pa Mulungu kumpempha iye kugawana nane machitachita a mtima wake ndi ine). Ndimazitonholetsa ndekha pamaso pa Mulungu amene ali Mzimu pamene ndi kupemphera komanso kulingalira mozama malembo opatulika – komanso nthawi zina pamene ndikupemphera kapena kuyimba mwa mzimu (Aefeso 5:18, Yuda 20-21.)

LAMULO LACHITATU – KULORA MZIMU WOYERA

KUKUFUNGATIRA..

Mzimu Woyera ali Mulungu mu ofesi ya Mzimu. Tiyenera kulumikizana nawo. Ayenera kukhala mwa ife. Tiyenera kukhala womasukira ku Mzimu wa Mulungu. Baibulo limatiphunzitsa kuti tiyenera kusamvetsa chisoni Mzimu Woyera. Nkotheka kumvetsa chisoni Mzimu Woyera. Izi zikhoza kuchitika posalabadira zosangalatsa Mzimu. Ndimadzindikira kuti pamene sindidalabadiridwe. Ndimakhumudwa. Ndimadzindikiranso kuti pamene ndalabadiridwa pamodzi ndi kulemekezedwa, ndimamva bwino mu moyo wanga ndipo ndimakhala womasuka. Izi zili chimodzimodzi ndi Mzimu Woyera. Mwa chitsanzo, pamene tiri mu kalasi ndipo ndiitana mphamvu ya Mzimu Woyera, ndimaona ikuyenda mkalasi monse. Ndikukhulupilira kuti umakhala mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu umene timakhala tikuona. Machitachita ophweka otere a Mzimu Woyera amasiyanitsa chikhalidwe chonse pa dziko lapansi.

LAMULO LACHINAYI – KULANKHULA ZIMENE MZIMU WOYERA WAVUMBULUTSA

Tsopano ndidzayamba kudzadzidwa ndi Mulungu, kulankhula zimene zikuwira mkati mwa ine. Ndine amene ndatengedwa ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu yomwe ikuyenda mwa ine.

..... “ Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu pakuti chimene tizipempha monga chiyenera sitidziwa koma Mzimu mwimi atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka.....” (Aroma 8:26).

Poyamba sindidali kukhulupilira kuti Mulungu amaganiza kuti sindidali kudzindikira kapempheredwe. Tangomvetserani kwa ine! Ndikhoza kulankhula kwa Mulungu. Koma monga taona kale, chilichonse chimene ndimachita mwa mphamvu za ine ndekha osati za Mulungu chili ntchito yakufa ndipo izi ziphatikirapo kupemphera. Sindiyenera kupemphera mwa ine ndekha. Ndiyenera kupereka mwayi kuti Mulungu alankhula kupyolera mwa ine. Ilo ndi pemphero lenileni. Mwa ichi ndimamufikira Mulungu kuzitonholetsa ndekha kufunafuna masomphenya, kuchera khutu ku kuyenda kwa Mzimu ndipo kenako kuyamba kuyimba pamodzi ndi kupemphera mwa mzimu mkati mwanga. Kenako pang’ono ndi pang’ono ndimayamba kuona kuyenda kwa Mzimu mkati mwanga. Ndimamva ngati kutumphatumpha kwa

moyo. Uwo ndi moyo wa Mzimu Woyera kupereka mphamvu ku mzimu wanga. Imakhala mphamvu yopereka moyo wanga mtendere, chikondi chikhulupiliro, chiyembekezo, pamodzi ndi chimwemwe mwa Mzimu Woyera!

KUBWERERANSO KU CHILAMULO CHA MZIMU WA MOYO MWA KHRISTU YESU.

Monga takamba poyamba tikukhulupilira kuti ili ndi phatala chikhristu ku chipangano chatsopano. Kulankhula mwa tchutchuchu mwake.

Chilamulo cha mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu ndi mphamvu imene munthu amaimva mkati mwake pamene wakweza maso ake pa Yesu amene akukhala mkati mwa iye kulandira mau olankhulidwa ndi Mulungu, masomphenya pamodzi ndi katundu wa chiyanjano mwa Mzimu Woyera.

Ichi ndi chimene chimatimasula ku chilamulo cha uchimo ndi imfa. Halleluya!! Tsopano popeza ndikudzindikira choti ndichite, apa chofunika ndingochita pamene ndikuona chotdogozo cha Mzimu Woyera. Mwa ichi ndimagwiritsa ntchito nthawi yanga ku kulambira, kuyimba mwa mzimu, kupemphera mwa mzimu pamodzi ndi kutchera ku masomphanya pamodzi ndi kuyenda kwa mzimu. Ndimatakasa kuyenda kwa mzimu poyimba momasuka ku uzimu kuyimbira mfumu ya mafumu uku ndikuona masomphanya pamaso pake monga mtumwi Yohane adaona mpando wa chifumu wa Mulungu kumwamba. Apa nkosavuta kuona mphamvu ya Mulungu ikutakasika mkati mwa moyo wathu.

Pomaliza pa zonse, udzaona kuti ndili wopembedza wokhala mwa mzimu osati mwa thupi? Ichi ndi chimene aliyense wa ife ayenera kuchita.

KUSANTHULANSO MAFUNGULO ENA KUCHOKERA MU CHAPUTALA SEVENI.

- Pali njira ziwiri zoyesera kusunga chilamulo
- Imodzi ndi yochita mwa iwe wekha
- Yina ndi yochita kupyolera mwa Mzimu wa moyo mwa yesu Khristu.
- Chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa Khristu yesu chimakhala phata la Chikhristu ku chipangano chatsopano.

- Chilamulo ichi chiyenera kulalikiidwa nthawi zonse.
- Ngati chilamulo ichi sichilankhulidwa mosindika, mapeto ake tonse timabwerera ku chipemembedzo pembedzo.
- Chilamulo ichi chimatanthauzilidwa
- Malamulo anayi okolezetsa miyoyo yathu kupyolera mu mphamvu za Mzimu Woyera ndi awa:

A Kukhala mwa Mzimu

B Kupyonyerera pa Mzimu Woyera amene walumikizana ndi Mzimu wako

C Kukhala womasukira ku ulemerele wa Mzimu Woyera

D Kulankhula zimene Mzimu Woyera akuvumbulutsa

- Lembera fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBIRANA

- Ngakhale sitikhala mwa lamulo, kodi wachiyesa chilamulo kukhala chokuteteza kuti usagwe pamene walephera kukhala mwa mzimu?
Kambilanani umo ichi chimagwirira ntchito mu moyo wako. Perekani zitsanzo zake.
- Kodi ukugonjetsa zilakolako za thupi lako kupyolera mu kulimbana nazo wekha kapena poitana pa mphamvu ya Mzimu Woyera kuti igonjetse izo?
- Kodi udayamba wamvapo chiphunzitso china chofotokoza pamodzi ndi kutanthauzira za chilamulo cha Mzimu Woyera mwa Khristu Yesu? Ngati ndi chomwecho, kodi chidatanthauzilidwa bwanji? Chimagwira nthcito bwanji? Chimagwira ntchito bwanji? Chidagwira nthcito bwanji mu moyo wako kalero? Kodi ungate kupereka zitsanzo?
- Lembera tanthauzo la chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa Yesu Khristu mogwirizana ndi yankho la mkozi
- Kambilanani pamodzi umo wagwiritsila nthcito malamulo anayi operekeri mphamvu ku moyo wako kupyolera mwa Mzimu Woyera.
- **KULEMBERA-** “ Ambuye, lankhulani kwa ine za chilamulo cha Mzimu wa Moyu mwa Khristu yesu. Kodi ndakhala ndikuchigwiritsa

ntchito motani? Kodi ndakhala ndikuchilephera kuchigwiritsa ntchito motani?

KULEMBERA KWACHIWIRI- “ Ambuye, lankhulani kwa ine za malamulo operekera mphamvu moyo wanga kupyolera mwa mzimu Woyera kodi mukufuna kulankhula chiyani kukhudzana ndi kagwiritsidwe nthcito ka malamulo awa ku moyo wanga?

Lembera mu bukhu lako lapadera zimene Ambuye akulankhula kwa iwe ndipo konzekera kugawana ndi anthu mu kalasi. Monga mwa nthawi zonse, kukhoza kukhala kwabwino ngati ungawerenge izo walembe pa gulu la anthu.

CHAPUTALA CHA CHISANU NDI CHITATU CHOONADI # 7
NDIMAKHALA MWA CHIKHULUPILIRO KUTI MULUNGU ALI
EMMANUELI

Tsopano tayandikira ku mapeto. Apa tsopano takambilana mitu isanu ndi umodzi imene munthu ayenera kudzindikira kuti akathe kugonjetsa “munthu wakunja” ndi kukhala moyo wodabwitsa wa uzimu koma adakali mu chilengedwe chomwechi cha mthupi osakhalanso ndi kulimbana kochitika mu moyo mwake. Tapeza kuti Mulungu aliyense mu zonse komanso kuti ife tiri zotengera ndiponso kuti sitikhala ndi moyo mwa ife tokha koma kuti Yesu ali moyo wathu ndipo ife tiri akufa ku chilamulo ndi kuti tsopano ndi chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa Khristu Yesu chomwe chikutimasula ku chilamulo cha uchimo pamodzi ndi imfa. Izi ziyenera kukhala chomwecho! Pokhala ndi kumvetsa kotere, kumene kumafika kwa ine nthawi zonse pamene ndikulemba, tsopano tiri okonzeka kukhala moyo wa chikhristu wogonjetsa. Kodi palinso chotchinga china chilichonse chomwe chiyenera kugonjetsedwa? Inde, ndikuchita mantha kuti chilipo. Ndi vuto la kukaikira. “Ndinapachikidwa ndi Khristu koma ndiri ndi moyo wosatinso ine ayi koma Khristu ali ndi moyo umene ndiri nao tsopano mthupi ndiri nao m’chikhulupiliro cha Mwana wa Mulungu ameneanandikonda.....” (Agalatiya 2:20)..... kudzindikira zinthu zonse izi ndi mwa maphunziro ndi chinthu china ndipo ndi chinthu china cha padera kuika chikhulupiliro changa, chiyembekezo, pamodzi ndi chigomezero changa pa mphamvu zanga pamodzi ndi kuganiza kwanga. Chipangano chatsopano chimalankhula motere, “Ntchito ya Mulungu ndi kukhulupilira...” Kodi izi zili zoona?

Zikuoneka ngati kuti ntchito ya Mulungu ikadakhala yophweka kukadakhala kuti ili china chake osati kungokhala wokhulupilira nthawi zonse.

Ndikukhala mu dziko kapena mu mpingo umene siukhulupilira zokhala pa chiyanjano ndi Mzimu Woyera (11 Akorinto 13:14). Ena amaona ngati kuti ndili wopenga chifukwa choti ndimaona masomphenya pamodzi ndi kumva kulankhula kochokera ku dziko la uzimu nthawi zambiri. Nthawi zina ngakhaleso maganizo anga a ine amandiuza kuti ndili wopenga..... “Salidi masomphenya a Mulungu. Awo ndi maganizo ako chabe. Uko sikuli kulankhula kwa Mulungu. Awo ndi maganizo ako chabe oyendayenda mmutu mwako. Siumawakhulupilira, kodi umakhulupilira? Umatero kuti kuvumba mvula ndipo dziko lonse limizidwa mu chigumula? Zoonadi, uli wopenga! Ukutero kuti Mulungu adakuuza kuti umpereke mwana wako ngati nsembe. Kodi iwe ukufuna kuti tikakutsekere ku chipatala cha anthu a misala? Ukutero kuti Mulungu wakuuza kuti uyende ndi anthu ma milioni awiri mu chipululu ndipo iye awatsamalira modabwitsa? Inde, adachitadi koma ayi taumumvetsa bwino. Ukuteronso kuti tigwetsa linga la mzinda wa mphamvu pouyenderera chabe pamodzi ndi kuomba malipenga! Kodi ukuyembekezera kuti ndikhoza kukhulupilira zopusa zooterozo? Ine ndikukhala mu dziko lenileni sindikukhulupiliranso kuti zozizwitsa zikhoza kumachitika masiku ano.

Choonadi ndi chakuti chifukwa cha mchitidwe wotere, zozizwitsa sizingathe kuchitika mu dziko lanu.

..... “Ndipo iye chifukwa cha kusakhulupilira kwao sanachita kumeneko za mphamvu zambiri...”(Mateyu 13:58).....”

Yesu adalephera kuchita zozizwitsa kwao chifukwa cha kusakhulupilira kwawo ntchito ya Mulungu ndi kukhulupilira kusakhulupilira ndi tchimo. Kusakhulupilira kumatipangitsa kuti tisalowe mu dziko la lonjezano. Kusakhulupilira kumatsekereza kuti tisaone zimene Mulungu amatipatsa. Popanda chikhulupiliro sikutheka kusangalatsa Mulungu (Aheberi 11:6)

CHITSANZO CHA ANAA ISRAELI KULIMBANA NDI KUSAKHULUPIPILIRA.

Ngozi ya anthu amene adachita pangano lakale awa (Israeli) ndi yoti amalephera kukhulupilira ngakhale kuti amatha kuona zodabwitsa za mphamvu ya Mulungu pakati pawo Mulungu adati, “Chonde phunzirani ku

zolephera zawo. Chonde phunzirani kulumikiza chikhulupiliro ndi mau anga olankhulidwa kuti mukhoza kulowa mu mpumulo wanga” Tiyeni timve mau a Mulungu ndipo tiyeni tiphunzire zonse zidalembedwa chifukwa cha ife.

..... “ Adalangizanso tsiku lina ndi kunena m’davide, itapita nthawi yayikulu yakuti, lero monga kwanenedwa kale;

Lero ngati mudzamva mau ake musaumitse mitima yanu.

Pakuti ngati Yoswa akadawapumitsa iwo, sakadalankhula m’tsogolomo za tsiku lina. Momwemo utsalira mpumulo wa sabata wa kwa anthu a Mulungu.

Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake adapumulanso mwini wake ku ntchito zake monganzo Mulungu ku zake za Iye. Chifukwa chake ticite changu cha kulowa mpumulowo, kuti wina angagwe m’chitsanzo chomwe cha kusamvetsa.....” (Aheberi 4:7-11)

Mau amphamvu bwanji! “ Ambuye, tiloleni kuphunzira kukhulupilira inu powerenga zitsanzo zonse za zodabwitsa zanu pa nthawi zadutsazo. Tisakukhumudwitseni pamodzi ndi kukuchimwitsani posakhulupilira ubwino wanu pamodzi ndi kulakhula kwa mawu anu mu mitima yathu ndipo mmalo mwake kukhulupilira ntchito za manja athu pamodzi ndi maganizo athu. Tiloleni kuphunzira kukukhulupilirani inu Mulungu wa moyo. Mutikhulukire paliponse pamene talakwitsa. Mitiyeretse ndipi ili ndi pempho lathu. Tiloleni kuti tilowe mu mpumulo wanu. Lumbitsani mitima yathu. Tiloleni tikhulupilire pamodzi ndi kuchita ntchito zimene mumachita kuti dziko lapansi likathe kuona inu pakati pathu kupyolera mwa ife- thupi lanu. Tichilitseni ndipo tidzakhala a mphumphu. Tipatseni chisomo chanu ndipo tidzakhala olimba ndi amphamvu. Tipatseni chikhulupiliro chanu ndipo tidzakhulupilira chifukwa ndi inu amene mukugwira ntchito mwa ife ku chifuniro chanu”

NKHANI (MBIRI)

Ndakhala wodabwa pa nthawi yayitali kukhudzana ndi kusiyana kumene ndakhala ndikukuona pakati pa malonjezano a pa Deteronomo 28 ndi umo mpingo wa Yesu Khristu ulili mu dziko lapansi mmene tikukhala. Tiyeni tione madalitso a Mulungu olonjezedwa kuti adzafika pa ife ngati tichita mau ake mu chikhulupiliro.

“Ndipo kudzali mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu mwachangu ndi kusamalira kuchita malamulo ake onse ndi malemba ake amene ndikuuzani

lero kuti Yehova Mulungu wanu adzakukulitsani koposa a mitundu onse a dziko lapansi ndipo madalitso a wa onse adzakugwerani ndi kukupezani mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu.....” Deteronomo 28 : 1-2)

Wow, osati lonjezo loipa! Ili ndi lonjezo losakhulupilika kwa ine chifukwa ndimaganiza kuti pamene ndakhala mkhristu, apa ndiye kuti ndikhala munthu wosauka pa dziko lapansi. Mmalowake Mulungu akulonjeza anthu ake amene adachita nawo pangano kuti ngati iwo adzamvera mau ake iye adzawadalitsa kukhala anthu a chuma ndipo adzakhala mtundu wotsogola pa dziko lonse lapansi!

Kodi tikutha kuona umboni wa ichi kukwanilitsidwa mu nthawi yathu? Ndikuganiza chomwecho. Taonani dziko la Amerika pa ndalama yathu “ mwa Mulungu timakhulupilira” Pochita izi tidasanduka kukhala dziko lamphamvu kwa mbiri pa dziko lonse lolemera kuposa onse. Pali zambiri mu lonjezo la Mulungu.

..... Ndipo Yehova adzakuchulukitsirani zokoma, m’zipatso za zoweta zanu ndi mzipatso za nthaka yanu ndi m’ dziko limene Yehova analumbilira makolo anu kuti adzakupatsani ilo. Yehova adzakutsegulirani chuma chake chokoma ndicho thambo la kumwamba kupatsa dziko lanu mvula mnyengo ndi kudalitsa ntchito zonse Yehova adzakuyesani mutu osati mchira ayi....” (Deteronomo 28:11-13)

Kodi mukuganiza kuti izi zikufotokoza zimene Mulungu wachitira dziko la Amerika pa zaka zikwi ziwiri zadutsazo? Tabwereketsa ku mayiko ambiri (komanso ngakhale kwa adani athu) sitidangongole kufikira posachedwapa, taleka kutsatira mau a Mulungu ndipo malonjezano a Mulungu ayamba kuchoka ndipo tsopano tayamba kulowa mutemberelo la Mulungu lolembedwa pa Deteronomo 28

Ndikukhulupilira kuti malonjezano awa alipobe kwa anthu onse pamodzi ndi maiko onse pa dziko lapansi lero lino. Ndikukhulupilira kuti tikhoza kuunguza unguza ndi kuwaona lero lino. Koma chinthu chimene chikundiwawa ndi choti akhristu a ku Amerika Sali mutu. Nthawi zambiri ali angongola osati ongongoletsa. Kafukufuku akuonetsa kuti anthu ambiri owonetsa zinthu pa television Sali a khristu ayi. Ndikukhulupilira kuti ambiri a anthu a ndale Sali akhristu. Nchifukwa chiyani akhristu Sali atsogoleri ku

Amerika? Kodi malonjezano a Mulungu asiya kugwira ntchito mwa dzidzidzi? Kodi baibulo lasanduka labodza? Ayi sichoncho. Nanga vuto nchiyani? Kodi mpingo wa Mulungu wasiya kumvera mau a Mulungu kuti tsopano sitingathenso kuyenda mu madalitso ake olonjezedwa? Kodi tasiya kumvetsera ku kulankhula kwake pamodzi ndi kuyenda mu kumvera?

Pamene ndidali kung'ung'uza za anthu owonetsa ma television zaka ziwiri zadutsazo, Ambuye adalankhula mu mtima mwanga motere.....” Mariko ngati siukuwakonda bwanji osangophunzitsa m'bado wotsatirawo za umo angachitire ndi ma television? Ndidayesera kufotokozera Mulungu kuti sindidali kufuna kupita patsogolo; Ndimangofuna kungong'ung'uza pang'ono chabe. Apa ndidakumbutsidwa kuti Mulungu adapha anthu 14, 700 onse ong'ung'uza mu chipululu tsiku limodzi pamene adang'ung'uza pa tsiku lotsatira iye adapha oposa pa tsiku loyamba.

Ndayetsetsa pa moyo wanga kukhazikitsa lamulo kuti ndisakhale wong'ung'uza!

Mulungu sakufunafuna anthu oliralira koma anthu omvetsera ku chimene iye akulankhula ndi chikhulupilira chonga cha mwana wamng'ono – kuchita zimene walankhula pamodzi ndi kuziona. Kodi ine ndidzamukhulupilira iye kapena ndidzadalira pa mphamvu zanga kuti ndichite zinthu zotsogola? Kodi ndidzakhabe wokhulupilira? Kodi ndidzaphunzitsa m'bado wa patsogolo? Apa sindikutha kudzikira. Tidzayenera kudikira ndi kuona nkokwanira kupumuntha thupi langa mpaka ku imfa.

ZOYENERA KUTI UCHITE.....

Kodi udzakhala wokhulupilira? Kodi udzatha kutaya zikaikiro zako zonse ku dzenje la gehena kumene zimachokera ndi kukhala mu mphamvu ya Mulungu wa mphamvu yonse yolamulira moyo wako? Kodi udzakhala? Uyenera kuchita chisankho. Uyenera kusankha njira ya moyo, chikhulupilira, ndi chiyembekezo kapena njira ya mantha ndi chikhumudwits. Chisankho chili chako. Palibe angathe kukuchitira. Kodi chidzakhala chiyani? Lembera chisankho chako mu buku lako. Lembera kuti udzakhale nacho ngati umboni pa Mulungu. Zodabwitsa zidzakhala kwa iwo akukhulupilira. Lola kuti moyo wako ukhale wodzadzidwa!!

KUSANTHULANSO FUNDO ZA PA CHAPUTALA CHACHISANU

NDI CHITATU

- Mphamvu ya Mulungu pamodzi ndi chisomo zimafika kudzera mu chikhulupiliro.
- Ntchito ya Mulungu ndi kukhulupilira.
- Dziko lapansi lidazolowera kukaikira
- Ndimakonda kupenyenera pa malire anga pamodzi ndi kukaika.
- Chipembedzo chimakhulupilira kuti Mulungu samachitanso zodabwitsa
- Mulungu akufuna kutipanga ife kukhala mutu osati mchira.
- Mulungu akufuna ife kuti tidzitsogolera osati kutsatira.
- Mulungu akufuna ife kuti tizikongoletsa osati kubwereka.
- Kodi mpingo udzakhoza kudzuka ndi chikhulupiliro pamodzi ndi kulola Mulungu kuti audzadze?
- Kodi iwe udzatero?
- Mu zolemba zako, lembera fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBIRANA

- Lembera malonjezano aakuru a Mulungu amene wakupatsa pa moyo wako. Kodindi zinthu zina ziti zimene akufuna kuchita kupyolera mwa iwe? Kodi zili zopyola mphamvu zako? Kodi izi zili ndi kanthu kwa iwe? Kodi Mulungu akwanilitsa izi kupyolera mu mphamvu zako kapena zake?
- Kodi ukusungabe maloto Mulungu waika mwa iwe mu mtima mwako? Kodi ukutha kuwapereka pamaso pa Mulungu kuti uone zimene iye akufuna kuti uchite tsiku ndi tsiku kukwanilitsa maloto awa? Kodi ukuchita zimene iye wakulamulira?
- Kodi ukuphatikiza chikhulupiliro ku malonjezano a Mulungu amene wakupatsa? Kodi ukukhulupilira kuti akhoza ndipo akwanilitsa izo ngati ungayende pamodzi ndi kumvera mau ake?
- Kodi uli wong'ung'uza kapena wokhulupilira? Mwina ukhoza kufuna kupereka pemphero la kulapa kuti ulandire machilitso pamodzi ndi kubwezeretsedwanso kulapa ndi maziko a kusintha. Pamene ndikung'ung'uza, kodi ndikulankhula chiyani kukhudzana ndi mphamvu ya Mulungu yolamulira? Kodi ukuona kuti iye amamva bwanji mu mtima mwake za ichi? Kodi anthu

ong'ung'uza amalabadira za mphamvu yodabwitsa ya Mulungu?
Kodi ukuganiza bwanji?

- Mulungu adakwiya ndi Mose chifukwa choti adali kumangomufotokozera iye kuti adali wa chibwibwi ndipo pa chifukwa cha icho sakadakhoza kugwira nthcito ya Mulungu. Pamene Mose amadandaula, kodi adali kulabadira za mphamvu yodabwitsa ya Mulungu? Kodi Mulungu amayembekezera kuti Mose agwira nthcitoyo ndi mphamvu zake kapena mphamvu za Mulungu? Pamene Mulungu wakupatsa ntchito kuti agwire pa dziko lino lapansi, Kodi iye akuyembekezera kuti uyigwira ndi mphamvu zake kapena ndi mphamvu za Mulungu? Kodi umadzipenyera kwa iwe wekha kutu ukwanilitse masomphenya a Mulungu pa moyo wako kapena umapenyera kwa Mulungu?
- Mchifukwa chiyani akhristu sakutsogolera mu dziko lathu lero lino? Kodi tiyenera kukhala otero? Kodi chingachitike ndi chiyani kuti izi zisinthe? Kodi udzakhala mbali imodzi ya kusinthako? Kodi udzakhala kapolo kwa Mulungu mu njira iliyonse akukupempha kuti ukhale? Gawana kudzipereka kwako ku masomphenya amene Mulungu waika mu mtima mwako ndi anthu ena pa gulu lako. Kenako yamba kulembera za ichi tsiku ndi tsiku kumulola Mulungu kukutsogolera sitepe iliyonse ku kukwanilitisa.
- **KULEMBERA**- “Ambuye, lankhulani kwa ine kukhudzana ndi masomphenya anu pa moyo wanga. Kodi mukufuna ine kuti ndichite chiyani? Kodi ndiyenera kuchita chiyani lero? Kodi masomphenya anu ndi otani pa dziko langa lino? Zikomo kwambiri pa zimene mwandivumbulutsira...” Fika wokonzeka kugawana ndi gulu lako kuchokera mu zolembera zako.

CHAPUTALA CHA CHISANU NDI CHINAYI, - KUKHALA MWACHINGEGWE KOMA MWA UZIMU.

Topano tiri ndi madera onse ofunikira kuwalakika pa munthu wakale kuti tsopano tikakhale mwa uzimu komabe tiri a thupi mwa chilengedwe kuonetsera moyo wodabwitsa wa uzimu pamodzi ndi mphamvu komanso

mtendere wa mkati pamodzi ndi mpumulo wa uzimu.

Tsopano tafika ku mapeto a buku lathu ngakhale kuti sitiyima apa. Ayi, ndipitilizabe kubwerezabwereza choonadi ichi mumachaputala otsatirawo. Ndili wokopeka mtima kuti sitingathe kuyenda muvumbulutso la choonadi ili kufikira titakhala ndi kumvetsa kwabwino. Zaka zapitazo, pamene ndidapeza buku lodzala ndi choonadi mkati mwake, ndidawerenga buku lonse katatu. Ndimadziwa kuti ndimafuna kukhala mu zimene bukulo limafotokoza. Sichinthu chabwino kusayenda mu choonadi chovumbulutsidwa kwa iwe. Ndandanda wa mabuku ena okamba za choonadi chomwechi ukupezeka kumapeto kwa buku ili.

CHOONADI CHISANU NDI CHIWIRI CHOKULOLA KUTI ULUMIKIZANE NDI ULEMERELO WA MULUNGU.

Choonadi #	1	Mulungu aliyense mu zonse
Choonadi #	2	Ndine chotengera
Choonadi #	3	Sindilinso ndi moyo
Choonadi #	4	Ndafa ku chilamulo
Choonadi #	5	Khristu Yesu ali moyo wanga
Choonadi #	6	Ndimakhala mwa Mzimu (mmasomphenya pamodzi ndi kulankhula kwa Ambuye).
Choonadi # 7		Ndimakhala mwa chikhulupiliro kuti Mulungu ali Emmanueli.

CHOONADI CHISANU NDI CHIWIRI ICHI CHIMAGWIRITSIDWA NTCHITO KUGONJETA YESERO.

Tsopano tiyeni tisonkhanitse pamodzi choonadi chisanu ndi chiwiri ndipo tione

umochimagwirira ntchito.

Pamene wakomana ndi yesero pa moyo wako. Zikadakhala bwino kukadakhala

kuti padalibe mayesero popeza tsopano tiri akhristu koma izi sizili chomwecho ayi. Pali njira yogonjetdera mayesero. Khristu aliyense amakomana ndi mayesero. Njira yowagonjetsera mayesero. Khristu aliyense amakomana ndi mayesero. Njira yowagonjetsera adaionetsa kale Yesu amene adayetsedwa ngakhale kuti adalibe tchimo lili lonse (Aheberi 4: 15)

UMO UNGALOLERE ZINTHU KUCHITIKA

Ndakhala ndikuuzidwa nthawi zambiri kulola zinthu kuchitika ndi kumulola Mulungu kuti zitero- koma ndimalephera kuti zoterozo zikhoza kuchitika motani. Mwa chitsanzo. Munthu akupanda khofi pa saya. Nthawi yomweyo thupi lako limafuna kubwezera koma umadzakumbukira mau a mu Baibulo olankhula motere;

..... “ Koma ndinena kwa inu, musakanize munthu woipa koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lako la manja, umtembenezire linaso.....”
(Mateyu 5:39).....”

Oh, Ndiyeneradi kumukonda iye! Mwa ichi ndimayesera, nkuyesera nkuyera. Komabe ngakhale ndimayesera, pansa pa mtima ndimafuna kumubwezera. Apa ndimakumbukira munthu wakunja wa pa Aroma 7:19 pamene ndimachita cholakwika chimene sindifuna kuchita. Ndimapeza ndekha ndi kusunga mkwiyo pa munthuyo ngakhale ndikuyesera kuti ndimukonde pamodzi ndi kumukhululukira. Kenako ndimakumbukira pa Agalatiya 3:3 pamene akulankhula motere;

..... “ Kodi muli opusa otere? Popeza munayamba ndi mzimu , kodi tsopano mutsiliza ndi thupi?.....”

Ndikudziwapo kanthu kena kokhudzana ndi ichi! Ndidapulumsidwa , osati ndi kuyetsesa kwanga koma ndi ntchito ya Mzimu Woyera. Kodi tsopano ndikuganiza kuti ndikhoza kuzipanga kukhala wangwiro mwa mphamvu za ine ndekha osati koma mwa mphamvu za Mzimu Woyera? Chisoni chifukwa cha kupusa kwanga. Ndi kulapa....!!

Tsopano ndapeza chinthu ichi;

..... “ Sichinakugwereni inu chiyeso koma cha umunthu koma Mulungu ali wokhulupilika amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanzo populumukirapo kuti mudzakhoza kupilirako.

(1 Akorinto 10:13).....”

..... “ Ambuye, mwapereka njira yopulumukirapo ndipo ndikukumbukira njirayo”

..... “ Ndinapachikidwa ndi Khristu koma ndiri ndi moyo wosatinso ine ai koma Khristu ali ndi moyo mwa ine koma moyo umene ndiri nawo tsopano m’thupi ndiri nao m’chikhulupiliro cha mwana wa Mulungu amene anandikonda ndidzipereka Yesu”

Agalatiya 2:20)

..... Tsopano mwalowetsa mmalo mwa ine Yesu, mwa ichi tsopano ndi moyo wa Yesu mwa ine osati inenso.....”

..... “ Yesu ameneyo chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pamaso pake anapilira mtanda nanyoza manyazi.....” (Aheberi 12: 2..... “ Yesu Ambuye Yesu ndikudza kwa inu. Ndikweza maso anga pa inu. Chonde ndipatseni masomphenya a kakonzedwe ka vuto ili”

..... “Mwana wanga, kumbukira pamene adani anga adandiukira kopanda chifukwa,..... komanso kundipachika pa mtanda wamaliseche. Kumbukira umo ndidagwetsa nkhope yanga pa mtanda ndi kulankhula motere Atate akhululukireni pakuti sakudzindikira chimene akuchita” Iwensu mwana wanga, waukitsidwa kopanda chifukwa pamodzi ndi kuchepetsedwa pa gulu koma chikondi changa chikuyenda mu mtima mwako kukhulukira adani ako. Uzione wekha monga wapachikidwa pa mtanda kubwerezanso mawu anga kwa anthu okuukirawo ndi kulankhula nawo. Ona chikondi changa choyenderera mwa iwe ndipo udzakhala wamphumphu-ona ichi mwana wanga.....”

“Inde Mbuye wanga, ndikuona chikondi chanu kuyenda mwa ine kwa iwo ondiukira ine ndikundidzudza mopanda chifukwa ndipo ndikupachikidwa nanu pa mtanda pamodzi ndi kulankhula mau omwewo, “ Atate muwakhulukire pakuti sakudzindikira chimene akuchita”

Umu ndimo ziyenera kukhalira. Kalikonse talankhula mu bukuli kakhoza kupherezedwa mwa chidule mu nkhani yomaliza iyi. Kodi udatsatira mbali zonse? Izi zidali;

- | | |
|-----|--|
| (1) | Ndimona kupweteka |
| (2) | Ndimona kulamulidwa umo ndingayankhire |
| (3) | Ndimayesera kumvera kulamulidwako ndipo ndimadzindikira kuti sindingachite izo |
| (4) | Ndimakumbukira osayesera mwa thupi koma kutsatira |

- (5) chitsogozo cha Mzimu Woyera
Ndimakumbukira kuti pali njira
ya kupulumukirapo kupyolera
mwa khristu Yesu
- (6) Ndimakumbukira kuti ali mwa
ine mmalo mwa umunthu
wanga
- (7) Ndimakweza maso anga pa
Yesu ndi kuti andiyankhe
- (8) Iye amayankha ndi
masomphenya pamodzi ndi
kulankhula kwa mau ake
(rhema) komanso mphamvu
- (9) Ndimalankhula zimene
wandiuzza kuti ndilankhule
pamodzi ndi kuona mphamvu
yake ikuyamba kuyenderera mu
mtima mwanga.
- (10) Ndimayamba kulambira.

Nhoodziwika bwino kuti siuyamba kuyesera mu njira yolakwika popita ku chilamulo poyamba ndi mphamvu za iwe wekha. Umayamba kwa mzimu – mkulankhula “ Ambuye, ndapweteka. Mungathe kundilankhula pamodzi ndi kundichilitsa? “ Mu njira yotere, apa ndiye kuti ukudumpha sitepe 2-6 ndipo ukuchokera ku sitepe 1-7. Ngati chisomo cha Mulungu chikulola kudumpha chilamulo ndi kupita mwa tchutchutchu ku Mzimu Woyera, iyo ikhoza kukhala njire yabwino.

CHITSANZO

Ndiloleni kulankhula motere kwa inu; Popeza Yesu ali kuunika kwa dziko lapansi ndipo tchimo limaimilidwa ngati mdima, tidzalola kuti Yesu aimilire kuunika ndipo yesero langa liimilire mdima. Kodi mdima mumaugonjetsa bwanji? Poukankha kunja kodi? Ayi. Koma umo ndimo ambiri a ife timachitira ndi tchimo mu miyoyo yathu. Timalimbana nalo kuliturutsa kunja. Misala yotani! Utandiona ndili mkati mwa chipinda ndikuthamangitsa mdima, ukhoza kunditengera ku chipatala cha anthu a misala!

Mmalo mwake, ife kuti tiyatse kuunika. Motani? Pofika kwa Mulungu amene amakhala mu mitima yathu ndi kumupempha kuti adzivumbulutse kwa ife pakati pathu. Kodi mau ake ali otani? Kodi masomphenya ake ali otani? Yesu anati, “ Mau (rhema) ndalankhula kwa inu ali Mzimu ndi Moyo” (Yohane 6:63) Ndi mau ake pamodzi ndi masomphenya, tsopano pamabwera kuyenda kwa Mzimu wa moyo umene umakumasula ku chilamulo cha uchimo ndi imfa, komanso kukulola kukhala moyo wa uzimu wolumikizana ndi ulemerele wa Mulungu.

CHITSANZO CHINA

Mmalo molankhula motere, “ Ambuye, ndikuyesera kumukonda munthuyo, chonde ndithandizeni” Udzalankhula motere, “ Mulungu sindingathe kumukonda munthuyo koma inu mukhoza kutero. Inu muli phata la chikondi chonse pa dziko lonse lapansi ndipo mumakhala mwa ine. Ndi kukupemphani kuti muyende mkati mwa ine ndipo ndimukonde munthuyo ndi chikondi chanu cha uzimu.

..... Ukweze maso ako pa masomphenya a Yesu pamene adakonda adani ake pa nthawi imene adali pa mtanda ndipo pamene ukuchita motere, chikondi cha uzimu chidzayenderera mkati mwako kupereka mphamvu kwa munthu wa mkati mwako. Halleluya!! Apa udzayamba kulambira pamene chikondi cha Mulungu chikuyenderera mwa iwe. Zoonadi, Chikhristu ndi cha uzimu.

KUSANTHULANSO FUNDO ZA PA CHAPUTALA CHA CHISANU NDI CHINAYI

- Fundo zisanu ndi ziwiri izi mu machita chita
- Lembera fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Santhulanso za yesero lomwe wakomana nalo sabata yatha. Kodi udathana nalo bwnaji? Fananizitsa umo udathana nalo ndi masitepe khumi opezeka mu chaputala ichi. Ndi masitepe angati mwa awa amene udayendamo? Kodi ukhoza kufotokoza iliyonse payokha? Kodi udakomanapo pakati pa ndi yesero ndipo unadumphama masitepe awiri kufikira la chisanu ndi lomodzi ndipo

kenako kuchokera pa loyamba mpaka la chisanu ndi chiwiri? Ugawane izi ndi gulu lako. Khalani pa mphwando la chisomo cha Mulungu choonetsedwa pakati panu.

- Kodi ukufuna kuyesera kuthamangitsa mdima mmoyo mwako mwa iwe wekha kapena ukufuna kupenyera pa kuunika? Fotokoza mwa tchutchuchu zimene ukuchita. Gawanani zotsatira zake. Chinachitika nchiyani?
- **KULEMBERA** “ Ambuye kodi mukufuna kulankhula chiyani kwa ine za njira imene ndingathane ndi mayesero anga? “ Lembera zimene akulankhula pa buku lako lapadera. Konzekera kugawana ndi anthu pa gulu lako.

CHAPUTALACHAKHUMI
ZITSANZO ZAANTHU MU BAIBULO AMENE ADAPHUNZIRA
MAPHUNZIRO AWA.

- Baibulo lili lodzadza ndi mbiri ya miyoyo ya anthu amene adafika kwa Mulungu ndipo adadutsa kupyolera mu maphunziro omwewo takambilana mu buku ili. Izi nthawi zonse zimathandiza kuona munthu akudutsa motere. Wotere amazakhala mlangizi wako kukuonetsera kumene ukupita komanso pamene uyenera kuimapo ndi mapazi ako awiri. Tiyeni tione mbiri za miyoyo ya ena mwa anthu awa – awiri ku chipangano cha kale ndipo awiri ku chipangano chatsopano. Awa ndi Abraham, Mose Petro ndi Paulo!

ABRAHAMU ADAPHUNZIRA KUKHULUPILIRA MULUNGU OSATI
MPHAMVU ZAKE (GENESIS 12-23)

Nkhani ya mbiri ya moyo wa Abraham ili pa Genesis 12 pamene akufotokoza maitanidwe ake motere “ Ndipo Yehova anati kwa Abram Tanka iwe mdziko lako ndi kwa abale ako ndi ku nyumba ya atate wako kunka ku dziko limene ndidzakusonyeza iwe mtundu waukuru ndipo ndidzakudalitsa iwe ndi kubukitsa dzina lako nukhale iwe mdalitso ndipo ndidzadalitsa

amene akudalitsa iwe ndi kutemberera iye amene akutemberera iwe ndipo mwa iwe adzadalitsika mabanja onse (Genesis 12:1-4).....”

Ambuye adalankhula kwa Abrahamu ndipo Abrahamu adamvera. Apa zikuonetsa kuti adali wotsatira pamodzi ndi womvera Mulungu malingana ndi kuona kwanga. Akadakhala kuti ali mu nthawi ya chipangano chatsopano, tikadamutcha kuti “ wopulumutsidwa” koma popeza adali kukhala mu nthawi ya chipangano chakale Yesu asadapereke moyo wake pa mtanda, apa tikhoza kumutcha munthu wa Mulungu chabe.

Abrahamu tsopano ali wotsatira wa Mulungu. Kodi waphunzira kuti Mulungu aliyense mu zonse komanso kuti iye ali chotengera chabe mmene Mulungu amakhalamo kugwira ntchito yake kapena kodi akudalirabe pa mphamvu zake kuti akachite ntchito ya Mulungu? Tiyeni tione.

..... “ Ndipo munali njala m’ dzikomo ndipo anatsikira Abrahamu ku Aigupto kukakhala kumeneko chifukwa kuti njala inali yaikuru m’ dziko m’ menemo. Ndipo panali pamene anayandikira kulowa m’ Augupto anati kwa Sara mkazi wake, Taonani ndidziwa kuti ndiwe mkazi wokongola maonekedwe ako- ndipo padzakhala pamene adzakuona iwe Aigupto adzati, uyu ndi mkazi wake ndipo adzandipha ine koma iwe adzakuleka ndi moyo. Uzikanenatu kuti iwe ndiwe mlongo wanga kuti chidzakhala chabwino ndi ine chifukwa cha iwe ndi kuti moyo wanga usungike ndi iwe. Ndipo panali pamene Abrahamu analowa m’ Augupto, Aigupto anaona kuti mkazi anali wokongola kwambiri. Ndipo..... ake a Farao anamuona iye, namyamikira iye kwa Farao ndipo anamuka ndi mkazi kunyumba kwake kwa Farao.....” (Genesis 12:10-16).....”

Abrahamu adalephera yesero lake loyamba. Ngakhale kuti adali kuti atchedwe “Tate wa chikhulupiliro”, apa adayamba ndi kulephera mu chikhulupiliro chake pa kukhulupilira maganizo ake. Adali ndi mantha aakulu kuti Mulungu alephera kumuteteza kotero kuti adamuka kamiza mkazi wake kulankhula bodza ponena kuti sadali mkazi wa Abraham. Ichi sichili chikhulupiliro chachikuru monga ndi kuonera. Apazikungoonetsa kuti adali asadakule mu chikhulupiliro uko kudali kuyamba chabe kwa nkhani iyi. Kenako Mulungu adalankhula kwa Abrahamu motere

..... “ Ndipo anamturutsa iye kunja nati, Tayang’ anatu kumwamba uwerenge nyenyezi ngati ukhoza kuziwerenga zimenezo ndipo anati kwa iye” Zoteroto zidzakhala mbeu zako. Ndipo anakhulupilira Yehova

ndipo kunayesedwa kwa iye chilungamo.....”

(Genesis 15:5-6)”

Apa tsopano zikuonetsa kuti Abrahamu adayamba kukula mu chikhulupiliro cha Mulungu wamphamvu yonse. Mulungu sikuti wangomupatsa (rhema) mau olankhulidwa) komanso kuti waphatikizirapo masomphenya – ndipo pakutero chikhulupiliro cha Abrahamu chadzamitsidwa. Tsopano tikhoza kuona zotsatira zake zabwino. Patapita zaka khumi ndi chimodzi zodikiriz pa Ambuye kuti akwanilitse mau ake, Abrahamu adayamba kumvetsera ku njira zina zothandizira kukwanilitsa mau a Mulungu kuti achitike. Kodi izi sizikuoneka ngati zimene iwenso udachitapo?

..... “Ndipo Sarai mkazi wake wa Abrahamu sanam’balire iye mwana ndipo anali ndi mdzakazi wa ku Aigupto dzina lake Hagara. Ndipo Sarai anati kwa Abrahamu, Taonanitu Yehova anandiletsa ine kuti ndisabale lowanitu kwa mdzakazi.....”

(Genesisi 16:1-2)

Hagara adakhala ndi pakati ndipo adabereka mwana wamamuna yemwe naye adali ndi mphamvu ya kubereka. Zikuonetsa kuti munthu akhoza kuthandiza Mulungu pamene akuchedwetsa kukwanilitsa mau ake. Nthawi zambiri takhala ndi mwana wamamuna wokula nsinkhu kupyolera mwa iye. *Khristu adzabadwe. Tamvetserani ku mau otsatira kwa Abrahamu

..... “Pamene Abramam anali wa zaka makumi asanu ndi ani kudza zisanu ndi zinayi, Yehova anamuonekera Abramam nati kwa iye, Ine ndine Mulungu wamphamvu yonse, yenda iwe pamaso panga nukhale wangwiro” (Genesisi 17:1)

Mwa njira yina akulankhula motere, “Yenda pamaso panga ndipo usiye kuchita machimo” Ouch!! Kodi zidali zoipa motere Mulungu? Ndimandokuthandizani kukwanilitsa mau anu. Kodi simungathe kulandira chimene ndakuchitirani? Tamvetserani ku dandaulo la Abrahamu.

..... “Ndipo Abrahamu anati kwa Mulungu, Ha! Ishmayeli akhale ndi moyo pamaso panu! Ndipo Mulungu anati koma Sara mkazi wako adzakubalire iwe mwana wamwamuna ndipo udmutchi dzina lake Isaki ndipo ndidzalimbikitsa naye pangano langa kuti likhale pangano la nthawi zonse (Genesis 17:18)”

Awa ndi mau oswa mtima. Ndayesetsa kukwanilitsa masomphanya amene

Mulungu adandipatsa ndipo tsopano ndikuona kuti sakulandira zimene ndachita. Iyi ndi nthawi yoti ndikhoza kubwerera m’mbuyo ndi kulankhula motere, ndipo anakhala ngati mlendo mGerari,. Ndipo Abrahamu anati kwa Sara mkazi wake, Iye ndiye mlongo wanga ndipo Abimeleke mfumu ya Gerari anatumiza namtenga sara.”

Zikuonetsa kuti tathana ndi tchimo ili kale. Abrahamu akulepherabe kukhulupilira Mulungu kuti amusunga iye. Mmallo mwake, akukhulupilira mapulani ake. Mukuona, pamatenga nthawi kuti munthu akhale wamphamvu mu chikhulupiliro pamodzi ndi kugonjetsa zofooka za umunthu wathu. Sizingochitika nthawi imodzi.

Mulungu amapereka yesero ndi yesero pa moyo wathu kufikira tikaphunzira kumukhulupilira Iye. Pomaliza pake, Abrahamu adakhala ndi mwana pamene iye adali ndi zaka zana limodzi. Apa zikuonetsa kuti padatenga zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu (25) atachoka mu dziko la Harani.

..... “ Ndipo Sara anatenga pakati nam’balira Abrahamu mukalamba wake mwana wamamuna nthawi yomweyo Mulungu adamuza iye.....” (Genesis 21:2)

..... “ Ndipo Abrahamu anali wa zaka zana limodzi pamene anambadwira Isake mwana wake.....” (Genesis 21:5)

Phunziro lomwe ndaphunzira apa ndi loti Mulungu amatenga nthawi yaitali kusiyana ndi umo ndingachitire ine. Ndisowa kukhala ndi chipiliro. Atatha kulandira mwana wolonjezedwayo pamodzi ndi mphatso ya chisomo, tsopano tionanso za yesero lomaliza. Apa tiona ngati Abrahamu adaphunzira kukhulupilira mu mphamvu ya Mulungu wamphamvu zonse kapena akukhulupilirabe mu mphamvu za iye yekha. Tidzaonanso ngati Abrahamu adzamamatira mphatso yomwe Mulungu adampatsa kapena adzampatsa kapena adzamamatira pa Mulungu pamene Mulungu watipatsa mphatso, nkosavuta kuumilira mphatsoyo mmalo moulilira pa Mulungu.

..... “ Ndipo panali zitapita zimenezo Mulungu anamuyesa Abrahamu nati kwa iye, Abrahamu ndipo anati, “Ndine pano” Ndipo anati tengatu mwana wako wamwamuna wa yekhayo Isaki amene ukondana naye numuika ku dziko la Moriya numpereke iye kumeneko nsembe yopsyereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuza iwe. Ndipo Abrahamu analawira

mmamawa namanga buru wake natengako anyamata ake aiwiri pamodzi naye ndi Isaki mwana wake.....

Vesi 9- Ndipo anafika ku malo komwe Mulungu anamuza iye ndipo Abrahamu anamanga guwa la nsembe nakonza nkhu ni namanga Isaki mwana wake namuika iye pa guwa la nsembe pamwamba pa bkhuni.
..... (Genesisi 22:1-10)

Nkhani yosangalatsa kwambiri! Kodi ukutha kuona tsopano mweso wa chikhulupiliro wa Abrahamu? Kodi amaganiza chiyani pamene amaika mwana wake pa guwa la nsembe monga nsembe kwa Ambuye? Buku la Aheberi likutifotokoza motere:

..... “ Ndi chikhulupiliro Abrahamu poyesedwa anapereka nsembe Isake ndipo iye amene adalandira malonjezano anapereka mwana wake wa yekha amene kumanenedwa za iye kuti, “ mwa Isake mbeu yako idzayitanidwa” poyesera iye kuti Mulungu ngokhoza kuukitsa ngakhale akufa” (Aheberi 11:17-19).

Abrahamu amakhulupilira kuti Mulungu akhoza kumuukitsa kwa akufa mwana wake. Apa tsopano tikhoza kuona kuti Abrahamu adasanduka kukhala munthu wamphamvu mu chikhulupiliro amene sadalinsoko kukhulupilira pa mphamvu zake za thupi koma pa mphamvu za Mulungu wamphamvu yonse. Tsopano wakhala munthu amene akukhala monga mwa kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu wamphamvu yonse. Tiyeni tiyende mu mapazi ake!

MOSE APHUNZIRA KUKHULUPILIRA MULUNGU OSATI MPHAMVU ZA IYE YEKHA (EKISODO 1-7)

Nkhani ya Mose yayamba pa Ekisodo 2:10 pamene akulankhula motere, “ Ndipo atakula mwanayo anapita naye kwa mwana wa mkazi wa Farao ndipo iye anakhala mwana wake ndipo anamutcha dzina lake Mose nati “ chifuke ndinamvuula mmadzi..... “ Ekisodo 2:10.....”

..... “ Ndichikhulupiliro, Mose atakula msinkhu anakana kutchidwa mwana wake wa mwana wa mkazi wa Farao nasankhula kuchitidwa zoipa pamodzi ndi anthu a Mulungu kosati kukhala nazo zokondweretsa za zoipa kanthawi. (Aheberi 11:24-26).

Tikuona kuti ngakhale Moses adakula ali ku nyumba ya chifumu ya Farao, iye adasankha kukhala wotsatira wa Mulungu wamphamvu yonse mpaka kuvomereza mazunzo onse. Izi zikuonetseratu kuti adali monga Khristu wa ku chipangano chakale. Ngakhale adataya zonse chifukwa cha Mulungu, kodi adayenera kuphunzira kukhulupilira Mulungu kuti akhoza kumachita zonse? Tiyeni tione.

..... “ Ndipo kunali masiku amenewo atakula Mose kuti anaturukira kukazonda abale ake napenya akatundu awo ndipo anaona munthu Mhebri wa abale ake. Ndipo anaunguza kwina ndi kwina ndipo pamene anaona kuti palibe munthu, anakantha Maigupto namfotsera mu mchenga. Mmawa mwake anaturukanso ndipo taonani anthu awiri Aheberi ali kugwirana ndipo ananena ndi wochimwayo, kuti umpandiranji mnzako? Koma anati “ wakuyika iwe ndani ukhale mkuru ndi woweruza wathu? (Ekisodo 2:11-14)

Popeza Mose adaona kuti ali mombolo wa anthu ake, adagwiritsa ntchito njira zimene iye amadzindikira kuti akhoza kukwanilitsa cholinga ichi – njira ya lupanga. Izi zimene zidali mu maganizo a Mulungu pamene adamusankha Mose kukhala mombolo wa Ayuda a mndende. Mulungu amafuna kuchita ntchito iyi mwa mphamvu yake yodabwitsa, kuti dziko likadzindikire kuti iye ali pakati pa ana a Israeli. Kodi ukuganiza kuti Mulungu akufuna kuchita zomwezo ku m’bado uno? Tiyeni titsatire nkhaniyo mwa tchutchutchu.

..... “ Pamene Farao anachimva ichi, anafuna kupha Mose. Koma Mose anathawa pa nkhope pa Farao nakhala m’dziko la Midyani nakhala pansu pa chitsime..... (ekisodo 2:15)

Mphamvu za Mose zalephera apa. Mphamvu zake zapasuka ndipo tsopano akuthawa kuchita mantha. Apa sangakhale mombolo. Ali chabe. Tsopano apita ku malo a yekha ku chipululu malo kumene Mulungu amakonda kutengerako anthu amene Iye akufuna kuwasula kuti awagwiritse ntchito ku chifuniro chake. Kodi Mose akufuna kupita kapena akufuna kuzemba? Tamvetserani apa

..... “Ndipo Mose anavomera kukhala naye munthuyo ndipo anampatsa Mose mwana wake wamkazi zipora.....” (kisodo 2:21)

Pamene Mulungu watitengera ku malo otere- kunenetsa ngati kuti kulephera kwathu, pamakhala zinthu ziwiri monga mwa kuyankha kwathu. Timakhoza kutsutsana naye kapena timakhoza kulola kuti tione chimene Mulungu akufuna kutionetsa. Mose adapita ndi mtima wake wonse wofuna kuteru, ndipo ali ku chipululu, Mulungu adamuonetsa ulemerele wake.

..... Ndipo mnthenga wa Mulungu anamuonekera m’chirangali chamoto choturuka moto koma chosanyeka chitsambacho. Ndipo Mose anati, ndipatuketu ndikaone chooneka chachikurucho chitsamba sichinyeka bwanji? Pamene Yehova anaona kuti adapatuka kukapenya, Mulungu ali mkati mwa chisamba, anamuitana nati, Mose, Mose. Ndipo anati, “Ndiri pano” ndipo iye anati, usayandikire kuno, bvula nsapato zako kumapazi ako pakuti pa malo pamene upondapo iwe mpopatulika. Ananenanso, Ine ndine Mulungu wa atate wako, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isaki ndi Mulungu wa Yakobo. Ndipo Mose anabisa nkhope yake popeza anaopa kuyangana Mulungu. Ndipo Yehova anati, (Ekisodo 4:17.....” Ndipo ukagwire m’dzanja lako ndodo iyi imene ukachite nayo zizindikiro.....” chinthu chodabwitsa bwanji! Munthu wekha ku chipululu – apa ndi pamene nthawi zonse timapeza mphamvu ya Mulungu. Mose adalandira vumbulutso la Mulungu kumeneko chomodzimodzi monga Paulo, komanso ngakhale Yesu adayambira utumiki wake wodabwitsa atatha kukhala masiku makumi anayi, ku chipululu. Kodi kumutsatira Mulungu ku chipululu ngati Iye angathe kukutsogolera kumeneko? Taonani kunyinyirika kwa Mose kuti agwiritsidwe ntchito mwa mphamvu ndi Mulungu. Mose akupenyererabe pa zofooka zake, kulephera kwake kulankhula mwachangu, komanso kusowa kwa zomuyenera monga mtumiki wa Mulungu. Mulungu adakwiya naye chifukwa choti sadavomereze kuti zikhala zotheke kuti Mulungu alankhule kupyolera mwa iye ndi kukhala cholankhuliramo chake Mulungu safuna ife kumulemba malire. Ngati tikukhala monga mwa Mzimu wake pamodzi ndi mphamvu yake komanso mneru zake, sitikhalanso ndi malire koposa kudalira pa Mulungu kotheratu. Mulungu akufuna kudzutsa anthu amene akhoza mumvetsera kulankhula kwake pamodzi ndi masomphenya komanso mnzeru zake ndi kumachita zokhazo zimene Iye akulamulira ndipo kudzera mwa

anthu otere, Mulungu asanduliza miyoyo ya anthu okhala pa dziko lapansi. Chomwe Iye akusowa ndi anthu basi. Kodi ukhoza kukhala mmodzi wa anthu otere ophunzira kumva kulankhula kwa Mulungu komanso kumaona masomphenya osadalira pa luntha lathu koma mu zonse kumutsatira Iye? Ngati ndi chomwecho Mulungu adzakugwiritsani ntchito kukasintha miyoyo ya anthu pa dziko lapansi. Iye sakufuna anthu a mnzeru za thupi kapena a mphamvu. Iye akusowa anthu omwe angakhale moyo wa uzimu monga Yesu amachitira. Awa ndi anthu amene amasintha dziko mmene iwo akukhala.

Tsopano taonani zimene Mulungu adachita kwa Mose.

..... “ Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Taona ndakuika ngati Mulungu kwa Farao ndi Aaroni mkuru wako adzakhala mneneri wako. (Ekiyodo 7:1)

Liu loti “ Monga” silili mu buku ili “ Ndakupanga kukhala Mulungu kwa Farao....” Pamene tikumasula mphamvu yodabwitsa ya Mulungu kupyolera mu miyoyo yathu, timaoneka ngati Mulungu ku dziko lapansi. Ku chipangano chatsopano tikutchedwa “ thupi la Yesu”. Tsopano Mose ali mombolo wodabwitsa osakhulupiliranso mphamvu za iye yekha kugonjetsa adani koma kudalira pa kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mmoyo mwake kupereka chiombolo kwa anthu ambiri.

Tidzaoneka ngati Mulungu kwa iwo ali nafe chifukwa choti tikumasula mphamvu ya Mulungu wamphamvu yonse kupyolera mu miyoyo yathu kapena tidzakhala choseketsa ku dziko lapansi pamene tikulowa mu chipembedzo chisankho ndi chako.

PETRO APHUNZIRA KUKHULUPILIRA MULUNGU OSATI KUZIKHULUPILIRA YEKHA.

Tsopano tiyeni tibwere ku chipangano chatsopano ndipo poyamba tione pa Petro- munthu amene adasiya zonse kutsatira Yesu.

..... “ Petro anayamba kunena naye onani ife tinasiya zonse ndipo tinakutsataniinu.....” (Mariko 10:28)

Apanso zikuonetsa ngati munthu wopulumutsidwa. Ambuye Yesu asadafe pamodzi ndi kuuka ku manda. Kodi Petro adaphunzira kudalira pa mphamvu ya Mulungu wamphamvu zonse kapena adali kudalira pa mphamvu za iye yekha kuti akhazikitse ufumu? Nkhani yonse ya umo mphamvu ya kudzidalira kwa Petro pa mphamvu zake pamodzi ndi kupasuka kwake yalembedwa pa Luka 22:31-34 ndipo tidzawerenga motere.

..... “Simoni, Simon anafunsa akutengeni kuti akupeteni ngat tirigu koma ndimakupempherera kuti chikhulupiliro chako chingazime ndipo iwe pamene watembenuka mtima ukhazikitsa abale ako. Ndipo anati kwa iye, Ambuye ndiripo ndi kapite ndi inu ku ndende ndi ku imfa. Ndipo Iye anati, “Ndikuuza, Petro sadzalira tambala lero lino kufikira udzakana katatu kuti sindidziwa..... (Luka 22:31-34)

Petro adayankha nati “Ngakhale onse adzakhumudwa chifukwa cha inu, ine sindidzakhumudwa nthawi zonse.

(Mateyu 26:23)

Apa tikutha kuona Petro wodzadzidwa ndi kudzikhulupilira mwa mphamvu za iye yekha. Sindidza.....” Tikuona u “ine” mu moyo wa Petro ngakhale kuti adali wophunzira wa Yesu ndipo adasiya zonse kutsatira yesu. Tsopano Mulungu adzapasula mphamvu zonse zozidalira za Petro. Pmane Yudasi adampereka Yesu,

..... “Pamenepo Simoni Petro pokhala nalo lupanga analisolola nakantha kapolo wamkuru wansembe, nansenga khutu lake lamanja koma dzina lake la kapoloyo ndiye Maliko. Pamenepo Yesu anati kwa Petro, longa lipenga m’chimake chake, chikho chimene Atate wandipatsa, ine sindi..... ichi.

(Yohane 18:10-11)

Apa mpokwanira kulowetsa wokhulupilira wodzipereka mu chitsokonezo. Pano ndikuteteza Mulungu wanga ndi mphamvu zanga zonse ndipo tsopano akutsutsana nanenso kukhala ngati ali mbali ya anthu ofuna kumuononga! Poonjezera apo, Yesu akuona ngati ndi chifuniro cha Mulungu kuti moyo wake uwonongedwe. Apa ndi zinthu zosamveka konse.

Moyo umavuta kuumvetsa ngati siudalumikizanitsidwe ku kuyenda kwa Mzimu chifukwa choti njira za Mulungu sizili njira zathu ndipo maganizo a

Mulungu Sali maganizo athu. Zimangokhala ngati ufumu wozondoloka dodolido pamene woyamba ali womaliza ndi womaliza ali woyamba ndipo ngati usunga moyo wako udzautaya ndipo ngati utaya moyo wako udzaupeza. Sindidakhoze kusanthula dongosolo pamodzi ndi zolinga za Mulungu. Chinthu chofunikira ndi kasayerekeze kutero. Mulungu amavumbulutsa izo kupyolera mwa aneneri, ansembe komanso mafumu kwa Mulungu wathu. Wankurukuru. Mwa ichi tikhoza kupempha Mulungu pa zimene zikuchitika ndipo nthawi zonse amatiuza

Usiku usadathe, Petro adamukana Yesu katatu ndipo adaturuka kunja akulira mosweka mtima. Masiku ambiri asadathe Petro adapezeka kuti adasiya zonse ndipo adakabwereranso kupita ku ntchito yake yopha nsomba. Tsopano apa ali woyenerera kugwiritsidwa ntchito ndi Ambuye. Umunthu wake watheratu. Tsopano akutha kuona kuti sangathe kuchita kenakalikonse mwa mphamvu za iye yekha kuti amange ufumu wa Mulungu. Mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa watsimikizilika kuti uli wopanda pake. Tsopano monga munthu wotha mnzeru, apa ali tsopano woyenerera kugwiritsidwa ntchito. Yesu adamuchilitsa Petro pa Yohane 21 ndipo adamuitananso ku utumiki polankhula motere, “Dyetsa nkhosa zanga” Kenako tsopano Petro anadikira mphamvu yochokera kumwamba asadayambe kugwira ntchitoyo.

..... “Ndipo pakufika tsiku la Pentekosite, anali onse pamodzi pa malo amodzi. Ndipo mwa dzidzidzi anamveka mau ochokera kumwamba ngati nkokoma wa mphepo yolimba nadzadza nyumba yonse imene anali kukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawikana onga moto ndipo unakhala pa iwo onse wayekhayekha. Ndipo anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera nayamba kulankhula ndi malilime. (Machitidwe 2:1-4)

Tsopano Petro wakonzekera kulowa mu utumiki wodabwitsa.

Taonani nchito yake ya tsiku ndi tsiku

.... Koma Petro ndi Yohane anali kukwera kunka ku kachisi pa ora lakupembedza ndilo chisanu ndi chinayi”

(Machitidwe 3:1).....”

Waphunzira tsopano kupemphera tsiku ndi tsiku, kufunafuna mphamvu ya Mulungu kuti tsopano adzadzidwe nayo pamodzi ndi mnzeru. Mulungu wamaliza phunziro lonse. Wadutsa naye Petro mu njira zosiyanasiyana

akumukonza kuchotsa umunthu wake pamodzi ndi kuzidalira kwake. Mulungu wamuchilitsa Petro kumuitananso ku utumiki, kumudzodza ndi mphamvu ndi njira yomweyo imene iye amachitira ndi aliyense wa ife. Kodi iwe uli pa siteji iti pa kusanthulidwa kotere?

PAULO APHUNZIRA KUKHULUPILIRA MULUNGU OSATI KUZIKHULUPILIRAYEKHA.

Pomaliza tsopano tiyeni tibwere pa Paulo munthu womalizira mu kusanthula kwathu. Tiyeni tione umo Mulungu adamuphunzitsira Paulo kukhulupilira mu mphamvu zodabwitsa za Mulungu osati za munthu zomwe zili za malire.

Paulo akufotokoza za ubwana wake pamodzi ndi maphunziro komanso kudzipereka kwake pa Afilipo 3 motere,

..... “Ndingakhale inenso ndiri nako kukukhulupilira mnthupi ngati wina yense ayesa kukhulupilira mnthupi makamaka ineyo wodulidwa tsiku lachisanu ndi chitatu wa m’badwo wa Israeli wa fuko la Benjamini, Mheberi wa Aheberi monga mwa lamulo, mfarisi.....”
(Afilipo 3:4-6)

Ngati padali munthu wina wadzipereka, adali Paulo. Iye adali wodzipereka koma mu njira ya chipembedzo ndipo adali kusunga chilamulo ndi kukhala moyo wa mchilamulo komanso kuzunza onse amene iye amawaona kuti sadali monga mwa chilamulo cha Mulungu pamodzi ndi kudzipereka kotheratu ndipo adachigwiritsa ntchito mu moyo wake. Komabe zonse izi amachita zidali monga mwa mphamvu zake za thupi. Iye adali kukhala monga mwa mnzeru za umunthu- kudya mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa. Sadali munthu woyenda monga mwa Mzimu. Adali asadamvepo kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu. Iye amakhala monga mwa chilamulo basi. Iye amachita monga ndimachitira zaka khumi zadutsazo pa moyo wanga wa chikristu. Inenso ndidakhala moyo wa mchilamulo. Sindidali kumva kulankhula kwa Ambuye kapena kuona masomphenya. Ndinkatsutsa anthu mu mpingo amene sindidali kugwirizana nawo. Ndidali kukhala monga mwa nzeru za thupi. Ndidali monga mfarisi wa makono!

Kenako Mulungu anati, “ Wataikiratu ndikuona mtima wa Paulo. Akundifunafuna ngakhale kuti akutsutsana ndi mpingo wanga. Wangosokonezeka pang’ono chabe pamodzi ndi kutsocheretsedwa. Ndikomana naye ndipo ndimuongola bwino” Kodi adakomanadi? Inde, pa njira ya ku Damasiko!..... “ Koma Saulo wosaleka kupumira pa akuphunzira a Ambuye kuopsya ndi kupha ananka kwa mkuru wa ansembe napempha kwa iye akalata a kunka nao ku Damasiko kumasunagogi kuti akapeze ena otsata” njirayo amuna ndi akazi akawatenge. Kudzanao omangidwa ku Yerusalemu ndipo poyenda ulendo wake kunali kuti iye anayandikira Damasiko ndipo mwadzidzidzi kudawala momzingira kuunika kochokera kumwamba ndipo anagwa pansi namva mau a kunena naye Saulo Saulo. Undilondalonderanji? Koma anati ndinu yani Mbuye? Ndipo anati “ Ndine Yesu” amene umulondalonda.....”

(Machitidwe 9:1-20)

Wow! Nkhani yodabwitsa bwanji? Tangochokera ku chipembedzo kulowa ku chikhristu chodabwits! Tangochokera ku mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa kupita ku mtengo wa moyo kuchokera ku mphamvu za thupi kupita ku mphamvu za uzimu. Kusintha kotere kuyenera kukhala mwa mkhristu aliyense. Kuyenera kukhala mu moyo wanga. Kuyenera kukhala mu moyo wako. Kodi kwachitika mwa ine? Ndalankhula poyamba kuti chitsokonezo nthawi zonse ndi sitepe yoyambilira kuvumbulutso. Paulo anadutsa mu chitsokonezo pamene kenako adadzindikira kuti zonse adali kukhulupilira zidali zolakwika ndipo tsopano adayenera kuti akawerengenso ndi kuona zonse adaphunzitsidwa. Paulo adataya maganizo onse a anthu ndi maphunziro awo ndipo adangosunga za Mulungu.

..... “ Kapena kukwera kunka ku Yerusalemu sindinankako kwa iwo amene anakhala atumei ndisanakhale mtumwi ine komatu ndinamuka ku Arabia ndipo ndinabweranso ku Damasiko. Pamenepo patapita zaka zitatu ndinakwera ku Yerusalemu kukadzindikirana naye kefa”

(Agalatiya 1:17-18)

Aliyense wa ife ayenera kukhala payekha ndi kumfunanso Mulungu mu mizimu yathu. Iye (Mulungu) aposa nzeru za maphunziro a mau a Mulungu (theology) zimene ndikhoza kuphunzira kwa munthu wina Mulungu akungofuna kukhala mkati mwathu ndi kugwiramo ntchito. Njira yake yompeza iye ndi kutenga nthawi pang’ono kuphunzira kumuona iye umo

amayendera mwa ife. Uko ndi kuphunzira kwabwino. Uko si kuphunzira kwa mmabuku koma komuona akuyenda mu moyo wathu. Ndimatha kuona mphamvu yake. Ndimatha kuona masomphenya ake. Ndimatha kumva kulankhula kwake. Izi siungazipeze pamene wakhutula mtima wako kwa iye.

Patadutsa zaka zitatu, Paulo adapita ku Yerusalemu kukaonetsa mavumbulutso ake kwa a kuruakuru. Ataonetsa izi kwa atsogoleri awo Paulo adapitilira kulalikira uthenga mwa mphamvu.

..... “Pamenepo patapita zaka zitatu ndinakwera kunka ku Yerusalemu kukadzindikirana naye Kefa ndipo ndinakhala naye masiku khumi ndi asanu vesi 21- pamenepo ndinadza ku mbali za suriya ndi kilikiya.....”

(Agalatiya 1:18-24)

Ndi mavumbulutso a tsopano otere, Paulo adayambanso kumtumikira. Utumiki wake udali watsopano ndi wodabwitsa! Amachilitsa odwala, komanso kuukitsa akufa. Tsopano ali chotengera chomasula mphamvu yodabwitsa ya Mulungu.

..... “Komatu zonse zimene zinandipindulira zomwezo ndinaziyesa chitayiko chifukwa cha Khristu. Komatu zenizeninso ndiyesa zonse zikhale chitayiko chifukwa cha mapambanidwe a chidzindikiritso cha khristu Yesu Ambuye wanga chifukwa cha Iyeyu ndinatayikitsa zinthu zonse ndipo ndiziyesa zapadzala kuti ndikadzionjezere Khristu.....”

(Afilipo 3:7-11)

Paulo wadutsa mu imfa pamodzi ndi mzukiro wa iye yekha. Tsopano akutha kuona kuti Sali iyenso kukhala ndi moyo koma Khristu ndi amene ali ndi moyo mwa iye. Halleluya!! Paulo tsopano akutha kuona Mzimu ukuyenda mwa iye. Sakukhalanso monga mwa thupi. Iye akukhala mwa mzimu ndipo mtengo wa moyo uli mkati mwa mtima wake. Iye ali womezetsedwa ku ulemelero wa Mulungu!

MASITEJI AWIRI PA MOYO WA CHIKHRISTU.

Pali masiteji awiri mu moyo wa chikhristu. Yoyamba ndi chipulumutso

pamene wakomana ndi Yesu.

Yachiwiri ndi pamene Agalatiya 2:20 yachitika mu moyo wako. Kodi masiteji onse awa achitika mu moyo wako? Ngati ayi, pita ku chipululu ndipo ukakumane ndi Ambuye omwe amayendayenda mu mtima mwa munthu kosalekeza.

Tikatha kulandira chipulumutso chatu, pamakhala nthawi yotsatira ya kulimbana pamodzi ndi zolephera. Pomaliza pake timadzadzindikira kuti tafa ndi Yesu Khristu ndipo tsopano tabisika mwa Iye. Kuli ngati kuti ndili ndi 50,000 USD ku banki koma mu umbuli wanga ndikuganiza kuti ndili ndi 5,000.00 UsD. Tsono ndikuyesa kukhala ndi moyo wanga mwa muyeso wa 5,000.00 USD kufikira pomaliza pake ndidzadzindikira kulakwa kwanga ndipo kenako ndikatenganso ndalamazo mdalitso lachiwiri monga anthu ena amatchulira.

KUSANTHULANSO FUNDO ZINA ZA PA AROMA 10.

- Baibulo likufotokoza za mbiri ya anthu amene adaphunzira kukhulupilira Mulungu osati mphamvu za iwo okha.
- Ili ndi phunziro limene tonse tiyenera kuphunzira.
- Pophunzira phunziro ili, timasintha kuchokera ku chipembedzo kubwera ku chikhristu chodabwitsa.
- Timapeza nthawi zonse mphamvu ya Mulungu ku chipululu.
- Tiyenera kukhala ofunitsitsa kupita ku chipululu kukaona za kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu.
- Pamene mphamvu za kuzidalira zapasulidwa, tsopano tikhoza kulumikizitsidwa ku ulemelero. Mphamvu zodabwitsa za uzimu zimayamba kuyenda mwa ife.
- Lembera fundo zina zimene ukuona kuti zili zofunikira kwa iwe.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBILANA.

- Kodi ukuvomereza kuti chisokonezo nthawi zonse chimabweretsa vumbulutso?
- Kodi udyamba wadutsapo nthawi ya chisokonezo chimene mapeto ake chidabereka vumbulutso lalikuru? Ngati zili choncho,

kodi ukhoza kukumbukirapo za izo zidachitika. Monga ukuoneramu, kodi nkoyenera kuchita chikondwerero cha nthawi ya chisokonezo podzindikira kuti Mulungu ali ndi zolinga za tsopano kupyolera mu chisokonezocho?

- Kodi wadutsapo masitepe ofanana ndi anthu anayi omwe tasanthula mu chaputala ichi? Ngati ndi choncho, kumbukira masitepe onse mu moyo wako ogwirizana ndi chaputala ichi. Kodi tsopano iwe uli pati? Kodi uli pa siteji iti? Kodi ndi sitepe yotsatira iti imene Mulungu akukutengera? Kodi ukukonzekera wekha kutenga sitepe iyi? Kodi ukuyenda ndi mphamvu ya Mulungu kapena ukukana? Monga Mose, Kodi ukufuna kudzipereka ku zolinga za Mulungu mu moyo wako?
- KULEMBERA-
“Ambuye, chonde lankhulani nane kukhudzana ndi masitepe a chikhristu mu moyo wanga. Kodi ine ndili pati? Kodi mukunditengera kuti? Kodi mukufuna ine kuti ndiyankhe motani pa nthawi ino?
Lembera zonse mu buku lako lapadera zimene Ambuye alankhula ndipo fika wokonzeka kugawana izi ndi gulu lako.

CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHIMODZI

UPANGIRO WOFUNIKA KU CHIPULULU.

Ndi chinthu chosangalatsa kuona umo nthawi zambiri Mulungu amatenga anthu amene akuwakonzekera ku chipululu pa nthawi monga ngati njira imodzi yokawaphunzitsa umo angatumikirire Iye. Mukuganiza kuti nchifukwa chiyani amachita zimenezi? Kodi pali kanthu kenakake ku chipululu kamene sitingathe kukapeza mu mabungwe athu? Ngati ndi chomwecho, kanthu kake nchiyani? Kodi Mulungu amatitengera kumeneko kuti tikazinzike? Kukaononga ziyembekezo zathu zonse? Nchifukwa chiyani amatitengera ku chipululu?

Kodi Mulungu adakutengerapo ku chipululu? Ngati ndi chomwecho, nthawi iti? Kodi udaphunzira chiyani kumeneko? Kodi iye adachita mu mtima mwako pamodzi ndi mu moyo mwako zimene amafuna kuchita? Tiyenera

kupeza mayankho ku mafunso awa kuti tikathe kuphunzira kupereka mwa changu kupyolera mu izo taziona mmoyo mwathu mu nthawi yokhala ku chipululu ndi kupitilirabe ku dziko la malonjezano.

MULUNGU NDIAMENE AMATITENGERA KU CHIPULULU.

Kumbukirani kuti pamene Mulungu adatsogolera ana a Israeli Iye adawadutsitsa mu chipululu. Izo zidachitikanso ndi Yesu:

..... “Ndipo Yesu wodzala ndi Mzimu Woyera anabwera kuchokera ku Yordano natsogozedwa ndi Mzimu kunka ku chipululu.....” (Luka 4:1)

Sikuti ndimakangoyendayenda ku chipululu. Mulungu amasankha nthawi zomwe zili zoyenera kwa ine ndipo amanditsogolera ku chipululu. Iye ali ndi zolinga za padera mu maganizo ake. Iye amadzindikira kuti icho ndi chimene ndikusowa. Mulungu mnthupi nkovuta kuti ine ndione ichi. Ndakhala ndi kuona bwino kwambiri mu mabungwe anga. Ndakhala moyo wofewa, wovala bwino komanso kudya bwino ndi kuona zosowa zanga zonse zikukwanilitsidwa. Kupita malo kumene zoterezi sindikapeza ndi chinthu chovuta kwambiri.

KUCHIPULULU NDI KUMENE KUZIDALIRA KWAKO KUMAPASULIDWA.

Ndidadzindikira mwa changu kuti sitingathe zofunikira zonse ku chipululu. Ichi chikhoza kukhala chipululu chenicheni cha thupi kapena Mulungu akhoza kungondichotsa pa ntchito yanga yokhazikika ndi kundibweretsa mu nthawi ya kusintha pamene tsopano ndikakamizika kumukhulupilira Iye. Mu njira yina iliyonse – awa ndi malo pamene kuzidalira wekha ku mapasulidwa. Ndi malo pamene ndimaphunzira kusadalira mphamvu zanga koma mphamvu zodabwitsa za Mulungu yemwe ali wondipatsa zosowa komanso wokwanilitsa. Mulungu adapereka chakudya kwa ana a Israeli tsiku ndi tsiku pamene adali kuyenda mu chipululu mu njira yodabwitsa. Kudali kumeneko kumene adaphunzira kuti ufooka umasandulika mphamvu ndipo iyi ndi njira imene ana a Mulungu amakhalira.

Ndadutsa mu nthawi za kusintha zambiri pa moyo wanga komanso moyo wa

zochitika chitika wa chipululu ndipo pamene ndikulemba Mulungu amandiuza kuti iye ali wopatsa pamodzi ndi wokwanilitsa ndi wokwanilitsa ku moyo wanga, komanso ndiyenera kumukhulupilira Iye. Izi amandilankhula pafupipafupi. Chitsanzo chimodzi chili panso apa;
11-26-89

..... “ Ambuye , ndikuona kuti mukufuna kundibwezeretsa lero lino. Ndikuona kuti mwayamba kale ntchito yondibwezeretsa usiku uno.....”

..... “ Inde, mwana wanga, ndayamba kale ichi mkati mwa usiku uno. Ndatumiza angelo kuti akutumikire. Iwe uli mwana wanga wokondedwa ndipo mwa iwe ndikukondwera”

..... “ Koma Ambuye, ndimakulakwirani nthawi zambiri”

“ Mariko, ndikukupatsa mayesero omwe siudaonepo. Ndikukutambasula ku ntchito imene ndakuyitanira. Ichi ndi chifukwa chake ukuona kulephera chifukwa ukulimbana kutambasula chikhulupiliro chako monga ndidakuuza kumayambiliro kwa chaka chino.....”

.... “ Inde, Ambuye, ndikukumbukira kuti mudandiuza kutambasula chikhulupiliro changa. Ichi ndidaiwala kotheratu.....”

..... “ Mwana wanga, zonse zimene wadzindikira ndi zidziwitso chabe. Iyi ndi njira ndakhazikitsira munthu. Usadandaule popeza ndili ndi iwe”

..... Mariko, kulitsa pamodzi ndi kutambasula chikhulupiliro chako popeza ndikugwira ntchito yodabwitsa kupyolera mu moyo wako. Sindidzakusiya kapena kukutaya. Ndidzakhala ndi iwe. Khulupilira ine. Pitoliza kulemba, kusanthula, pamodzi ndi kuphunzitsa. Iwe uli wofunikira kwambiri kwa ine. Ichi ndi chifukwa chake ndikukusanza pamodzi ndi kukulimbikitsa. Mwa ichi, mwana wanga chita chikondwerero cha nthcito iyi mmene ili mkati mochitika osati kumapeto ake. Ndibwerezanso kutero kuti chita chikondwerero.

Ndidzatumiza anthu ena kukulimbikitsa pa nthawi ino. Umo ndimo thupi langa limagwirira ntchito. Umalimbikitsa anthu ena pamene ukuona cholinga ndipo iwo amakulimbikitsa pamene akuona cholinga cha mapeto ake. Landira iwo amene ndatumiza kwa iwe....”

..... Inde, Ambuye wanga’

..... “Mwana wanga udzapita patsogolo uku ndi uko ndipo udzalankhula mau. Koma pa nthawi ino ndakuitana kubwera kukonzekera chotengera pamodzi ndi mau amene ndidzamuza iye kuti alankhule. Pemphera ku kumasulidwa kwa zinthu zonse. Pa nthawi ino ndidzapitiliza kukwanilitsa zosowa zako penyerera ichi.....”

Ambuye adandipatsa malangizo umo ndingakondere mkazi wanga kwambiri komanso chinthu china chotsatira chimene amafuna kuti ndichite tsiku limenelo.

Apa mutha kuona umo Mulungu akunditambasulira. Iye akundiphunzitsa kukhulupilira mwa Iye komanso kumvetsa malo pamene wandiika pamodzi ndi zolinga zokhalira pamenepo komanso umo ndingayankhire ndidakali pamenepo. Mnzeru zotere pamodzi ndi mphamvu zimayenda mu moyo wanga pamene ndikulemba. Izi sikuti ndi mnzeru za thupi chabe. Pomaliza pake, Mulungu adandilangiza za moyo wa tsiku ndi tsiku.

KU CHIPULULU NDI KUMENE TIMAPHUNZIRA KUSIYA KUDANDAULA.

Kuyambira pa numeru 11 mpaka 18, akufotokoza za umo ana aIsraeli amadandaulira pamazo pa Mulungu. Izi zidabweretsa mkwiyo wa Mulungu komanso zotsatira zoipa. Ukhoza kufuna kuwerenga machaputala awa kuti mukathe kuona zinthu zimene Mulungu amachita ndi mitima ya anthu ake. Iye adali kuchotsa kudzikudza, njiru, umboni, kusakhulupilira komanso kusowa kuthokoza pa zinthu zonse. Tsiku lina Mulungu adapha anthu 14,700 amene amadandaula pamaso pa Mulungu (Numeru 17:49). Pamene ndidaona ichi, ndidaona kuti nkofunikira kusiya kudandaula. Mulungu amadana ndi kudandaula. Iye watilamulira nthawi zonse kukhala wokondwera komanso mu chilichonse kuthokoza pamodzi ndi kuyamika chifukwa ali Ambuye wa zonse. Pamene tikudandaula, timalephera kuona U Mbuye wake mu zonse ndipo timayamba kudzialira tokha pamodzi ndi kusakhulupilira.

Kulankhula mwa tchutchuchu ndimakhala ndi nthawi zambiri zimachitika nthawi zambiri pamene ndalephera pamaso pa Mulungu ndi kuyamba kudzialira mwa ine ndekha. Mwa ichi kudandaula kwakhala chida choonera

kuti ndachoka pa maso pa Mulungu pa moyo wanga. Mose adalinso kupsyinjika nthawi zambiri.

Ngati mundichitira motere, chonde ndiphenitu – Ngati ndapeza ufulu pa maso panu, musalole kuti ndione tsoka langa (Numeri 11:15)

Ndikhoza kudzindikira ndi ichi “ Mulungu, chonde, nditengeni kuti ndisaone kusauka kwanga pamene ndalephera pa maso panu” Ichi chimakumbutsa za chimene ndiri. Ndi chinthu chabwino kuti ndikuphunzira kukhala moyo wolumikizana ndi ulemerele wa Mulungu.

Nchodziwika bwino kuti malingaliro ena amene amabwera mmutu mwathu mu nthawi za kuyesedwa kwathu amachokera kwa satana. Yesu adapita ku chipululu (Luka 4:1) Ndipo adali ndi kukambilana ndi satana. Satana adamuyesa Iye kugwiritsa ntchito mphamvu zake kuti azithandize yekha. “ Lankhula kwa miyala iyi kuti isanduke mikate” Satana adali kulankhula mwa matsutsano mu kulankhula kwake “ Ngati mwana wa Mulungu” Satana amafuna kugwiritsa ntchito kuzikudza kwake, “ Ndidzakupatsa ulamuliro wonse” Satana adamuyesa Yesu kuti amuyese Mulungu “ Usayese Ambuye Mulungu wako” Satana adagwiritsa ntchito malemba opatulika mu kuukira kwake kugwiritsa ntchito malembo molakwika.

Mwa ichi, mbali imodzi ya zimene zimachitika mu zochitika mwa chipululu chatu cha uzimu ndi yoti timakomana maso ndi maso ndi usatana, matsutsano matukutuku, maganizo a umbombo mu mitima yathu pamodzi ndi mu maganizo athu, kudzindikira bwino kuti ndi kulankhula kwa satana ndi kuwagonjetsa pogwiritsa ntchito kulankhula kwa Mulungu wa kwa Mulungu wa mphamvu yonse. Kuchipululu ndi malo komanso nthawi mu moyo wathu pamene timapeza pamodzi ndi kuchotsa kulankhula kwa satana mkati mwa ife komanso kudzindikira kuyenda kwa Mzimu pamodzi ndi kulankhula kwa Mulungu mkati mwathu.

KUCHIPULULU NDI KUMENE TIMAMVA KULANKHULA KWA MULUNGU.

Pa Deteronomo 5:22-31, Mose akufotokoza za kubweretsanso kwa kulankhulanso kwa Mulungu pamodzi ndi chiyanjano kwa anthu ake a

pangano.. Iye adalenga munthu ndi cholinga kuti azikhala naye mu chiyanjano adali pa chiyanjano ndi Adamu ndi Heva pa nthawi yaitali kufikira nthawi pamene tchimo lidapasula chiyanjano. Tsono ku chipululu, Mulungu akufuna kubwezeretsa chiyanjano ndi ana ake popereka kwa ana a Israeli mau ake-kulankhula kwake. Ndi kulankhula kwake, pamabwera moto umene tikudzindikira kuti ndi moto wopsyereza wa Mzimu Woyera mu moyo wathu pamene akupsyereza tchimo, kutidutsitsa mu imfa mu matupi athu kuti tikathe kukhala a mphumphu ku mizimu yathu. Ana a Israeli sadali otsimikizika kuti amafuna kudutsa mu imfa ya thupi yotere. Kudali kowawa. Iwo adakana kulankhula kwa Mulungu ndipo mmalo mwake adasankha kutsatira chilamulo. Pali malo ake a chilamulo monga tafotokoza kale. Chimatisunga kufikira tikaphunzira kumvetsera ku kulankhula kwa Mulungu ndipo chimandiphunzitsa kuti thupi langa lilibe mphamvu kundipanga ine kukhala wangwiro. Tsono ana a Israeli adakana kulankhula kwa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake sadafike ku dziko la malonjezano koma onse adafera mu chipululu. Dziko la malonjezano ndi chipatso chokhala mu kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu. Ngakhale ana a Israeli adagonjetsa mizinda yomwe idali mu dziko la malonjezano adachita izi kupyolera mu kumvera zonse zochokera mu kulankhula kwa Mulungu.

Ku chipululu ndi ku malo kumene tiyenera kuphunzira kumva kulankhula kwa Mulungu pamodzi kulowa mu kumvera konse. Ngati ungate kusemphana ndi phunziro ili, nkovuta kuturuka mu chipululu mu moyo wako. Ngati siudaphunzirebe mpaka pano kumva kulankhula kwa Mulungu, ndikupempha kuti uwerenge umboni wanga mu buku la “kulankhulana ndi Mulungu” ngati ukudziwa umo ungamvere kulankhula kwa Mulungu koma siukutha kumvetsera pamodzi ndi kukhala womvera pa zinthu zambiri, chonde, lapa ndi kuyambanso mwa tsopano luti ukathe kuyenda moyo wa uzimu.

KUSANTHULA FUNDO ZINAZA PA CHAPUTALA II

Chipululu ndi gawo lofunikira ku madera onse pa moyo wathu.

- Pali fundo zofunikira zimene tingaphunzire ku chipululu
- Mulungu amatitsogolera ku chipululu pamene nthawi yakwana.
- Ngati tingaphunzire maphunziro Mulungu watipatsa Mulungu amatitsogolera ku chipululu.
- Ngati sitingaphunzire maphunziro. Mulungu watipatsa, sitingathe

- kutuluka ku chipululu koma mmalo mwake timafera kumeneko.
- Mbali yina ya chipululu ndi dziko la malonjezano.
- Lembera fundo zina zomwe zili zofunikira kwa iwe.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi udayamba wapita ku chipululu? Kodi udakaphunzira maphunziro Mulungu amafuna kukuphunzitsa kumeneko? Kodi adali otani? Kodi moyo wako wasintha bwanji monga mwa zotsatila za kumvera kwako ku maphunzirowo? Gawana izi ndi gulu lako.
- Kodi udaonako kulankhula kwa Mulungu mu mtima mwako? Kodi udaonako kulankhula kwa satana mu mtima mwako? Kodi wagwetsa pansu kulankhula kwa satana ndi kukangamira kulankhula kwa Mulungu mkati mwako? Kodi uli womvetsera pamodzi ndi womvera kwa Mulungu?
- Kodi wapita ku chipululu ndi mtima wonse pamene Mulungu adakutsogolera kumeneko? Kodi wadzipereka ku dzanja lake ndi cholinga kuti akuphunzitse ndi kukulumikizitsa ku ulememero wako? Gawana izi ndi gulu lako.
- KULEMEBRA- “Ambuye , kodi mukufuna kulankhula chiyani ndi ine kukhudzana ndi zochitika mu moyo wanga ku chipululu? Kodi zidali kuti? Chidali chiyani? Kodi mumafuna kundiphunzitsa chiyani? Kodi ndaphunziradi? Kodi ndili wofuna kuyenda ndi mphamvu yanu kapena ndikukana pamene mukundigwira dzanja? Zikomo Ambuye pa zimene mukulankhula....” Monga mwa nthawi zonse, lemba mafunso awa mu buku lapadera kuzitonholetsa wekha pa maso pa Ambuye ndi kutchera khutu ku kuyenda kwa Mzimu. Lembera zimene akulankhula kwa iwe. Gawana izi ndi gulu lako.

CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHIWIRI.

KUWERENGANSO CHIPANGANO CHATSOPANO

Mu kusanthula kwanga choonadi chisanu ndi chiwiri kumayambiriro kwa bukuli, ndimawerenganso chipangano chatsopano ndipo ndimapeza kuti lili buku la tsopano. Lidakhala la moyo kusiyana ndi poyamba ndipo vumbulutso loyaka moto mu mtima mwanga lidali mwa ine. Tiyeni tisanthulenso magawo

angapo a bukuli limodzi ndipo tione chimene tingapeze. Tisadatero, tiyeni tikumbukire pamodzi choonadi chisanu ndi chiwiri cha buku ili.

Choonadi #	1	Mulungu ali yense mu zonse
Choonadi #	2	Ndine chotengera
Choonadi #	3	Sindilinso ndi moyo
Choonadi #	4	Khristu ali moyo wanga
Choonadi #	5	Ndafa ku chilamulo
Choonadi #	6	Ndimakhala ndi moyo mwa Mzimu
Choonadi #	7	Ndimakhala ndi moyo mwa chikhulupiliro kuti Mulungu ali

Emmanueli

KUSANTHULANSO AROMA 6, 7 NDI 8

Aroma 6 pamodzi ndi 8 chikufotokoza masiteji a moyo wa chikhristu. Aroma chaputala 6 chikugwirizana pa zinthu zochitika pa chipulumutso chathu. Aroma chaputala 7 chikufotokoza za kulimbana komwe timakhala nako tisadasandulike kukhala mwa khristu ndipo pa Aroma 8 akufotokoza za moyo wa mtendere pamodzi ndi mphamvu zomwe timakhala nazo pamene taphunzira kuti tafa ndipo moyo wathu wabisika mwa Mulungu mwa Yesu Khristu. Ukhoza kuwerenga mwa pemphero machaputala awa tsopano lino tisadapite patali. Paulo akufokoza za moyo watsopano pa Aroma 6:4 motere. “ Chifukwa chake tinaikidwa mmanda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa kuti monga Khristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerele – tikayende moyo wa tsopano” Popeza tsono ndadutsa mwa ubatizo wa mmadzi, tsopano ndili wokonzekera kuyamba moyo watsopano. Ndikudzindikira kuti moyo wanga wakale udapachikidwa pamodzi ndi Khristu Yesu (Aroma 6:6) Ndimadzitenga ndekha monga wakufa ku uchimo ndipo ndili ndi moyo mwa khristu Yesu (Aroma 6:11) ndipo ndimachita moyenera osaperekanso mwayi kuti uchimo ulamulire mu matupi athu. Izi zikumveka bwino. Sichoncho kodi? Lingalira mozama za ichi. Tiyeni tionenso apa.

..... “ Pakuti chabwino chimene ndichifuna sindichichita koma choipa chimene sindifuna chimenecho ndichichita. Ndipo chotero ndipeza lamulo ili kuti pamene ndifuna chabwino choipa chiliko.... Munthu wosauka ine adzandilanditsa ndani mthupi la imfa?

(Aroma 7:19,21-24).....” Payenera kukhala zochitika zambiri kuposa kudzindikira chabe. Ndili pa mkhondo ya uzimu. Ndili mu kulimbana pakati pa thupi langa ndi mzimu. Thandizo! Inde, pali thandizo lalikuru.

..... “ Pakuti chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa khristu Yesu chandimasula ine ku lamulo la uchimo ndila imfa” (Aroma 8:2.....”

Aha! Palinso chilamulo china chomwe ndidali kuyiwala (kapena kuti sindidachiphunzire). Ichi ndi chilamulo cha mzimu wa chilamulo cha moyo mwa khristu Yesu. Ichi ndi chinthu chosangalatsa kwambiri. Tsopano ndi kulingalira movyola. Tsopano ndili pa muyeso wa uzimu ndipo sikuti ndikungokhudza mzimu wanga. Ndikukhudza mzimu wa khristu umene walumikizana ndi mzimu wanga komanso kuona kuyenda kwa moyo wake. Ndikupenyenera ndekha pa kuyenda kwa mzimu mkati mwanga (Aroma 8:5,6) ndipo ndikuona kuyenda kwa mphamvu mu moyo wanga wonse (Aroma 8:11). Ndikuona kulumikizana kotheratu ndi Mulungu pamene ndikuona kuyenda kwake mkati mwanga (Aroma 8:15-16). Tsopano akunditsogolera kuyambira mkati mwanga. Ndikuona kuzama kwa mzimu kutsogolera kwanga (Aroma 8:26) Sindichita kanthu mwa ine ndekha kapena mwa maganizo kapena mphamvu zanga. Nthawi zonse ndimapenyenera mphamvu pamodzi ndi kupuma kwa moyo wanga. Ulemerero kwa Mulungu! Wandimasula ku kudzidalira kwanga kulikonse. Wandipanga kukhala wa nthumadzi mu uzimu mwanga ndi Mulungu mmalo modzidalira ndekha.

KUWERENGANSO AKOLOSE

Poyamba penipeni pamene ndidawerenga mabuku a Paulo, ndidakusanthula mwachangu pakatikati peni peni pa phata lake. Icho ndichakudya chenichotafuna cha uzimu kenako ndidalinso kuona za” zimene sindidali kumvetsa kwenikweni. Tsopano ndikuona kuti kuthamangira pakati penipeni – phata la uthenga sizinthu zabwino ndidali kusemphana ndi zinthu zofunikira zomwe zikadakhocha kundipatsa mphamvu za padera. Izi sindingathe kuchita mwa ine ndekha koma Yesu ndi amene angachite kupyolera mwa ine. Mwa chitsanzo tiyeni tiwerenge kalata ya kwa Akolose. Ukhoza kuwerenga machaputala atatu usadapitilire. Pansi apa pali kulembera kwanga pa kulingalira kwanga pa machaputala a Akolose. Usanthule mozama.

Poyamba tikuona kuti Paulo adali kubwerezanso zimene iye amaona monga za phindu monga “ kukhala mu zenizeninso” za moyo: chikhulupiliro chiyembekedzo ndi chikondi (Akolose 1:4,5, I Akorinto 13:13) Izi ndimazona ngati chida choyesera umu ndikukhalira mwa khristu. Pamene ndazama pa maso pa ulemerero wa Mulungu ndimakhala wodzadzidwa ndi chikhulupiliro, chiyembekezo pamodzi ndi chikondi. Pamene ndakhala kutali ndi ulemelero wa Mulungu, zinthu zitatu izi sizimakhala mwa ine. Tsono tiyeni tifike pa vesi 10.

..... : Kuti mukayende koyenera Ambuye kukamkondweretsa monsemo ndi kubala zipatso mu ntchito yonse yabwino ndi kukula mchidzindikiritso cha Mulungu.....”

Apa tsopano ndili ndi lamulo lomwe ndiyenera kumvera. Ndikhoza kuyesera kuyenda moyenera Ambuye. Sindidali kudzikindikira zaka zadutsazo za mawu ndi kulemba mau otere “ Chidziwitso chenicheni” monga ngati tanthauzo la liu “chidziwitso” kodi pali “ chidziwitso” ndi “chidziwitso chenicheni”. Kodi zikhoza kutero kuti chidali chidziwitso cha mutu ndi chidziwitso cha mtima kapena kuti mtengo wa moyo ndi mtengo wodziwitsa za bwino ndi zoipa? Oh, chabwino, palibe nthawi yodandaula. Ndili lamulo limene ndiyenera kumvera! Ndiyenera kuyenda moyenera Ambuye. Tsopano tiyeni tipite vesi yachiwiri.

..... “Olimbikitsidwa m’chilimbiko chonse monga mwa mphamvu ya ulemerero wake kuchitira chipiliro chonse ndi kuleza mtima konse pamodzi ndi chimwemwe ndi kuyamika Atate amene anatiyeneretsa ife kulandirana nao cholowa cha oyeramtima mkuunika (Akolose 1:11,12).....”

Zosangalatsa zedi! Mwina ndi mphamvu yodabwitsa ya Mulungu imene imandilimbitsa kuyenda moyenera. Mwina ndi Iye amene andiyenereza ine.

..... Amene anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima natisunthisa kulowa ufumu wake” (Akolose 1:13).....”

Sindidadzindikire za ichi zonse zili pa phata la ntchito ya Mulungu osati ine.

..... “ Amene tiri nao maomboledwe mwa iye, m’kukhululukidwa kwa zochimwa zathu.....” (Akolose 1:14).....”

Apanso tikhoza kuona kuti chipulumutso changa sichili mu kuyesetsa kwanga koma mu machitachita a Mulungu.

..... “ Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa iye chidzalo chonse chikhaliye.....” (Akolose 1:19). Mulungu waika chidzalo chake mwa Yesu. Yesu ndi amene amaonetsera mphamvu yake yonse.

..... “Mthupi lake mwa imfayo kukaimika inu oyerana ndi opanda chirema ndi osatsutsika pa maso pake.....”

Akolose 1:22

Chifukwa cha ntchito ya Khristu, ndikuonetsedwa wopanda chilema pamaso pa Mulungu. Ukutanthauza kuti sizimene ndimachita zimene zimandipangitsa kukhala wopanda chilema? Kukongola kwanga kuli pa zimene Yesu wachita? Zosangalatsa! Mwina tsopano ndimasuke pang’ono mu ntchito yomalizika ya Yesu Khristu.

..... “ Ngatitu mukhalabe m’chikhulupilira, ochirimika ndi okhazikika ndi osasunthika kulekana nacho chiyembekezo cha uthenga wabwino umene mudaumva wolalikidwa cholengedwa chonse cha panso pa nthambo umene ine Paulo ndakhala mtumiki wake” (Akolose 1:23).....”

Ndimadziwa kuti padayenera kukhala “ ngati” penapake. Izi zidali zabwinokwambiri kwa ine. Ndikhala wosalakwa ngati ndiyenda mu chilungamo? Ayi, umakhala wosalakwa ngati wakhulupilira ntchito yomalizika ya Khristu mu mtima mwako. Ukhulupilira? Izi zili chomwecho? Ungokhulupilira? Kukhulupilira chiyani?

..... “ Ndiwo chinsinsicho chinabisika kuyambira pa nthawi ndi kuyambira pa mibadoyo koma anachionetsa tsopano kwa oyeramtima ake kwa iwo amene Mulungu anafuna kuwadzindikiritsa ichi chimene chiri chuma cha ulemerero wa chinsinsi pakati pa amitundu ndiye Khristu mwa inu chiyembekezo.....”

(Akolose 1:26-27)

Ndimakhulupilira mu chinsinsi chachikuru. Kodi chinsinsi chachikuru ichi nchiyani? Ichi chili Khristu Yesu amene akhala mwa ine ndipo ali chiyembekezo. Mmalo mokhulupilira mphamvu zanga zanga kundipanga kukhala wa ulemerero, ndiyenera kukhulupilira mu mphamvu yake yokhala mwa ine kundipanga kukhala wa ulemerero.

..... “amene timlalikira if endi kuchenjeza munthu aliyense mu nzeru zonse kuti tionetsere munthu aliyense wa mphumphu mwa Khristu.....” (Akolose 1:28).....”

Mwa ichi ali iye ukumulalikira. Kalero ndimalalikira za ine kuyesera kukhala woyera mwa mphamvu za ine ndekha. Ndidazolowera kulalikira za ine komanso zimene ndimachita koma tsopano zii zidatha mwa ine. Tiyeni tilalikire za WINA wokhala mwa ife mu mitima yathu amene ali Yesu Khristu. Tiyeni tilalikire kufikira tikaonetsetsa kuti aliyense ali ndi Khristu Yesu komanso mphamvu ya Mzimu Woyera. Ichi ndi chimene tiyenera kulalikira. “ Kuchita ichi ndizivutisa ndi kuyesesa monga mwa machitidwe ake akuchita mwa ine ndi mphamvu” (Akolose 1:29)...” ndi chiyembekezo. Mau amodzi a mphamvu ndi “ energies” kutanthauza kuchita zinthu mwa mphamvu. Kumadzindikiraka ngati kuyenda kwa machitachita a mphamvu mkati mwa moyo. Kumachotsa kulemedwa chikaikiro pamodzi ndi mantha mwa uzimu. Nthawi iliyonse uitana pa Ambuye kuti achite kanthu Iye amachita nthawi yomweyo.

“Yesu, mukutanthauza kuti zili zophweka motere?” “inde”

“ Koma siuyenera kuti uchite mwa mphamvu yako china chilichonse” “ chabwino, Mariko, usalimbane mwa thupi kulowa mu mpumulo. Koma pamene uli mu mpumulo osakhalanso mwa mphamvu zako, kenako tsopano kuyenda kwa mzimu kumayamba mwa iwe” “ Zotsangalatsa!”

..... “ Pakuti ndifuna kuti inu mudziwe nkhawa imene ndiri nayo chifukwa cha inu ndi iwowa a m’lodikaya ndi onse amene sanaone nkhope yanga mthupi kuti itonthozeke mitima yao nalumikizike pamodzi m’chikondi kufikira chuma chonse cha chidzalo cha chidziwitso kuti akadzindikire iwo chinsinsi cha Mulungu ndiye Khristu....”

(Akolose 2:1-3). “Ukuona Mariko, munthu amachita nkondo ndi cholinga kuti mitima ya anthu kuti ilimbikitsidwe”

..... “ Ichi nchosangalatsa. Ndidazolowera kupanda anthu mu chikondi cha chokhristu kuti alape.....”

“Mariko, ndikufuna kuwalumikiza mu chikondi komanso mu kumvetsa kwa chikhulupiliro ndi kuona umodzi umene akuona ndi Khristu amene akuyenda mu mitima. Mu kuyenda kwa mzimu kotere, mu chilichonse akusowa. Mwa ichi ngati angaphunzire kutchera ku kukuyenda kwa mzimu akhoza kukhala ndi mnzeru za uzimu komanso mphamvu za uzimu zodabwitsa.....”

“Zodabwitsa!” ndikuganiza kuti ulaliki wanga phata lake lizikhudzana ndi kuyenda kwa mzimu mu mtima mwa wokhulupilira. “ Tsopano ukumvetsadi

bwino!”

..... “ Pakuti ndingakhale ndiri kwina m’thupi komatu mu mzimu ndiri pamodzi ndi inu, wokondwera pa ku penya makonzedwe anu ndi chilimbiko cha chikhulupiliro chanu cha kwa Khristu.....” (Akolose 2:5).

“ Ambuye ndimadziwa kuti ukufuna ine kupenyenera pa moyo wanga. Tsopano ndidzayamba kulalikira za ichi”

“ Mariko, udaphonya theka lomaliza la chiganizo kawiri. Kukhazikika kumene munthu ayenera kukhala nako ndi kwa chikhulupiliro mwa Khristu ndi zimene Iye ali komanso amachita mkati mwa mtima wa wokhulupilira”

“ Oh! Chabwino”

“ Mariko, chimene ndikufuna kuti iwe uzilalikira ndi zokhala Mkhristu kugonjetsa zonse za chilendo komanso kukhazikitsa ufumu wake mu mitima ya anthu” “ Koma ngati ndilalikira za chikhulupiliro nthawi zonse, mapeto ndikhoza kukhala ngati schuller kapena mmodzi wa aziphunzitsi a chikhulupiliro”

“ Kodi izi zikhoza kukhala zoipa? Kodi sitidagwirizane za kukhala mu zenizeni zimene zili chikhulupiliro, chiyembekezo pamodzi ndi chikondi (1 Akorinto 13:13)?”

“ Inde, ndikukhulupilira tidatero. Ukutanthauza kuti ndiyenera kulalikira zinthu zitatu izi kosalekeza? “ izi zili pa mtima pa ufumu “ Hmmm”

..... Chifukwa chake monga momwe munalandira khristu Yesu Ambuye, muyende mwa iye”

(Akolose 2:6).

“ Mariko, kodi udalandira Yesu Khristu motani? “ Ndidalimbana mu njira yanga kudzera zovuta zambiri za maphunziro komanso zosadzindikirika ndipo kenako ndina.....”

“ Ayi siudatero. Mngelo wa Ambuye adali kunong’oneza mmakutu mwako mau omweo kawirikawiri kufikira udalephera kukana ndipo kenako udagonjera mphamvu yanga...” “Inde, ndikuganiza kuti izo ndi zoona ndithu”

“ ukuona Mariko, udalandira Khristu Yesu Ambuye kupyolera mu chikhulupiliro icho kuyenda mu mtima mwako kukhulupilira kuti ndachita zonse ndipo chomwe udayenera kuchita ndi kukhulupilira chabe ntchito yanga ya chipulumutso. Tsopano ndikufuna kuti ugwiritse ntchito yanga ya chipulumutso. Tsopano ndikufuna kuti ugwiritse ntchito chikhulupiliro chako.

Usayerekeze kuchita izi mwa iwe wekha. Ine ndiri Alefa ndi Omega-Woyamba ndi Omaliza. Pameneukusowa kanthu kena kalikonse – penyerera kwa ine amene ndimakhal mkati mwako komanso ndimapereka chisomo kwa opempha. Usayang’ane ku mphamvu za iwe wekha. Siudapulumsidwe mwa mphamvu zako. Siungazisunge wekha mwa mphamvu zako. Mwa ichi, bwera kwa ine ndipo ndidzakuchilitsa ndi kukukhazikitsa pa phiri lotchedwa PHIRI LA ZIONE.

..... “ Odzika mizu ndi omangirika mwa iye ndi okhazikika m’chikhulupiliro monga mwa phunzitsidwa ndi kuchulukitsa chiyamiko.....” (Akolose 2:7).

Ukuona, Mariko, kukhazikitsidwa ukusowa simu ntchito za thupi zako. Uko kuli mphamvu za kuyenda kwa Mzimu mu chikhulupiliro changa choturuka mu mtimamwako monga mtsinje wa madzi a moyo ndi kusintha mkati mwako. Ichi chimene ukusowa. Bwera, khazikika mu kuyenda kwa mzimu wanga. Bwera mwana wanga”

“Inde Ambuye wanga, ndikubwera kwa inu”

“Mwana wanga chimene uyenera kuchita mu moyo wako ndi kulambira ine kuti ukhale ndi zonse. Ine yense mu zonse, Ndine woyamba ndi womaliza. Ndine moyo wako ndi kupuma kwako. Mwa ichi, machitachita ako ayenera kuphatikizidwa ndi kuyamika mmalo molimbana. Kodi ukutha kuona ichi?”

“Inde, Ambuye wanga”

..... Penyani kuti pasakhale wina wakulanda inu ngati chuma mwa kukonda nzeru kwake ndi chinyengo chopanda pake potsata mwambo wa anthu potsata zoyamba za dziko lapansi osati potsata Khristu pakuti mwa iye chikhulupiliro chidzalo cha uMulungu mthupi ndipo muli odzadzidwa mwa iye, ndiye mutu wa ukuru wonse ndi ulamuliro amenenso munadulidwa mwa iye ndi mdulidwe wosachitika ndi manja, mavulidwe a thupi.....” (Akolose 2:8-12)

Mariko, anthu ambiri adzabwera ndipo adzakulankhula motere, “chita ichi” ndipo “chita icho” “yesera ichi ndipo yesera icho”. Usanyengedwe. Chikhristu chili ine basi. Sichili malamulo. Sichili maphunziro. Chili ine Yesu kukonda iwe, kukonda dziko lonse kupyolera mwa iwe. Ichi ndi chimene chikhristu chili. Ambiri adzayesera kuchiyesera zinthu zambiri. Sichili zinthu zambiri izi. Ndi ine kukonda iwe komanso kukonda iwo. Ichi

ndi chimene chikhristu chili. Usanyengedwe mwana wanga”

“Inde, Ambuye wanga”

“Tsopano kukhuzana ndi mtima wako, pamene ukusowa thandizo, Ine ndili thandizo ngati pali choipa, ndimakhala pomwepo kuthana nacho. Palibe munthu angathe kuchilitsa mtima. Ndi ine amene ndingachite. Ichi ndi chifukwa chake kupindula kwanga mu machilitso kuposa malingaliro a munthu chifukwa palibe munthu angachilitse mtima. Mtima ndi wa Ambuye. Uli wang, atero Ambuye wa makamu”

..... Chifukwa chake munthu asakuweruzeni inu mchakudya kapena chakumwa kapena kunena za tsiku la phwando kapena tsiku lokhala mwezi kapena la sabata ndizo mthunzi wa zirinkudzazo koma thupi ndi la khristu. Munthu aliyense asakunyengeni..... pakuti munafa pamodzi ndi Khristu kusiyana nazo zoyamba za dziko lapansi.....” (Akolose 2:16-23) “Mariko, cholinga chimene ndalemba chenjezo ili ndi choti ndikudzindikira kuti anthu ambiri adzaganiza kuti icho ndi chikhristu akuchita koma ayi. Izo ndi zolenga anthu mmutu mwao. Uko ndi kukopera chikhristu. Kukopera kotere kumakhala ndi malamulo opanda pake monga “usakhudze” “usalawe”. Izi ndi zakunja koma ine ndimakhala mu mtima mwa munthu. Inde, kunja ndi kwambiri koma ine ndi mayang’ana mu mtima. Kulimbana ndi zakunja kwa thupi sikukonza mu mtima. Kuchilitsa mtima, nkofunika. Tsono sitikhazikika pa za kunja. Apa sitikutero kuti kunja sikoyenera. Kunja ndi zotsatira za kukonza mkati mwa mtima.

Mwa ichi iwe ndi Ine tidzipenyenera pa mtima, umo tingathe kuuchilitsira komanso umo ndingamasulire mphamvu yanga kupyolera mu mtima wa munthu chifukwa pochita izi tidzakhoza kuchita zinthu zonse. Taona, ndalankhula. Ndidzachikwanilitsa. Atero Ambuye wa mphamvu yonse.

“Lingalirani za kumwamba osati za pa dziko ayi pakuti munafa ndipo moyo wanu wabisika ndi khristu mwa Mulungu.

Pamene khristu adzaoneka ndiye moyo wathu.....” (Akolose 3:2-4) “Tsopano, Mariko, lingalira za kumwamba – za uzimu zokhazokha. Sitidzapenyenera za dziko lapansi koma za uzimu koma za kukhazikitsa ufumu wanga mwa chikhulupiliro. Ichi ndi chimene tikambilane. Tikambilana za ichi. Izi ndi zimene tizilalikira. Izi ndi zimene tiziphunzitsa. Pochita izi. Tidzachelitsa mtima wa munthu. Pochita izi, tidzachelitsa maufumu a dziko

lapansi. Kodi Sali onse m’manja mwanga? Inde, mwana wanga, kuyambira waung’ono kufikira waukuru, onse ali anga. Mwa ichi tidzawachilitsa chifikwa tidzakhazikitsa maganizo athu pa za uzimu. Mariko, lalikira za Mzimu wanga pamodzi ndi kuphunzitsa. Iyi nfi ntchito yako. Izi ndi zochitikanthawi ya moyo wako wonse. Palibe mpyp kuna mzimu wanga. Bwera ku mzimu wanga, mwana wanga ndipo udzasandulika . Bwera ndipo nditeronso kuti bwera.”

“Pamene ukusanthula pa malamulo mu theka la chiwiri la Akolose, amaoneka osiyana. Sadzakhhalanso malamulo amene umamvera kupyolera mu mphamvu zako. Ayi, tsopano adzakhala malamulo omwe ndizimvera kupyolera mu mphamvu za Mzimu. Tsono malamulo awa ali osungidwa ndi mphamvu ya Mzimu. Iwe uziwatsatira chabe. Ndakupanga iwe kukhala wotero. Palibe wina wofanana ndi iwe. Mwana aliyense mwa ana anga onse wakonzedwa mwapadera ndi dzanja langa. Aliyense wa inu ali wa padera. Aliyense wa inu ali wanga. Pita, mwana wanga mu mtendere” “ Inde, Ambuye wanga”

KUSANTHULANSO FUNDO ZINA ZA PA AROMA 12.

- Phata lemleni la chikhristu ku chipangano chatsopano ndi kukula kwa moyo wa uzimu pamodzi ndi ubale ndi Yesu Khristu.
- Munthu akakhala ndi vumbulutso la phata la chikhristu, buku lonse la chipangano chatsopano limakhala ndi tanthauzo latsopano.
- Malamulo aku chipangano chatsopano amatsatidwa pokhala mu moyo wa zenizeni za Khristu Yesu.
- Ndi Khristu Yesu amene amasunga malamulo awa kupyolera mwa ife. Si ife kusunga malamulo. Sitingathe kuwasunga chifukwa ali a uzimu ndipo ife tiri a mthupi
- Tiyenera kuphunzira kulola Mulungu kulankhula kwa ife pamene tikuwerenga chipangano chatsopano. Tiyenera kupempherera “ mzimu wa vumbulutso” kuti maso amitima yathu awalitsidwe kuti tikathe kumudzindikira iye (Aefeso 1:17-18).
- Lembera fundo zina zomwe zidali zofunikira kwa iwe kuchokera mu chaputala ichi.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBILANA

- Kodi yankho lako ndi lotani kukhudzana ndi chitsanzo cha

kusanthula baibulo?

- Ngati mudaona, tidayamba ndi kulingalira pa phunziro kenako tidadzamabe kufikira ku kulankhulanandi Mulungu- lolembedwa ndi nkozi yemweyi. Kodi uku ndi kumene kuli kusanthula baibulo kuyenera kukhalira (Aefeso 1:17-18)? Kodi ichi mwachita mu kusanthula kwanu baibulo? Bwanji osayamba kuyesa ndime imodzi pansi apa?
- Lingalira mozama ndime zina kuchokera ku chipangano cha tsopano ndi kuona ngati mogwirizana ndi baibulo- choonadi cha nuku ili sizikuoneka za tsopanonso. Yesani Agalatiya 3,4,5, Afeso 1-5, Afilipo 1-4. Yesani njira ya kulingalira yomwe chitsanzo chake chaperekedwa mu chaputala ichi ndipo mukambilane fundo ya pamwambapa. Ona ndi zochitika ziti zili zabwino kwa iwe. Ukhoza kufuna kuonjezera sabata imodzi kapena ziwiri ku kosi iyi pamene membala aliyense wa gulu lako akupita ku nyumba kwake ndi kukusanthula malembo opatulika ali pa mwamba apa. Kenako mugawane zimene Ambuye akuvumbulutsirani.
- Khalani pa gulu lanu ndipo mupeze ndime mu baibulo ndipo musanthule – kumulola Mulungu kulankhula nanu kupyolera mu ndimeyo.
- Mukhoza kusankha ndime iliyonse. Njira yina yabwino ikhoza kukhala yolumikizitsa ophunzira monga adadikira mu chipinda cha pamwamba kudikira tsiku la Pentekosite. Monga gulu kuwerenganso zonse zidachitika pa Machitidwe 1:4-13, 21,2:4) kenako mukhale mozungulira ndipo mugwirane manja ndipo aliyense afotokoze umo akumvera mu mtima mwake. Aliyense akhoza kutero mwa mphindi imodzi kapena ziwiri. Ukhoza kulankhula zimene ukunena kuti Ambuye akulankhula. Kenako nonse mupemphere pamodzi. Osachita mantha ayi.
- Kulemba- “ Ambuye, lankhulani nane chimene kusanthula baibulo koono kuli. Kodi ichi ndi chimene ndakhala ndikuchita? Kodi pali njira zina zimene ukufuna kusanthula pa kusanthula baibulo kuzamitsa chidziwitso? Ngati ndi choncho motani? Zikomo Ambuye pa zimene mukunena” lembera mafunso ali pa mwambapa mu buku lako lapadera ndipo ulebere zonse Ambuye akuyankha. Bwerani mu kalasi ndipo mugawane.

CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHIWIRI.
MAPHUNZIRO A MAU A MULUNGU KAPENA KUKHALA MOYO
WAUZIMU.

Pomaliza tatsiliza chigawo ichi cha mbiri ya moyo wanga. Tadzindikira choonadi chisanu ndi chiwiri:

- | | | |
|------------|----|--|
| Choonadi # | 1- | Mulungu ali yense mu zonse |
| Choonadi # | 2- | Ndine chotengera |
| Choonadi # | 3- | Sindilonso ndi moyo |
| Choonadi # | 4- | Khristu ali moyo wanga |
| Choonadi # | 5- | Ndafa ku chilamulo |
| Choonadi # | 6- | Ndimakhala ndi moyo mwa mzimu. |
| Choonadi # | 7- | Ndimakhala ndi moyo mwa chikhulupiliro |

kuti Mulungu

ali Emmanueli

Mwina mwake tikhazikitse maphunziro atsopano pa choonadi ichi. Maphunziro anga oyamba ndi amene ndingathe kuwatchula kuti “ maphunziro a mphusi” Mukudziwa , ganizo lililonse la munthu lili mphusi. Ndipo ndikhoza kutsimikizira ichi ndi malembo opatulika: “ Iwe uli mphusi, Yakobo” Mwina tikhoza kuwatcha maphunziro atsopano awa kuti “ moyo wolumikizika” kapena kuti “ kukhala moyo wolowa mmalo mwa wina” Kodi iwe ukuganiza bwanji? Kodi ndikufuna kulenga maphunziro atsopano? Mwina mwakw moyo siuli mu maphunziro. Mwina mwakw uli mu mtsinje kuyenda kwa mzimu. Mwina sindikufuna kutanthauzira mwa tchutchuchu za maphunziro awa a mau a Mulungu ndi kukana choonadi cha buku ili. Mwina mwake chimene tiri nacho panopa ndi machitachita atsopano (ozama) mu uzimu.

Ngati ndingasungunule choonadi cha buku ili kukhala maphunziro a mau a Mulungu apa ndili pa ngozi yolankhula motere, “ Tiri olumikizitsidwa kwa Mulungu mwa ichi chili chonse tingalankhule kapena kuchita ndi cha Mulungu, mwa ichi mvetsera uyu ndi Mulunhu kulankhula” Youch! Sizabwino. Izi sizili zimene ndidali nazo mu maganizo anga pamene ndidatsiliza buku ili. Kuyandikira koposa kuli ndi iye amene akhazikitsa chifatso mu moyo wake

chifukwa choti akudzindikira kuti ali fumbi chabe lolumikizitsidwa ku ulemerelo. Iye ali nthawi zonse fumbi. Mulungu nthawi zonse ali ulemerelo. Icho ndi chinthunzi changa pamene ndikukhala pa moyo wanga- kuti ndiri fumbi lolumikizitsidwa ku ulemerelo. Mu njira yotere, nthawi zonse ndimadzindikira amene awiri a ife tiri pamene talumikizitsidwa limodzi (1Akorinto 6:7).

Mwa ichi, mmalo molankhula kuti tiri ndi maphunziro atsopano a mawu a Mulungu, tiyeni tilankhule motere kuti taphunzira kapena kumudzindikira Mulungu mozama komanso kukhala moyo wa Umulungu koposa poyamba. Ndimakonda ichi kwambiri, Kodi iwenso?

Kumaliza buku ili komanso kulankhula mosindika kuti awa Sali maphunziro a mawu a Mulungu atsopano, koma kuti ndi kudzamitsidwa kwa chiyanjano ndi Mulungu, ndidaganiza kugawana nanu zina mwa zolemba zanga kuyambira chaka chatha kapena chinacho. Sikuti ndi za choonadi chisanu ndi chiwiri cha mu buku ili chifukwa pamene Mulungu pamodzi ndi ine takhala pansu ndi kumakambirana, timalankhula zambiri. Moyo sikuti wangokhala mu choonadi chisanu ndi chiwiri ichi. Tsono mupirire nane pamene ndikugawana nanu zinthu za uzimu izi.

10-30-89

Ambuye, kodi mukufuna kulankhula nane chiyani lero lino?

Mariko, ndikufuna kuti udzibwera kwa ine tsiku ndi tsiku nthawi ngati inoyo mu moyo wako. Pali kusintha kwakukuru. Pali zambiri zochitika zimene uyenera kumva kuchokera ku mau ochokera kwa ine tsiku ndi tsiku ngati ukufuna kuti ukhale bwino.

Chabwino, Ambuye, ndidzafunafuna kutero mwa chisomo chanu ku chita zotero. Tsono kukhudzana ndi lero, wamva kale kuchokera kwa ine. Lero ndakupatsa nthawi kuti ukhazikitse ofesi yako ndi kulembanso mabuku ako ndipo uwakonze mwa ukadaulo. Usadandaule. Pamene nthawi yafika kuti uwasindikize, udzakhala, nazo ndalama! Ndidzapereka ndalama izi. Panopa ndi nthawi yoti umalize ntchito ziwiri izi. Uyenera kudzindikira chifuniro cha Mulungu. Zonse zidzakhala mmalo mwake. Ona chipulumutso cha Ambuye.

China nchiyani? Mariko, konda mkazi wako..... Konda mkazi wako

ndi ana ako. Zikoo Ambuye.

11-1-89

Ndidauka kuchokera ku maloto:

Ndidali kuthamanga pa mpikisano ku madera a mapiri. Mphepo idali kuwomba kwambiri pa ine ndipo ndidali kuphepheruka. Kenako mphepo idaleka. Kenako njira idayamba kuchepa ku mapeto. Kenako ndidayamba kukwawa. Mantha adandigwira ndidaima ndipo ndidayamba kupanikizika. Wina adafika kumbuyo kwanga ndikudumpha. Ndimaona kuti akhoza kupweteka kapena kuzipha yekha. Kenako adatero pansi ndipo amandilimbikitsa ine kuchita zomwezo. Ndidali ndi mantha ndipo ndidayamba kukwawa chambuyo kukonzekera kufunafuna njira yina. Mantha adandigwira. Kenakondidatero opanda kena kalikonse kopweteka. Ichi ndidachitadi;

Tanthauzo lake;

Mariko, mantha a kubweretsa kuti tsopano ukathe kuima chiriri chotsa mantha. Ndili pano kukugwira dzanja ndatsogola kukakukonzera njira.

Inde, Ambuye. Kodi pali machitachita ena a padera amene ndiyenera kuchita?

Inde, konda mkazi wako kotheratu pamodzi ndi ana ako. Akusowa maganizo pamodzi ndi mtima wako.

11-25-89

Ambuye, nanga pa za chuma?

Mariko, kodi sindinakusalire nthawi yonse ayi? Kodi sindingathe kupitirira kukusamalira? Nchifukwa chiyani ukudandaula? Ngari ndimadyetsa mbalame za mlengalenga, kodi sindingathe kukusamala iwe?

Ambuye, zonse zimene ndachita ndikuona kuti zili zopanda pake.

Ukuona zoonza mwana wanga chifukwa ukuchita zonse mwa mantha ndi moyerekeza. Kodi siudzindikira kuti njira za munthu zili zosiyana ndi za Mulungu? Usakonze njira yako yako koma udikire pa ine. Usadandaule za mawa popeza za tsiku zikwanilw tsiku lake. Tsiku lililonse lili ndi mavuto ake . Upenyerere pa zosoweka za tsikulo. Upenyerere pa kuitana kwa lero.

Chabwino, Ambuye, kodi kuitana kwa lero kuli kotani?

Kumaliza mabuku ako onse. Kukhala wopindula. Kukhazikitsa bungwe lako

ndi kukonza zonse zofunikira. Iyi ndi ntchito ya lero. Kukonda mkazi wako ndi ana ako osawadzudza. Kodi kudzudza banja lako kwapindula chiyani? Palibe. Ona chipulumutso cha Ambuye. Ndikutero kuti ona chipulumutso cha Ambuye.

12-11-89

Ambuye, sindikudzindikira ndi ntchito zotani zili zofunikira kwa inu lero? Chonde ndiuzeni zimene ndiyenera kuchita. Chabwino, mwana wanga ntchito yofunikira kwambiri ndi ku perekamphatso kwa mkazi wako ya pa Khrstimass. Ichi ndi chofunika kwambiri kwa iwe. Ichi ndi chofunika kuchichita pa banja lako. Inde, Ambuye.

12-12-89

Ambuye, chonde uzirani moyo watsopano pa pattti ndi ine. Tikusowa mphamvu yanu ya machilitso lero lino.

Inde, Mariko, ndikudziwa. Tsopano popeza wafunsa, ndipereka. Ambuye, perekani mu miyoyo yathu anthu pamodzi ndi zosoweka zomwe mwa tikonzera. Ndidzatero, mwana wanga. Ona chipulumutso cha Ambuye. Ambuye, Kodi sikuli mu nthawi yake kuyamba kulemba mu pepala ya padera za mitundu ya mabuku?

Ayi, mwana wanga, ukhoza kuyamba panopa.

12-7-89

Mariko, nchifukwa chiyani ukuchita changu kuchita zinthu osayamba kaye wandifunsa ine? Kodi siukuona kuti ichi ndi chinthu choyambirira chimene chiyenera kumachitika? Kodi siukuona kufunikira kuti nkoyenera kuti uyambe kaye wamva kwa ine usadapereke zonse kwa okutsogolera ako? Inde, Ambuye, ndikuona kuti mukulankhula zoona. Nanga mukufuna kulankhulanso chiyani kwa ine?

Chabwino, poyambirira, awa sadali maganizo anga. Adachokera kwa iwe osati kwa ine. Mwa ichi sizingathe kupindula kwenikweni. Usaike ndalama mu ichi chifukwa sizipindula kanthu. Ine ndidzakhala mthandizi wako. Ndidzakupatsa zosowa zako. Usakhulupilire mkono wa nyama kukuthandiza pa zinthu za uzimu. Ndi Mulungu mwini amene angapereke zosowa zako.

Ndi Mulungu mwini amene adzalemekezede. Kodi siukudzindikira kuti tikukhazikitsa mbiri iwe ndi Ine? Tikugwira ntchito limodzi za ulendo wa mbiri pamodzi ndi chikhulupiliro. Iyi ndi mbiri yofunikira imene tikukhazikitsa. Ichi ndi chifukwa chake ndikupenyera mwa tcheru. Sindikufuna kuti zisemphane. Ukhoza kupeza ngongole ya ichi lero lino-koma sindikufuna kutero. Ndipereke zonse ndi ine. Dikira ndipo uona chipulumutso cha Ambuye. Sikoyenera kuti isokoneze moyo mu banja lako chifukwa cha zimene ndakuuza kuti uchite. Ndidzapereka mu njira yodabwitsa. Sibwino kuti utenge ngongole.

Chabwino, Ambuye. Ungopereka ku banki zoyenera kutero ndipo uzichita zimene ndakuuza. Inde, Ambuye.

2-20-90

Mariko, lero pali zinthu zambiri zomwe zikuchitika zimene zidzakhudza tsogolo lako mu njira zazikuru zodabwitsa. Lero ndi tsiku la mapemphero pamodzi ndi kukambila ine. Lero udzipereke kotheratu kwa ine monga nsembe ya milomo yako. Lero si tsiku lolemba kapena lowerenga koma lopemphera kuti ndikasunthe mapiri mu mitima ya anthu ndikachite zinthu zodabwitsa. Lero ndi tsiku lopemphera – pamodzi ndi kusala chakudya pamaso panga. Funafuna nkhope yanga mu njira ya mphamvu lelo lino ndipo mwana wanga ona zodabwitsa zimene ndichite mmalo mwa iwe.

Ungochita zokhazo zimene zili zoyenera. Zina zonse zidikire tsiku lina-Mwana wanga. Ona chipulumutso cha Ambuye.

Inde, Ambuye, ndilimbikitseni pamodzi ndi kunditsogolera lero lino. Ili ndi pemphero langa.

Ndidzatero, mwana wanga, koma ungobwera kwa ine. Ndidzachita.

2-23-90

Mariko, uyenera kumvetsa bwino kuti satana akukuukira iwe. Umukanize iye ndipo adzakuthawa. Ima chilili mwa ine ndipo ndidzakuthandiza.

Ndilimbikitseni, Ambuye wanga.. Mariko, ndidzakuthandiza lero lino.

Lidzakhala tsiku lodzodzedwa lolemba pamodzi ndi zochitika zambiri. Khala wokondwa ndi ine. Pita kukagwira ntchitoyo. Pali zinthu zambiri zimene tichite lero.

Moyo ukupitilirabe. Tsiku lililonse pamakhala zochitika ndi Ambuye. Tsiku lililonse lili sitepe ya chikhulupiliro- pokhulupirira kuyenda kwa mzimu kuchokera mu mtima mwanga. Inde, ndi moyo wodzipereka. Inde, nthawi zina ndimalakwitsa. Komabe ndi njira yabwino yokhalira yomwe ndaipeza pa moyo wanga. Kuchokera pa zimene ndingalankhule, iyi ndi njira aneneri mu baibulo amakhala kuchokera pa zimene ndazona, iyi ndi njira yomasulira mphamvu ya Mulungu wamphamvu yonse kupyolera mu mitima yathu. Ndikuona kuti ichi ndi choyenera kwa inu. Ngati ungagwe, ndikukulimbikitsa kuchita zomweao. Imilira ndi kulankhula motere, “ Mulungu, kodi tikhoza kuyeseranso kawiri?” Ndili ndi chikhulupiliro kuti titatha kuyenda mu ichi pa m’bado umodzi kapena iwiri, tidzakhala anthu ozama ndi luntha mu kuyenda ndi Mulungu. Pa nthawi ino, tiyenera kuyamba pamene tiri ndi kuchokera pamenepo. Sindikudziwa njira yina iliyonse.

Ndi pempho langa kuti madalitso a Mulungu akhale pa moyo wako pamene ukuyenda ulendo wa njira ya moyo yokhala modabwitsa koma mwa chilengedwe!

KUSANTHULANSO FUNDO ZINA ZAPAAROMA 13

- Cholinga cha bukuli sikukhazikitsa maphunziro atsopano a za mau a Mulungu.
- Moyo sikuti uli maphunziro mau a Mulungu koma uli padera.
- Cholinga cha bukuli ndi choti tikhale ndi kuzama kwa padera ndi Mulungu osati maphunziro atsopano a mau a Mulungu.
- Tizingolola moyo kuti uzingokulirabe mwa mphamvu mu chiyanjano ndi Mulungu osati maphunziro chabe
- Kwa ine, zonse zimene ndalankhula zili mu mabuku a zolemba zanga zomwe ndimalemba tsiku ndi tsiku. Uwo ndi moyo kwa ine. Umo ndimo ndimakhalira. Umo ndimo ndikupempha kuti usatire choonadi cha buku ili.

KUGANIZIRA PAMODZI NDI KUKAMBIRANA

- Nchifukwa chiyani tikuyetsetsa kuzama mu zatsopano za

maphunziro a mau atsopano a za Mulungu? Kodi izi ndi za mnzeru? Kodi izi ndi zoyenera? Kodi izi ndi zofunika? Kodi nkoyenera kusintha machitachita atsopano ndi Mulungu pa moyo wako ndi maphunziro atsopano a mau a Mulungu? Ngati ndi chomwecho, nchifukwa chiyani?

- Kodi maphunziro a mau a Mulungu amakhala a mmutu kapena mu mtima? Kodi maphunziro a mau a Mulungu ali moyo kapena ayi? Kodi akhristu azipenyera pa zochitika pa moyo wao ndi Mulungu kapena pa maphunziro chabe? Kodi mphamvu zako zambiri monga khristu umatayira kuti?
- Kodi maphunziro a mau a Mulungu amalumikizansitsa kapena kugawa mpingo? Kodi tikhoza kuyesa chinthu ndi chipatso chake? Ngati maphunziro a mau a Mulungu amagawa mpingo? Kodi tikhoza kuterokuti chipatso chosindikira ichi ndi choipa? Kapena kodi kukhoza kukhala bwino kulankhula motere “ndiri” ndi maphunziro a mau a Mulungu ndipo ena onse zipembedzo zokwanira 2300 zili zolakwa? Kodi ukuganiza bwanji apa?
- Kodi Yesu adasindikira za maphunziro a Mulungu kapena kodi amangoonetsera mphamvu ya Mulungu mu moyo wake? Kodi iye amapasula maphunziro a mau a Mulungu polankhula iye nthawi zambiri motere, “koma ndinena kwa inu?” Kodi chidakokera anthu kwa Yesu chidali chiyani?
- KULEMBERA- Lembera mafunso otsatirawa pa mwamba pa tsamba lako pa zolemba zako motere, “Ambuye, mungandilankhuleko chonde kukhudzana ndi choonadi ccha mu buku ili ndi umo zikugwirizana ndimaphunziro a mau a Mulungu? Kodi muli phindu ili lonse mu maphunziro a mau a Mulungu? Ngati ndi chomwecho, phindu lake ndi liti? Kodi pali ngozi iliyonse mu maphunziro a mau a Mulungu? Ngati ndi chomwecho, kodi ngozi yake ndi iti?” Lembera yankho lako limene Ambuye akupatse. Gawana ndi anthu pa gulu lako.

UMOYO WACHILENGEDWE

DONGOSOLO LA UMOYO WAKU EDENI

(Khalani moyo wautali kukwanilitsa cholinga chanu) Lolembedwa ndi Mariko pamodzi ndi Patti Virkler

Phunzirani umo;

- Mungakhalire moyo wa nthawi yaitali komanso wa thanzi
- Mungakhale a phindu
- Kuchotsa matenda a khansa kupyolera mu chakudya
- Kuchepetsa matenda a shuga
- Kuchotsa kunenepa kosayenera
- Kuchotsa matenda a mtima
- Kuchotsa matenda a

Buku ili lili lofunikira kwa iwe ngati:

- Ukudwala ndipo watopa ndi kudwaladwala.
- Ukufuna kulemekeza Mulungu mu thupi lako
- Ukufuna kukhala moyo wautali ndi wamphamvu

Buku ili lili lofunikira kupulumutsa moyo wako!

- Kupeza zodabwitsa za mu baibulo kukhuzana ndi zakudya komanso za moyo wa thanzi komanso zimene a kafukufuku apeza posachedwapa
- Kutenga ulamuliro wa thupi lako ndi umo ungalisungire kuti likhalebe ngati la mwana osati la matenda.

Phunzira umo ungonjetsere matenda pochita izi;

- Pophwesa mphamvu ya mankhwala mu thupi lako
- Kumanganso mphamvu za chitetezo ku matenda zokhala mwa iwe
- Kudyetsa ma selozi a mu thupi lako.

“Ndichititsa mboni lero kumwamba ndi dziko lapansi zitsutse inu, ndakaika pa maso panu moyo ndi imfa, mdalitso ndi temberero potero sankhani moyo kuti mukhale ndi moyo inu ndi mbeu zanu.....”

(Deteronomo 30:19) Dotolo wa mtsogolo sangapereke mankhwala koma adzasangalatsa odwala ake powapatsa malangizo a umo angasamalire thupi lawo mu chakudya, koma ku chitetezo cha matenda” atero Thomas Edison.

KULANGIZIDWA NDI MULUNGU

Buku lokuonetsa umo ungachilitsidwire ku zowawa za mtima kupyinjika, mantha.

Buku la manja la masamba 100	=	9.95 USD
Buku la ophunzira la masamba 80	=	10.95 USD
Makaseti a maphunziro pa maora awiri	=	10.95 USD
Mavidiyo a maphunziro a maora11	=	199.95 USD

